

Kuyang'anira

Mwa

Zolinga

HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a Harvest International Institute ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinathandizira anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

@Harvestime International Institute

ZAMKATI MWA BUKULI

Kagwiritsidwe Nthcito Ka Bukuli.....	3
Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira Limodzi Pagulu.....	4
Mau Otsogolera.....	5
Zolinga Za Maphunzirowa.....	6
1. Mau Otsogolera ku Kuyang'anira mwa Zolinga.....	7
2. Mulungu wa Cholinga.....	17
3. Cholinga	27
4. Kukonza Dongosolo	39
5. Anthu ndi Ndondomeko: Kukwaniritsa Dongosolo	51
6. Kumalizitsa: Kuunikira Dongosolo	64
Zoonjezera 1: Mau a Chikhulupiro cha Mpingo.....	74
Zoonjezera 2: Mau a Cholinga.....	77
Zoonjezera 3: Maikidwe a Zinthu M'chimake.....	79
Zoonjezera 4: Kulongosola Anthu mu Utumiki.....	84
Zoonjezera 5: Kukonza Dongosolo.....	93
Mayankho a Mafunso.....	97

KAGWIRITSIDWE NTCHITO KA BUKULI

KAKONZEDWE KA BUKULI

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

Zolinga: Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Werengani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

Vesi Yotsogolera: Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

Zopezeka mu Magawo: Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

Mayeso Odziyesa Nokha: Osathamangira kulemamba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

Zophunzira Zowonjezera: Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mawu Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

Mayeso Omaliza: ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

ZOWERENGA ZINA ZOFUNIKA POPHUNZIRA PHUNZIROLI

Mudzafunikira Buku Lopatulika

NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU

MKUMANO WOYAMBA

Kutsekulira: Yambani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

Khazikitsani Ndongomeko Zapagulu: Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene muzikumana.

Mayamiko ndi Matamando: Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

Gawani Mabuku Kwa Ophunzira: Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

Perekani Ntchito Yoyamba. Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene aziphunzitsidwa pa mkumano uli wonse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO

Kutsekulira: Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina a ophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a ophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

Kukumbutsira: Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

Phunziro: Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphunzira komanso m'mene angagwiritsire ntchito zimene aphunzira pamoyo wawo ndi utumiki.

Mayeso Odziyesa Nokha: Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankho kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adzipezere okha mayankho.

Mayeso omaliza: Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphunzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina aliyense ali ndi buku laphunziroli.

MAU OTSOGOLERA

“Kuyang’anira mwa Zolinga” ndi njira yoyendetsa utumiki wa Chikhristu moyenera komanso mwakuchita bwino. Kudziwa chifuniro cha Mulungu kokha sikokwanira m’moyo ndi utumiki wanu. Mukuyenera kupanga dongosolo la kukwaniritsira maitanidwe anu auzimu. Mukuyenera kuphunzira kugwira ntchito ndi Mulungu kuti mukwaniritse zolinga ndi dongosolo lake pa moyo wanu.

Bvuto lalikuru pakati pa atsogoleri a Chikhristu ambiri ndi kulephera kuika zinthu m’malo ndi kuyang’anira chuma chauzimu chomwe Mulungu wawapatsa. Ngati ogwira ntchito ya kholola lauzimu ndi ochepa, monga Baibulo linenera, ndiye kuti ochepawo akuyenera kugwiritsidwa bwino ntchito.

Kuika zinthu m’malo ndi kukonza dongosolo la utumiki sikuti kumasokoneza kachitidwe ka Mzimu Woyera ayi. M’malo mwake kumakuthandizani kuti mupange ziganizo zoyenera mogwirizana ndi chitsogozo chake pokwaniritsa zolinga ndi madongosolo ake. Chikhulupiriro chanu chimathandiza kukwaniritsa dongosolo la Mulungu, pakuti Iye amalowerera pamene inu mwayambapo.

Phunziro iri likuthandizani kuti mukakwaniritse utumiki umene Mulungu wakuitanirani. Mukonza cholinga cha utumiki molingana ndi chifuniro komanso zolinga zake. Muphunzira za kukonza zokhumba, kukwaniritsa dongosolo, komanso kuunikira zotsatira za ntchito ya utumiki wanu.

Gawo la zoonjezera m’phunziro lino liri ndi zitsanzo zoti zikuthandizeni kuona momwe kuika zinthu m’malo mu utumiki kumakhalira pa mpingo panu.

ZOLINGA ZA PHUNZIRO

Mukamaliza phunziro lino mutha kukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kumasulira mau oti, “Kuyang’anira mwa Zolinga.”
- Kulemba mwachidule maziko a kukonza dongosolo mwa Mau a Mulungu.
- Kudziwa cholinga cha Mulungu.
- Kukonza Mau a Cholinga a utumiki wanu.
- Kukonza zokhumba
- Kuika zinthu m’ malo kuti mukakwaniritse zokhumba.
- Kuunikira ntchito yanu kuti mukonze utumiki wanu.
- Kugwiritsa ntchito luso la phunziro lino mu mpingo wanu.
- Kugwiritsa ntchito luso la phunziro lino m’ moyo wanu.

CHAPUTALA 1

MAU OTSOGOLERA KU KUYANG'ANIRA MWA ZOLINGA

Zolinga:

Mukamaliza chaputalachi muzikwanitsa kuchita izi;

- Kufotokoza tanthauzo la Kuyang'anira mwa Zolinga
- Kufotokoza ubwino wakusamalalira potsatira zolinga
- Kuthana ndi okana Kusamalira potsatira zolinga

Vesi Lotsogolera

Koma zonse zichitike koyenera ndi kolongosoka (1 Akolinto 14:40)

MAU OYAMBA

“Kuyang'anira” ndi ndondomeko yomalizitsira dongosolo kudzera mwa anthu, zipangizo ndi chuma cha uzimu.

“Kuyang'anira potsatira zolinga” ndi ndondomeko yopangira dongosolo ndi kuyigwiritsa ntchito muwutumiki moyenera komanso mothandiza. Baibulo limati:

Koma zonse zichitike koyenera ndi kolongosoka (1 Akolinto 14:40)

Kuchokera koyambirira kwa Baibulo Mulungu anapanga dongosolo limene anawadziwitsa amayi komanso abambo amene analemba ndi kutsatira mosamala.

Mulungu anamuwuzira Mose kuti alembe ndondomeko yomagira Likasa. Anampatsa Davide ndondomeko yakamangidwe ka Kachisi. Anamlebetsa Hezekiya masophenya ake momveka bwino komanso mwadongosolo.

Phunziro iri ndi chiyambi cha “Kuyang'anira Potsatira Zolinga”. Muphuzira kuti zimakhudzana ndi chani, ubwino wake, ndikuti mungachite bwanji mukakumana ndi otsutsa.

KUSAMALIRA POTSATIRA ZOLINGA

“Kusamalira potsatira zolinga” ndiko kuyang'anira utumiki potsatira zolinga. “Kuyang'anira” ndi mawu ena a “udindo.” Adindo kapena oyang'anira amakhala ndi ulamulilo pa zinthu chifukwa chakuti wina anawadalira nazo. Ngati okhulupirira muli ndi udindo pa zinthu za uzimu zimene Mulungu anakupatsani monga:

Uthenga Wabwino; Okhulupirira aliyese ndi mdindo wa Uthenga Wabwino. Tikuyenera kugawana uthenga wake ndi anthu ena.

Chuma: Okhulupirira aliyese ndi mdindo pa chuma chimene Mulungu anamupatsa. Amene amagwira chuma cha utumiki mu tchalitchi kapena bungwe ndi adindo pa chuma chimenechi.

Katundu wa Utumiki: Monga Manyumba a mpingo, Katundu, ndi zipangizo.

Mphatso za Uzimu: Okhulupirira aliyese ali ndi phatso zosachepera imodzi za uzimu. Ndinu mdindo wa mphatso yanu ya uzimu ndi malo anu a utumiki mu Mpingo wa Ambuye.

Okhulupirira ena: Mulungu amagwiritsa ntchito anthu osati zochitika kuti amange ufumu wake. Kuyang'anira ndi udindo zimakhudza anthu. Ngati muli mtsogoleri muli ndi udindo pa anthu amene mukuwayang'anira ndikugwira nawo ntchito mu utumiki wanu. Mukuyenera kuwathandiza kuti moyo ndi mphatso zawo za Uzimu zikule kupititsa patsogolo utumiki wa Mulungu.

Mukuyenera kukhala mdindo wabwino wa zinthu zimenezi. Kukhulupirika ndi choyenereza chenicheni cha mdindo:

Komatu pano pafunika za adindo, kuti munthu akhale wokhulupirika (1 Akolinto 4:2)

Kuti mukhale oyang'anira wabwino mukuyenera kupanga madongosolo. Mau akuti "zolinga" ndi mawu ena a madongosolo kapena masophenya. Kuyang'anira potsatira zolinga ndi kupanga madongosolo pokhala oyang'anira wabwino wa zinthu zimene Mulungu wazipereka.

Yesu ananena fanizo pa Mateyu 25:14-30 la akapolo amene mbuye wao anawapatsa matalente.

Anawuzidwa kuti akhale adindo abwino pogwiritsa ntchito chumacho mwanzeru. Kupatula m'modzi, aliyese anali ndi dongosolo limene analitsatira bwino. Amene sanapange dongosolo pa zinthu zimene anapatsidwa sanazigwiritse ntchito ndipo anaweruzidwa wantchito wosakhulupirika.

Yesu amalimbikitsa kupanga dongosolo:

Pakuti ndani wainu amene akafuna kumanga nsanja yaitali, sathamnga wakhala pansinawergera mtengo wache, aone ngati ali nazo zakuimariza? (Luka 14:28)

Tikalankhula za kulemba dongosolo komaso kuyang'anira mphuziloli, sitikunena za m'mene amachitira amalonda. Tikunena za kupanga dongosolo motsogozedwa ndi mzimu woyera kuti utsogoleri uyende bwino. Popeza Yesu amadziwa zakutsogolo iyeyo akhoza kupereka zeru mukamapanga ndogoso lanu.

Kuyang'anira potsatira zolinga kumathandiza kuti mukhale adindo abwino pa utumiki umene Mulungu anakupatsani. Zimakuthanidzani kugwira ntchito ndi Mulungu pokwaniritsa cholinga chake. Baibulo limatsimikiza kuti anthu akayamba kupanga zinthu monga mwa dongosolo lake koma mwachikhulupiriro Mulungu amachita nawo.

Kuyang'anira monga mwa zolinga kumakhudzana ndi:

-Kupeza cholinga cha utumiki mogwirizana ndi cholinga cha Mulungu.

-Kupanga dongosolo lokwaniritsira zolinga.

-Kutsogolera anthu komanso ndondomeko pochita monga mwa dongosolo

Kukozanso ndongosolo mwa kusanthula.

Kukhala mdindo wabwino ndi kupanga dongosolo ndi ntchito yaikulu. Zimafunika kukhala ndi nthawi komanso khama. Ntchito zauzimu za mtengo, udzu ndi ziputu ndizosavuta kupanga koma sizimachedwa kuonongeka. Koma khama limafunika pa siliva ndi golide chifukwa ndi zokhalitsa.

Koma ngati wina amanga pa mazikkowo, golidi, siliva, miyala, ya mtengo wace, mtengo,, maudzu, dziputu, ntchito ya yense idzaonetsedwa; pakuti tsikulo lidzaisonyeza, chifukwa kuti yavumbuluka m'moto; ndipo moto wokha udzayersera ntchito ya yense ikhala yotani (1 Akolinto 3:12-13).

CHITSANZO CHA M'BAIBULO

Utumiki wa Yesu Khristu ndi umodzi mwa mautumiki amene anayang'aniridwa potsatira zolinga:

CHOLINGA:

Yesu amadziwa cholinga chake m'dondosolo la Mulungu. Iye amalakhula ziganizo zambiri za cholinga cha utumiki wake kumayambiriro kwa utumiki wake. Mwachitsanzo, onani Luka 4:18-19.

DONGOSOLO:

Yesu anali ndi dongosolo la utumiki wake. Anakozeratu kulalikira ndi kuphuzitsa Uthenga Wabwino, kuchiritsa odwala, kuturutsa ziwanda ndi kupanga zodabwitsa kutsimikiza mau a Mulungu. Anakwaniritsa cholinga cha Mulungu pofera machimo athu onse, kuononga ntchito ya woipa, ndi kuuka kwa akufa mwa mphamvu komanso ulemelero.

ANTHU:

Yesu anagwiritsa ntchito anthu muutumiki wake. Anaitana akuphuzira asanu and awiri kuti atumikire nawo pamodzi. Kenako anatomiza anthu makumi asanu andi awiri kukatumikira Uthenga Wabwino. Anatomanso akuphunzira onse kukalalikira Uthenga Wabwino ku maiko onse.

MAWONEDWE AZINTHU:

Yesu anasanthula utumiki wa ophuzira ake kuti akonzenso ndondomeko zawo (Luka 10:17-24). Atatha kukoza onse ndondomeko anawatuma ophunzira onse kuti achitepo kanthu (Mateyu 28:19-20 ndi Machitidwe 1:8).

UBWINO WAKUYANG'ANIRA BWINO

Kuyang'anira bwino utumiki umene Yesu anakupatsani ndikwabwino kwambiri chifukwa:

KUMAPEREKA CHOLINGA NDI CHITSOGOZO:

Ngati mukufuna kupambana mu utumiki wanu, cholinga chanu ndi ndondomeko zanu zikuyenera kukhala zofanana ndi za Mulungu.

Mukakhala kuti mukudziwa cholinga cha utumiki ndikupanga dongosolo kuti mukwaniritse cholingacho, mutha kutsogolera anthu ena. Atsogoleri abwino ayenera kudziwa komwe akupita kuti athe kutsogolera anthu amene akuwatsatira. Mu utumiki, chitsogozo ndi umodzi zimakhudzana ndi kukhala ndi cholinga chimodzi komanso kopita kumodzi.

Zisokonezo zimachepetsedwa ngati chitsogozo chiri chodziwika:

Pakuti Mulungu sali Mulungu wa chisokonezo koma wa mtendere; monga mwa Mipingo yonse ya oyera mtima. (1 Akolinto 14:33)

Chifukwa chake khalani akutsanza a Mulungu, monga ana okonedwa; (Aefeso 5:1)

M'phunziroli, muphuzira kuti Mulungu anali ndi cholinga komanso dongosolo kuyambira pachiyambi. Ngati zochitika za Mulungu sizikukhudzana ndi chisokonezo, utumiki wa akapolo ake sukuyenera kukhudzananso ndi chisokonezo.

KULOLEZA KUPANGA ZISANKHO ZOYENERA:

Zisankho zimasonyeza tsogolo. Izi ndi zoona ngakhale ndi pankhani ya chipulumutso. Mukuyenera kupanga chisankho chakuvomera kapena kukana Uhenga Wabwino. Tsogolo lanu limakhudzidwa ndi zisankho zanu. Moyo wanu ndi utumiki wanu unakhudzidwa ndi zisankho zimene munapanga. Mumapanga zisankho popanga dongosolo moganiza bwino kapena mongopanga chabe. Dogosolo ndi kuyang'anira motsogozowedwa ndi Ambuye zimakuthandizani kupanga zisankho.

KHAZIKITSA ZINTHU ZOYAMBIRIRA MUUTUMIKI:

Kudziwa cholinga ndi dongosolo la Mulungu kumapangitsa kuti mukhazikitse zinthu zoyambirira m'moyo komanso muutumiki. Izi ndi zinthu zofunika kwambiri zimene mungafune kuti zichitike moyambirira.

M'moyo wanu muli ndi zinthu zimene mungafune kuti zichitike moyambirira. Izi mumapanga mukudziwa kapena musakudziwa. Mumakhazikitsa zinthu zoyambirira chifukwa cha zizolowezi zimene zakhazikika m'moyo wanu, pogonjera ku zinthu zochitika kapena anthu okuzungulirani, kapena popanga zisankho mokhudzana ndi cholinga cha Mulungu.

Luka 12:16-20 akunena za munthu amene anasokoneza zinthu. Muphuzira za fanizoli mwatsatanetsatane pamapeto pa maphuzirowa. Nkhani imeneyi ikusonyeza kuti kusokoneza machitidwe azinthu kumabwera ndi chilango.

KUKULOLEZANI KUCHITAPO KANTHU ZINTHU ZISANACHITIKE:

M'malo mopangiratu dongosolo, anthu ambiri amatanganidwa ndi kuchitapo kanthu zinthu zitachitika kale. Izi zimapangitsa anthu kuti asachite zinthu mwanzeru komanso kutsatira zolinga.

Opanda kupanga dongosolo, sumadziwa kuti ukuchita chani, ukuchita chifukwa chani, nanga kuti ungachite bwanji. Chifukwa chakuti mulibe cholinga ndi ndongosolo, mulibe choti mukhoza kudziperekeru, simungasanthuleso machitidwe anu, ntchito ya Mulungu, ndipo mukhoza kukopeka ndi kusiya mthawi ya mavuto. Kupanga dongosolo kumasintha zilakolako zanu kuonetsa masomphenya, ndi zinthu zenizeni. Zimakuthandizani kudziwa zinthu zimene zikuyenera kuchitika komanso m'mene zikuyenekera kuchitikira kuti mukwaniritse cholinga cha Mulungu.

ZIMATHANDIZIRA KUTI ANTHU AZIDZIWA ZOMWE MUKUCHITA

Pokhala ndi dongosolo, anthu amadziwa udindo wawo. Amakhala okonzeka kufotokoza m'mene zikuyendera kwa Mulungu, anthu ena, komanso eni okha. Izi zitanthauza kuti kukhala okonzeka kupereka mayankha pa zinthu zimene iwo anapereka kuti zichitike.

Fanizo la matalente pa Mateyu 25:14:30 kapolo amayenera kuthokoza pa matalente amene mbuye wake anampatsa. Mbuye wawo anali ndi dongosolo, anafotokozerera akapolo ake, ndipo amayenera kukwaniritsa pogwiritsa ntchito chuma monga m'mene anawuzidwira.

Mulungu adzakuwerengerani mulandu osati pakungodziwa chabe chifuniro chake komanso pakuchichita:

Ndipo kapolo uyo akanena muntima mwake, Mbuye wanga azengereza kudza; ndimo akayamba kupanda anyamata ndi adzakazi ndi kudya ndi kumwa, ndi kuledzera (Luka 12:47)

KUOLEZA MASANTHULIDWE:

Kusanthula kumakhala kotheka chifukwa cha dongosolo kuti ziwoneke ngati mukukwaniritsa cholinga ndi dongosolo la Mulungu. Mumadziwa bwanji ngati mukupambana kapena kulephera? Ngati mulibe cholinga, kodi mungadziwe bwanji ngati munakwaniritsa?

KUPEREKA MWAYI OGWIRITSA NTCHITO ZINTHU ZA UZIMU

Dongosolo limathandiza kugwiritsa ntchito zinthu za uzimu moyenera. Kugwiritsa ntchito moyenera ndalama, katundu, anthu, mpatso za uzimu ndi maitanidwe antchito mu Ufumu wa Mulungu.

KUKUKOZEKERETSANI KULOWA MAKOMO OTSEGUKA

Mulungu amatsekula makomo kwa anthu ake:

Ndidziwa ntchito zako (taona, ndapatsa pamaso pako khomo lotseguka limene munthu sakhoza kutsekapo). Kuti uli nayo mphamvu pang'ono, ndipo unasunga mau anga, osakana dzina langa.

(Chivumbulutso 3:8)

Mulungu akatsekula makomo, mukuyenera kukhala okozeka kuyendamo. Izi sizotheka opanda kukozequera koyambirira. Werengani fanizo la anamwali opusa komanso ochenjera pa Mateyu 25:1-13). Mulungu amatsekula makomo, koma samakhala otsekuka mpaka kalekale. Amatsekulidwa ndikudikira malowedwe anu. Ndipo nthawi ina amatsekedwa ndipo nthawi zina satsekulidwanso.

ZIMAFANANITSA CHOLINGA CHANU KUFANANA NDI CHOLINGA CHA MULUNGU:

Atapulumsidwa Mtumwi Paulo, choyambirira anafunsa kuti “Mukufuna kuti ndichite chiyani?”

Amamufunsa Mulungu. “Dongosolo lanu pa moyo wanga ndi utumiki wanu ndi chani?” Cholinga chanu chikafanana ndi cholinga cha Mulungu, ndinu opambana. (Onani Marko 14:36:36 ndi Luka 5:11).

ZOTCHINGA PAKUKOZEKERA

Mukamagwiritsa ntchito mfundo za kuyang'anira potsatira zolinga, zimene muphunzire mudzakumana ndi zotchinga kuchokera kwa ena. Ichi ndi chifukwa chake ena samapangira dogosolo ndi kuyang'anira mautumiki awo:

KUSOWEKA CHOLINGA:

Zimakhala zovuta kuti anthu apange dongosolo ngati sanamvetsetsa kumvetsetsa cholinga chenicheni mu dongosolo la Mulungu. Mukuyenera kudziwa cholinga chanu ngati mungapange dongosolo kuti mulikwaniritse. Mphunziroli, muphunzira za cholinga chachikulu cha Mulungu ndi cholinga chanu mudongosolo la Mulungu. Mukamvetsetsa izi, mudzakwanitsa kuwawuzako ena ndikuwanthandiza kuzindikira mbali yawo mufumu wa Mulungu.

CHIKHULUPIRIRO CHAKUTI SI MALEMBA

Ngakhale ena amakhulupirira kupanga dongosolo si Malemba, Baibulo linadzala ndi amuna komanso akazi amene anapanga dongosolo motsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Mutha kuphunzira zochulukira zokhudzana ndi izi m'chigawo cha "Kudziwa Zambiri" mphunziroli.

Mudzaphuziranso m'chaputala cha chiwiri kuti Mulungu ndi Mulungu wa cholinga ndi dongosolo. Anagwiritsa ntchito anthu, mitundu ya anthu, Israeli, Mzimu Woyera ndi tchalitchi ndongosolo lake. Dongosolo lake linakhazikitsidwa kumayambiriro a nthawi, ndipo mpaka lero akugwirabe ntchito monga mwadongosolo lake.

CHIKHULUPIRIRO CHAKUTI ZIMATCHINGA MZIMU WOYERA:

Anthu ena amaganiza kuti dongosolo komanso kuika zinthu m'chimake zimatchinga ufulu wa

Mzimu woyera. Izi sizowona. Chitachitika chidzalo chamzimu woyera monga zinalembedwa pa Machitidwe 2, pambuyo pake dongosolo ndi kuika zinthu m'malo zinayambika (Machitidwe 6).

Mzimu Woyera sumatchingika ndi mwambo wa kuika zinthu mchimake popanga dongosolo mutumiki. Zimakupangani kuti mukhale atcheru potsogozedwa ndi Ambuye chifukwa mumapanga zisankho pofuna kudziwa cholinga ndi dongosolo lake.

Dongosolo litha kukhala mbali imodzi ya kupemphedwa, nthawi imene mukukumbukira pa zolinga ndi ndondomeko za Mulungu ndi kutsegula mzimu wanu ku chitsogozo cha Mzimu Woyera. Amasanthula mtima wanu ndi Mzimu, ndipo chifukwa ali ndi mtima wa Mulungu, amawulula dongosolo ndi zolinga za Mulungu. Mukamapemphera, werengani mawu, ndipo pangani dongosolo motsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Kupanga dongosolo ndi chochitika cha uzimu ndipo ntchito za mzimu sizimatchingika.

Chitsazo chimodzi chabwino ndi cha Yoswa ku mzinda wa Ayi pa Yoswa 8. Yoswa anali ndi dongosolo (ndime 4) koma sinatchinge chodabwitsa cha Mulungu (ndime 18). Dogosolo ndi zochitika muzimu zinachitika mogwirizana.

CHIKHALIDWE:

Mukafuna kuchita chinthu chirichonse chosiyana, mumatsutsidwa ndi onse amene anazolowera machitidwe ena a zinthu chifukwa samafuna kusintha. Amakhala kuti amachita zinthu zomwezo kwa zaka zambiri ndipo chinasantuka chikhalidwe. Yesu anali ndi vuto limeneli ndi Afalisi komanso Aphumzitsi.

Sizitanthauza kuti anthu amene amakonda chikhalidwe siwopulumutsidwa kapena kuti sali mbali imodzi ya Thupi la Khristu. Ndi abale komanso alongo ndithu ndipo tiyenera kuwakonda ndikuwathandiza m'mene tingathere. Koma anasankha kukakamira zikhalidwe za anthu osati kupita patsogolo kuti akwaniritse zinthu za tsopano motsogozedwa ndi Mzimu Woyera.

Yesu ndi Paulo onse anatumikira m'makachisi ndi m'masunagoge monga m'mene analolezedwera. Awa ndi manyumba a chipembedzo achikhalidwe nthawi imeneyo. Koma chifukwa cha kukanidwa chifukwa cha chikhalidwe. Anakakamizidwa kutenga uthenga wawo kwa okhulupirira amene anali okonzeka kulandira uthenga.

MANTHA PA TSOGOLO

Dongosolo limathana ndi mantha obwera chifukwa cha tsogolo. Anthu ena amachita mantha ndi tsogolo ndipo safuna kuganiza komanso kupanga dongosolo. Koma simukuyenera kuwopa chifukwa Mulungu amayang'anirabe. Akudziwa kale dongosolo la moyo wanu. Mukungoyenera kumufunsa Mulungu kuti abvumbulutse kwa inu.

Pakuti ndidziwa malingiriro amene ndilingiririra inu, ati Yehova, malingiriro a mtendere, si a coipa, akukupatsani inu adzukulu ndi chiyembekezero. (Yeremiya 29:11).

KUNYALANYAZA

Anthu ena amalephera kupanga dongosolo ndi kuyang'anira bwino zinthu chifukwa zimatenga nthawi ndipo ndi ntchito yaikulu. Anthu amenewa amanyalanyaza. Kunyalanyaza ndi ulesi. Ntchito ya ulsesi yafotokozeredwa mu Miyambo 24:30-34. Sizimabweretsa kholola la uzimu.

KUCHITA MANTHA NDI KULEPHERA:

Mdindo osakhulupirira pa Mateyu 25:14-30 anachita mantha ndi kulephera, kufikira sanayesere kugwiritsa ntchito zimene anapatsidwa.

Nthawi imene mumalephera ndi imene mumasiya kuyesera. Thomasi Edison, amene anabweretsa nzeru yopanga magetsi mdziko la Amerika anayesera kambirimbiri kokwananira mazanamazana koma analephera. Kenako Bambo Edson anapambana pakubwera ndi nzeru ya magetsi.

Baibulo linadzadza ndi nkhani za anthu amphamvu amene analephera koma anapambana chifukwa chakuti sanasiye kuyesera.

Kulempha kukonzeka kumatanthawuza kukonzekera kulephera.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani ndime yotsogolera.
2. Fotokozani tanthauzo la” kuyang’anira potsatira cholinga.”
3. Lembani chifukwa chani kuyang’anira potsatira cholinga ndikofunika.
4. Lembani mwachidule zotchinga zina zimene mungakumane nazo ndipo fotokozani kuti mungathane nazo bwanji.

Mayankho a mafusowa ali m’chaputala chomaliza kumapeto kwa bukuli

KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

1. Zitsanzo zina zadongosolo M'baibulo ndi izi:

- Genesisi 1-3, Mulungu anapangiratu dongosolo la chilengedwe, Anapanga dongosolo la munthu ndipo anawululula dongosolo la chipulumutso.
 - Nowa anapanga dongosolo lakamangidwe ka chombo: Genesisi 6.
 - Abraham anapanga zolinga pa ulendo wa kapolo wake Elieza. Genesis 24.
 - Yosefe anapanga dongosolo pa zaka za chilala. Genesis 41.
 - Mose anapatsidwa dongosolo kuti akapululumutse ana a Israeli kuchokera kukapolo. Eksodo 3-4.
 - Dongosolo la likasa linali la tsatanetsatane: Eksodo 24:12-40:38.
 - Mbuku la Numeli tiwona dongosolo la kalemba wa anthu (1:1-54) ndi mayalidwe a misasa (2:1-34).
 - Yoswa anapanga dongosolo mwatsatanetsatane kuti atsogolere a Israeli a kalande ndi kukagawa dziko lamalonjezano: Buku la Yoswa.
 - M'buku la Oweruza, ndondomeko zosiyanasiyana za chipulumutso zimene Mulungu anazichita.
 - Rute anatsatira dongosolo kuchokera kwa Naomi lokhudza Boazi. Buku la Rute.
 - Davide anakozeka kukapha chimphona: 1 Samueli 17.
 - Mfumu Hezekiya anakonza dongosolo lobweretsa pamodzi Israeli. Anapangaso dongosolo lokonzaso Kachisi ndi kumanga njira za madzi za Yerusalem: 2 Mbiri 28-31: 2 Mafumu 16-20.
 - Nehemiah anapangaso dongosolo lakuti amangeso linga: Buku la Nehemiah.
 - Aneneri achipangano chakale anawululula dongosolo la Mulungu pa dziko lawo.
 - Yesu: Chipangano chatsopano chinadzadza ndi zinganizo zonedwa ndi Yesu, zokhudza cholinga ndi dongosolo lake kuti akwaniritse cholinga cha Mulungu pa moyo ndi utumiki wake. Yesu anawuza cholinga ndi dongosolo lake kwa omutsatira ndi okhulupirira onse.
- Ntumwi Paulo anapanga dongosolo: Akanakhala kuti sanapange dongosolo Mzimu woyera sanasintha monga zinanenedwa buku la Machitidwe 16:6-10.
- Buku la Chibvumbulutso linawulura ndondomeko za Mulungu pa tsogolo.
1. Werengani za ndondomeko m'buku la Miyambo. Onani 13:16; 14:8; 15:22; 16:3, 9; 24:34; 29:18.
 2. Monga m'mene Chaputalachi cha tsindikira, dongosolo limene tikuphuzira ndi dongosolo lopangidwa motsogozedwa ndi Mzimu woyera. Sikupanga dongosolo

monga m'mene dziko lapasi limapangira. Simuyenera kutengera mabugwe adziko lapansi pa chitsogozo.

Onani machenjezo a ndondomeko za dziko lapansi mu ndi yotsatirayi:

Tsoka kwa ana opanduka, at Yehova, amene atenga uphungu koma si pa ine: napangana pangano opanda mzimu wanga, kuti aonjezere chimo ndi chimo; amene

ayenda kutsikira ku Aigupto, osafunsa kukamea kwanga, kuzidzimbaitsa iwo okha ndi mphavmvu za Farao, ndi kukhulupirira mthunzi wa Aigupto! (Yesaya 30; 1-2)

3. Werengani nkhani ya Elisa ndi chodabwitsa chakuchulukitsa mafuta zolembedwa pa 2 Mafumu 4:1-7. Mulungu anachulukitsa mafuta kuti akwaniritse zotengera zonse zimene mkazi anakonza. Nanga akanapanda kukonza chotengera chirichonse? Mafuta, chuma chopambana chikanatayika ndipo Mulungu sakanathanso kuchulukitsa chifukwa sanali okonzeka kulandira.

Kodi ndi zotheka Mulungu kutipatsabe madalitso ake pa moyo wanthu ngati titakhala okonzeka kulandira?

CHAPUTALA 2 MULUNGU WA CHOLINGA

ZOLINGA:

Mukamaliza Chaputalachi muyamba kukwanitsa kuchita izi:

- Kufotokoza cholinga cha Mulungu.
- Kufotokoza kufunika komvetsetsa cholinga ndi dongosolo la Mulungu.
- Kupeza zida zimene Mulungu amazigwiritsa ntchito kuti akwaniritse cholinga ndi ndondomeko zake.
- Kufotokoza kuti utumiki wa Yesu umagwirizana bwanji ndi cholinga ndi dongosolo la Mulungu.
- Kufotokoza kuti utumiki wa Mzimu Woyera ugwirizana bawnji ndi cholinga ndi dongosolo la Mulungu.

NDIME YOTSOGOLERA:

Anatizindikiritsa ife chinsinsi cha chifuniro chache, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa Iye, kuti pa makonedwe a makwaniridwe a nyengo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Khristu, za kumwamba ndiza padziko (Aifeso 1:9-10)

MAU OTSOGOLERA

Mulungu, ndi Mulungu wa cholinga ndi dongosolo. Ndi Mulungu wa chikonzekero. Kucholera ku chiyambi cha nthawi, monga m'mene tikudziwira, Mulungu anakonzeratu ndikugwira ntchito kuti akwaniritse cholinga chake mdziko lapansi.

Munthu ndi chida chimene Mulungu amachigwiritsa ntchito kuti akwaniritse cholinga chake. Amagwira ntchito kudzera mwa munthu, mtundu, ndi thupi lake la uzimu, mpingo wa Yesu Khristu. Makamaka Mulungu amadziwa ndi kugwiritsa ntchito amene amapanga dongosolo ndi cholinga cha moyo komanso utumiki wawo mogwirizana ndi cholinga cha Mulungu.

Mukapanda kuvetsetsa cholinga cha Mulungu, simunagwirizane ndi dongosolo lake. Ichi ndi chifukwa chake atumiki ambiri amalephera. Mphunziroli, muphunzira cholinga chachikulu cha Mulungu ndipo mukhala mukuwonanso dongosolo lokhala nawo maziko a M'Baibulo. Kukhala ndi kuthekera kowona cholinga chanu ndi kupanga dongosolo logwirizana ndi dongosolo la Mulungu.

MULUNGU WA CHIKONZERO

Mulungu ndi Mulungu wa chikonzero. Phunzirani izi kuchokera ku malo awa:

-Mulungu anakonza mwamba, mphando wake wa chifumu ndi ufumu: Masalimo 103:19; Miyambo 8:27.

-Anakonza dziko chifukwa cha anthu: Genesisi 1-3

-Mulungu atha kukonzekeretsa chinachilichonse chifukwa cha cholinga chake. Mbuku la Yona lokha. Mulungu anakozekeretsa ndipo anagwiritsa ntchito nsomba, (Yona 1-4).

-Mulungu anakonzekeretsa Yesu kuti akhale nsembe ya machimo athu: Ahebri 5:10; Zefaniya 1:7.

-Yesu asanadze, munthu wina dzina lake Yohane anatumidwa kudzakonza njira yake. Luka 1:76; 3:4

-Mulungu anakonza dziko lokongola komanso lamuyaya kuti ife tikakhale moyo wathu wonse. Ahebri 11:16

-Anakonza ufumu umene ife tikakhala mbali imodzi: Yohane 14:2-3.

-Tinawuzidwa kuti chimene Yesu anakakozera onse onkonda ndi omudziwa iye diso linalililose silinawone ngakhale khutu silinave. 1 Akolinto 2:9.

-Kwa osakhulupirira onse anakonza chiweruzo: Miyambo 19:29.

-Gehena anakonzedwera satana ndi angelo ake. Mateyu 25:41

-Mulungu akuyang'ana anthu okonzedwa ngati nkwati kwa mwamuna wake. Chivumbulutso 21:2

Kuchokera m'malo osiyasiyana awa muwona kuti, M'baibulo, anagwiritsa ntchito, anakonzekeretsa anthu kuchita ntchito yake:

-Nowa anakonza chombo mwachikhulupiriro: Ahebri 11:7

-Yosefe, anakonzedwa ndi mayesero komaso zowawa, napulumutsa dziko ku chilala: Genesis 41

-Mose anakozekeretsedwa m'chipululu: natsogolera mtumdu wonse m'chipululu: Buku la Eksodo.

-Estere anakoza phwando ndikupulumutsa ntundu wonse: Estere 7

- M'buku la oweruza ndi Mbiri muli ndanda wina wa atsogolo amene analephera nachita zoipa chifukwa mitima yawo inali yosakonzeka bwinobwino pamaso pa Mulungu. (2 Mbiri 12:14 ndi chimodzi mwa zitsanzo).

Mulungu amgwiritsa ntchito anthu akonzeka. Chifukwa cha ichi ndife olamulidwa kukhala okonzeka:

-Konzekerani kukumana ndi Mulungu: Amosi 4:12

-Konzani mitima yani chifukwa cha Ambuye: 1 Samuel 7:3.

-Khalani ndi mtima okonzeka: 2 Mbiri 19:3

-Kozekeretsani mitima yanu pomfuna Ambuye: 2 Mbiri 27:6

-Khalani okonzeka ndipo konzekeretsaniso ena: Ezekieli 38:7

-Khalani okonzeka kunchito iriyose ndikugwiritsidwa ntchito ndi Ambuye. 2 Timoteo 2:2

-Khalani chida chokonzeka ku ulemerero wake: Aroma 9:23

Mulungu ndi Mulungu wa chikonzere. Amagwira ntchito kudzera mwa anthu okonzeka. Sakuyang'ana okhulupirira amene si olimbikitsika, ogonja, osambweretseka pamodzi komaso osaika zinthu mchimake. Akuyang'ana amuna ndi akazi amene ndi okonzeka. Yesu anafotokoza fanizo la kapolo amene amadziwa mbuye abwera koma sanakonzeka kukwaniritsa:

Ndipo kapolo uyo, wodziwa chifuniro cha mbuye wache, ndipo sanakonzeka, ndi kusachita zonga zachifuniro chachecho, adzakwapulidwa mikwapulo yambiri. (Luka 12:47)

Chifukwa chani Yesu ali okhudzika ndi chikonzekero? Chifukwa chani amagwiritsa ntchito anthu okonzeka? Kodi timakozekera chiyani?

MULUNGU WA CHOLINGA

Chikonzekero chirichonse cha Mulungu chagona pa cholinga chake. Sikuti ndi cholinga chosamveka bwino kapena chiyembekezo chake basi. Akugwira ntchito chifukwa cha cholinga chenichi komaso chokhazikika. Cholinga cha Mulungu chinanenedwa moveka bwino m'mawu ake. Buku la Aifeso linamangirira bwino cholinga chake. Chiganizo cha cholinga cha Mulungu ndi ichi:

Monga mwa chitsimikizo mtima cha nthawi za nthawi, chimene anachita mwa Khristu Yesu Ambuye wathu.

Anatizindikiritsa ife chinsinsi cha chifuniro chache, monga kunamkkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa Iye, Kuti pa makonzedwe a makwaniritse a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Khristu, za kumwamba ndi za padziko (Aifeso 3:11; 1:9-10)

Mulungu afuna kuti onse akhale pa ubale wabwino wauzimu ndi iye:

Ambuye sazengereza nalo lonjezano, monga ena achiyesa chizengerezo, komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke koma kuti onse afike kukulapa. (2 Petro 3:9)

Cholinga cha Mulungu ndi chakuti anthu onse alandire chikhululukiro cha machimo kudzera mwa Yesu Khristu, ndikukhala pa ubale wabwino ndi iye, ndikukhala mbali imodzi ya Ufumu wa Mulungu (Yohane 3)

Mulungu amakozekeretsa anthu kuti awagwiritsa ntchito ndikukwaniritsa cholinga chake. Amene cholinga chawo ndi ndondomeko zao zimafana ndi za Mulungu amadzozedwa. Ngati simungavetsetse cholinga cha Mulungu, cholinga chanu ndi dongosolo lanu silingafanane ndi za Mulungu.

Mwachitsanzo, pamene Yesu anawulula kwa akuphuzira ake kuti akazuzika ndi kumwalira, Petro anamutsutsa. Iye sanamvetsetsa cholinga cha Mulungu. Sanagwirizane ndi dongosolo la Mulungu. Yesu anamutsutsa nati:

Koma iye anapotoloka, napenya ophunzira ache, namdzudzula Petro, nenena, Choka, pita kumbuyo kwanga, Satana iwe; popeza susamalira zinthu za Mulungu, koma za anthu. (Marko 8:33)

Mfumu Davide ndi munthu amene anagwirizana ndi cholinga cha Mulungu:

Pakutitu, Davide, m'mene adautumikira uphungu wa Mulungu m'mbadwo mwache mwa iye yekha, anagona tulo, naikidwa kwa makolo ache naona chibvundi; (Machitidwe 13:36)

Baibulo limatitsimikizira kuti zolinga za Mulungu zidzakwaniritsidwa.

Yehova wa makamu walumbira, nati, Ndithu monga ndaganiza, chotero chidzacidwa; ndipo monga ndapanga uphungu, chotero chidzakhala; (Yesaya 14:24)

Umenewu ndi uphungu wopangira dziko lonse; ndipo ili ndi dzandja lotambasulidwa pa amtundu nse. Pakuti Yehova wa makamu wapanga uphungu, ndani adzaleketsa? Ndi dzanja lache latambasulidwa, ndani adzalibweza? (Yesaya 14:26-27)

MULUNGU WA DONGOSOLO

Mulungu ali ndi cholinga chokhazikika ndipo amachitapo kanthu pa ndondomeko zake kuti zikwaniritsidwe. Amagwiritsa ntchito anthu, maiko, Yesu, Mzimu Woyera ndi mpingo kukhala mbali imodzi ya dongosolo lake.

Mchipangano chakale, anagwiritsa ntchito atsogoleri amphavu ngati Nowa, Abraham, Yosefe, Mose. Anadzozaso aneneri, mafunu, ndi oweruza kuti akwaniritse cholinga chake. Nthawi ya chipangano chatsopano Mulungu anagwiritsa ntchito anthu ngati Yohane mbatizi, ophuzira a Yesu, Paulo, Timoteo, Banabas ndi ena ambiri.

Mulungu anatenga anthu ochimwa amene sakanatha kufana naye, nawulula dongosolo lawo loyipa, kuti akwaniritse cholinga chake. Mulungu sanapange zochita zawo zoipa, koma anazigwiritsa ntchito posazitengera nakwaniritsa dongosolo lake.

Mwachitsanzo, Mulungu anati kwa Falawo oyipa ku Egypt:

Koma ndithu chifukwa chache ndakuimika kuti ndi kuonetsa mphamvu yanga, ndi kuti alalikire ddzina langa pa dzikko lonse lapansi. (Eksodo 9:16)

Moyo ndi utumiki unamagirilika pa cholinga cha Mulungu. Cholinga cha Mulungu chikatha moyonso umathera pompo.

Pakutitu, Davide, m'mene adautumikira uphungu wa Mulungu m'mbadwo mwache mwa iye yekha anagona tulo naikidwa kwa makolo ache, naona chibvundi (Machitidwe 13:36)

MAYIKO:

Nthawi ya Chipangano Chakale Mulungu anadzutsa mtundu wa Israeli kuti akwaniritse cholinga ndi dongosolo lake mdziko lapasi. Ngati mtundu, cholinga cha Israeli chinali kuvumbulutsa dongosolo la Mulungu kwa amitundu. Mowirikiza analephera ntchito imeneyi.

Chifukwa cha ichi chiweruzo chinadza pa Israeli kudzera kwa maiko amitundu ochokera kumadera ozungulira. Mulungu anali odzipereka kuti akwaniritse cholinga chake kufikira anagwiritsa ntchito zochita zawo ngakhale zinali zauchimo. Mulungu sanavomereza zochita zao chifukwa zinali zoipa koma anangozigwiritsa ntchito chabe.

YESU KHRISTU:

Kwa nthawi yaitali, cholinga cha Mulungu chinakhala chinsinsi. Kuchokera pa chiyambi, Mulungu analonjeza mpulumutsi amene kudzera mwa Iye chikhululukiro pa machimo chidzapezeka kwa anthu onse.

Lonjezo linaperekedwa koyamba kwa Adamu ndi Hava atachimwa m'munda wa ku Eden. Mulungu anati:

Ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo ndi pakati pa mbeu yako ndi mbeu yache; ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira chitende chache. (Genesis 3:15)

Ichi chinali chiyambi cha malonjezano ambiri a mpulumutsi. Kwa nthawi yaitali Yesu sanawulule tsatanetsatane wakuti adzakwaniritsa bwanji lonjezano limeneri. Chinali chinsisi chachikulu.

Pambuyo pake, nthawi ya aneneri a m'Chipangano Chakale, Mulungu anapereka tsatanetsatane wa dongosolo lake. Mchipangano Chatsopano, zinakwaniritsidwa pamene Mulungu anatuma mwana wake, Ambuye Yesu Khristu, kufera machimo anthu onse.

Dongosolo la Yesu silinakhalenso chinsisi. Madongosolo ndi zolinga zake zinawululidwa mowonetseratu mwa Yesu Khristu:

Anatizindikiritsa ife chinsinsi cha chifuniro chache, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti pa makonzdwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanite pamodzi zonse mwa khristu, za kumwamba ndi za padziko. (Aefeso 1:9-10)

Kuchokera ali wachichepere, Yesu amadziwa kuti cholinga cha Mulungu kunali kupereka chipulumutso kwa anthu onse, ndikupanga onse kuti akhale pa ubale wabwino ndi Yesu Khristu.

Yesu anakhala moyo wake kuti akwaniritse cholinga cha Mulungu pa dziko lapansi. Ngakhale anali mwana, Yesu samakhudzika ndi madongosolo komanso zolinga zake, koma za Mulungu Atate.

Ndipo iye anati kwa iwo, kuli bwanji kuti munalikundifunafuna ine? Simunadziwa kodi kuti kundiyenera ine ndikhlae m'zache za Atate wanga? (Luka 2:49).

Moyo ndi utumiki wa Yesu unayima kwambiri pa cholinga cha Mulungu. Dongosolo, chisankho ndi chochitika chilichonse mu utumiki wake zinalunjika pa cholingacho.

Mzimu wa Ambuye uli pa Ine, Chifukwa chache Iye anandidzodza Ine ndiuze anthu osauka uthenga Wabwino: anandituma ine kulalikira am'nsinga

mamasulidwe, ndi akhungu kuti apeynenso, Kukurutsa ndi ufuru ophwaynika, Kulalikirira chaka chosankhika cha Ambuye. (Luka 4:18-19)

Ichi ndi chiganizo chimodzi mwa ziganizo zambiri zonedwa ndi Yesu. Gawo la “Kupitiriza Kuphunzira” m’chaputalachi, likuwonetsa ziganizo zambiri zimene zinanenedwa zokhudzana ndi utumiki. Yesu anatuma ophunzira ake, kuphatikizirapo okhulupirira onse kuti akwaniritse cholinga chake:

Ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani ine ndiri pamodzindi inu masiku onse akufikira chimaliziro cha ntahwi ya panso pano. (Mateyu 28:20)

Pitani tsamba la “Kupitiriza Kuphunzira”, phunzirani ziganizo za cholinga chimene Yesu anawuza omutsatira ake. Izi ndizofunika, chifukwa ngati muli okhulupirira ndinuso otsatira Yesu Khristu.

MZIMU WOYERA:

Mzimu Woyera ndi mbalinso imodzi ya dongosolo la Mulungu. Yesu atabwereranso kumwamba, mphamvu ina inaperekedwa mwakutsiridwa kwa Mzimu Woyera monga m’mene anafotokozera pa machitidwe 4. Izi zimatchulidwa kuti ubatizo wa mzimu woyera.

Mphamvu ya Mzimu Woyera inaperekedwa kuti cholinga cha Mulungu chikwaniritsidwe m’dziko lapasi:

Komatu mudzalandira mphavu, Mzimu woyera atadza painu; ndipo mudzakhala mboni zanga m’Yerusalemu, ndi m’Yudeya lonse, ndi m’samariya, ndi kufikira malekezero ache a dziko. (Machitidwe 1:8)

Utumiki wa Yesu Khristu ndiofunika kwambiri kuti zolinga za Mulungu zikwaniritsidwe kufikira “Harvestime International Institute” anakonza phunziro palokha lakuti “Utumiki wa Mzimu Woyera”.

Phunziro lina loperekedwa ndi “Institute” ndi “Mphamvu ya Mfundo”, limafotokoza za ubwino wa mphamvu ya uzimu kuti tikwaniritse dongosolo la Mulungu lochulukana mwakulalikirira uthenga.

Kuwonjezera pa mphamvu, Mzimu Woyera umaperekanso chitsogozo ndi malangizo kwa okhulupirira kuti akwaniritse cholinga ndi dongosolo la Mulungu. Mzimu Woyera ndi nkhalapakati wa munthu ndi Mulungu chifukwa chakuti iye amadziwa cholinga cha Mulungu komaso amadziwa mzimu wa munthu.

Ndipo iye amene asanthula m’mitima adziwa chimene achisamalira mzimu, chifukwa apempherera oyera mtima monga mwa chifuniro cha Mulungu. (Aroma 8:27)

Kuti cholinga cha Mulungu chikwaniritsidwe, Mzimu Woyera amagwira ntchito ndi inu. Mukamalankhula mau ake, amakudzozeni kuti mutsutse osakhulupirira pa tchimo ndikuwatsogolera kuti avomere Uthenga Wabwino. (Onani Yohane 16:7-11)

MPINGO:

Mphamvu ya Mzimu Woyera inaperekedwa kwa onse okhulupirira amene anabadwa mwatsopano. Okhulupirira owona ali mbali imodzi ya mpingo, umene ndi chida chimene Mulungu amagwiritsa ntchito kuti akwaniritse cholinga ndi ndondomeko zake.

Ndi kuwalitsira onse adziwe makonedwe a chinsinsicho, chimene chinabisika kuyambira kale kale mwa Mulungu wolenga zonse; kuti mu Eklesia azindikiritse tsopano kwa akulu ndi maulamuliro m'zakumwamba mzeru ya mitundi mitundi ya Muungu. (Aefeso 3:9-10)

Mulungu amagwira ntchito m'moyo wa okhulupirira kuti akwaniritse zolinga chake:

Koma tsopano mwa Yesu Khristu inu amene munali kutali kale anakusendezani mukhale pafupi m'mwazi wa Khristu. (Afilipi 2:13)

“Kuchita zonkondweretsa iye” zitanthauza kuti kugwira ntchito mwa inu kuti akwaniritse cholinga chake ndi dongosolo m'moyo wanu. Izi zitanthawuza chipulumutso, chidzalo cha Mzimu Woyera, kukugwiritsani ntchito potumikira ena, ndikukufananitsani ndi mwana wake Yesu Khristu.

Amagwiranso ntchito m'moyo wanu kuti akwaniritse cholinga chake:

Ndipo musapereke ziwalo zanu kuuchimo, zikhale zida za chosalungama; koma mudzipereke inu nokha Kwa Mulungu, monga amoyo ataturuka mwa akufa, ndi ziwalo zanu Kwa Mulungu zikhale zida za chilungamo. (Aroma 6:13)

Mukalolera kukhala chida cha chilungamo cha Mulungu, zikutanthawuza kuti mukubweretsa moyo wanu ndi utumiki kufanana ndi cholinga komanso dongosolo lake. Pakupanga izi, mukhala chida chimene iye angachigwiritse ntchito.

Chifukwa chache tiri atumiki m'malo mwa Khristu, monga ngati Mulungu alikudandaulira mwa Ife; tumiriza inu m'malo mwa Kristu, yanjanitsidwani ndi Mulungu. (2 Akorinto 5:20)

Ndipo ochita naye pamodzi tindandauliranso kuti musalandire chisomo cha Mulungu kwachabe inu (2 Akorinto 6:1)

Ngati Mulungu sangagwire ntchito mwa inu komanso ndi inu, ntchito yanu yonse singapindule:

Akapanda kumanga nyumba Yehova, akuimanga agwiritsa ntchito chabe; akapanda kusunga mudzi Yehova, mlonda adikira chabe. (Masalimo 127:1)

Utumiki wanu sungapambane pokhapokhapo utamangidwa pa zolinga za Mulungu osati za munthu:

Ndipo tsopano ndinena ndi inu, Lekani anthu amenewa, nimuwalole akhale; pakuti ngati uphungu umene kapena ntchito iyi ichokera ka anthu, idzapasuka; koma ngati ichokera kwa Mulungu simungathe kuwapasula; kuti kapena ungaepezeke otsutsana ndi Mulungu. (Machitidwe 5:38-39)

CHOLINGA NDI DONGOSOLO LA MULUNGU

Kuchokera pa chiyambi cholinga cha Mulungu sichinasinthe. Anakhala nawo madongosolo ambiri okhudzana ndi cholinga chake koma cholinga chimakhalabe chimodzi modzi.

Monga mwaphunzira, Mulungu anawulula cholinga chake chenicheni m'mawu ake amene analembedwa. Anavumbulutsanso dongosolo lake lakuti mpingo, umene uli chida chimene amachigwiritsa ntchito kuti akwaniritse cholinga chake.

Koma ngati okhulupirira mukuyenera kupanga madongosolo mwatsatanetsatane ngati mukufuna kukwaniritse cholinga chake. Apa ndipamene dongosolo ndikukhazikitsa zinthu mchimake zimakhala zofunika. Mukuyenera kuzindikira cholinga chanu chanicheni m'cholinga cha

Mulungu. Kenako Mukuyenera kupanga madongosolo awutumiki wanu kufanana ndi cholinga.

Mphuziro lotsatirali muyamba kuchita izi mukamaphuzira kapangidwe ka chiganizo chacholinga.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osaonera.
2. Kodi cholinga cha Mulungu ndi chiti?
3. Ndichifukwa chani kuli kofunika kuvetsetse cholinga ndi ndondomeko za Mulungu?
4. Mulungu amagwira ntchito kudzera mzida ziti kuti akwaniritse cholinga ndi madongosolo lake?
5. Nenani mwachidule ubale pakati pa cholinga ndi dongosolo la Mulungu.
6. Lembani mwachidule ubale pakati pa utumiki wa mzimu wa Mulungu ndi cholinga komaso dongosolo la lake.
7. Fotokozani utumiki wa mpingo mogwirizana ndi cholinga komaso dongosolo la Mulungu.

(Mayankho amafusowa aperekedwa pa a chaputala chomalizira m'bukuli)

KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

1. Yesu Khristu amadziwa zambiri zokhudzana ndi mbali yake m'cholinga ndi dongosolo la Mulungu. Werengani zambiri za izi m'mabuku otsatirawa:

Mateyu 5:17; 8:3, 7; 9:13; 10:34-35; 13:41-42; 15:24; 18: 11, 20; 19: 28, 29; 20:18-19, 28; 21: 35:31; 26:24, 29, 32, 39, 64

Matheyu: 5:17; 8:3,7; 9:13; 10:34-35; 13:41-42; 15:24; 18:11,20; 19:28-29; 20:18-19,28;
21:13; 24:35; 25:31; 26:24,29,32,39,64

Marko: 1:38; 2:17; 10:33-34, 45; 14:21

Luka: 2:49; 4:18-19,43; 5:32; 9:22,56; 11:49; 12:51; 13:32-33; 19:5,10; 22:37,69;
24:44,46-47

Yohane : 3:16-17; 4:34; 5:30,43; 6:37-40,51; 7:16,33; 8:26,29,49-50; 9:4, 38-39;
10:10,16- 18; 12:24-27,32,46,49-50; 13:5; 14:2,16-18; 18:36; 16:12,22,25; 18:37;
12:2427; werengani chaputala 17 chonse chimene chikufotokoza kwambiri
mokhudzana ndi cholinga chake.

2. Werengani kwambiri za cholinga cha ophunzira a Yesu Khristu.

Mateyu: 7:33; 9:37-38; 10:7-8, 38-39; 16:24-25; 28:18-20

Marko: 1:17; 16:15-18; 8:34-35

Luka: 5:10; 9:2; 10:2-9; 12:29; 14:26-27,33; 22:29; 24:46-49

Yohane: 4:35; 6:27; 15:16; 20:21

Machitidwe: 1:4-5, 8

3. Werengani zambiri zokhudzana ndi cholinga m'machaputala awa:

Ezara 4:5; Masalimo 17:3; Miyambo 15:22; Mlaliki 3:1,17; 8:6; Yesaya 14:24-27;
23:9;
46:11; Yeremiya 4:28; Daniel 1:8; Machitidwe 11:23; 19:21; 20:3; 26:13; Aroma
8:28;
9:11,17; II Akolinto 9:7; Aifeso 1:4-11; 3:11; Akolose 4:8; 2 Akolinto 1:9; 3:10; I
Yohane 3:8

4. Davide anatomikira cholinga cha Mulungu m'badyo wake (Machitidwe 13:36).
Chifuniro cha Mulungu m'chani mumbadyo wanu.

CHAPUTALA 3 CHOLINGA

ZOLINGA

Mukamaliza chaputalachi muyamba kukwanitsa kuchita izi:

- Kupereka tanthauzo la “Mau a Cholinga”.
- Kufotokoza ubwino wa cholinga.
- Kufotokoza kusiyana kwa cholinga ndi chokhumba.
- Kufotokoza kusiyana kwa mawu a cholinga ndi mau a chikhulupiriro.
- Kulemba mau a cholinga.
- Kulemba ndandanda wa njira zimene anthu akhoza kudziwira njira ya cholinga.

NDIME YOTSOGOLERA

Potero, penyani bwino umo muyendera, si monga opanda nzeru, koma monga anzeru; akuchita machawi, ppopeza masiku ali oipa. (Aefeso 5:15-16).

MAU OYAMBA

Phuziro lapitali munaphuzira kuti Mulungu ndi Mulungu wa cholinga ndipo akupitilizabe kupanga ndikugwiritsa ntchito madongosolo ake kuti akwaniritse cholinga chake.

Mulungu amadzoza ndikuwagwiritsa ntchito amene amavetsetsa cholinga chake ndipo ali ofuna kukhala mbali imodzi ya zolinga zake. Moyo ndi utumiki zikuyenera kukhala zogwirizana. Mukuyenera kukhala ndi kutumikira ndi ganizo la cholinga chimodzi chimene chinatsogolera moyo ndi utumiki wa Yesu Khrist.

Phuziloli likuthandizani kapangidwe ka mau a cholinga kogwirizana ndi cholinga komanso madongosolo a Mulungu.

MAU A CHOLINGA

Mau a cholinga ndi mau amene amanena cholinga chakukhala ndi moyo. Amafotokoza kuvetsetsa kwanu kwa ntchito yeniyeni imene Mulungu anakupatsani. Ndi mau a masophenya ndi chikhulupiriro. Mau a cholinga amanena chifukwa chani mukukhala ngati bungwe, utumiki, kapena mpingo. Imanena chifukwa chenicheni cha utumiki wanu ngati guru. Kwa anthu, mau a cholinga amanena za mbali yanu m’dogosolo la Mulungu.

Mau a cholinga si mau a chiphuzitso. Mau a chiphuzitso amakuwuzani ziphuzitso zimene utumiki wanu umakhulupirira. Ndibwino kukhala ndi mau a chikhulupiriro, koma samafanana ndi mau a cholinga. (Chitsanzo, mau a chiphuzitso onani appenix mbukuli)

Cholinga chimasiyana ndi “chokhumba.” Cholinga ndi mau amene amafotokoza chifukwa chani utumiki ulipo. “Zokhumba” ndi mau a madongosolo amene agwiritsidwe ntchito kuti akwaniritse cholinga.

(Zokhumba) si zimene inu mupange. Cholinga chifotokoza chifukwa chani inu mulipo. Muphuzira zambiri za (Zokhumba) m’phuziro lotsatirari pa za kapangidwe ka dongosolo. Cholinga si zochitika m’chalitchi. Zochitika ndi zokwaniritsira madongosolo amene akugwirizana ndi cholinga. Mau a cholinga amawonetsa chifukwa chenecheni chimene

utumiki wanu ukupezekera. Zimanena mwachidule mbali ya utumiki wanu mutumiki wanu munthupi la Khristu.

Baibulo liri ndi ndandanda wa amuna komaso akazi amene anazindikira cholinga chawo chenicheni m'dongosolo la Mulungu. Tiwonapo m'modzi mwa anthu amenewa, Ntumwi Paulo.

Paulo amadziwa cholinga chenicheni chimene anawawuzanso ena. Analemba Timoteo:

**Koma iwe watsatsata chiphunzitso changa, mayendedwe,
chitsimikizo mtima, chikhulupiriro, kuleza mtima, chikondi, cipiriro
(2 Timoteo 3:10)**

Masomphenya ake anali kukwaniritsa cholinga:

**Si kunena kuti ndinalandira kale, kapena kuti ndatha konzeka wamphumphu,
koma ndilondetsa, ngatinso ndikachigwire ichi chimene anandigwirira Yesu
Kristu. (Afilipo 3:12)**

Mulungu anamuwuzza Paulo cholinga cheke:

**Koma Ambuye anati Kwa iye, Pita; pakuti iye ndiye chotengera changa
chosakhika, chakunyamula dzina langa pamaso pa amitundu ndi mafumu ndi
ana a Israeli; (Machitidwe 9:15)**

Munaphuzira m'chaputala chapitachi kuti cholinga cha Mulungu ndi kuti anthu onse afikire kuchidziwitso cha Ambuye wanthu Yesu Khristu. Cholinga cha Paulo mutumiki chinali chogwirizana ndi cholinga ndi madongosolo a Mulungu. Paulo akanalemba mau cholinga zikanakhala chonchi:

“Cholinga cha utumiki ndi kutengera dzina la Mulungu kwa:

.....Amitundu (osati a Israeli)
.....Mafumu (Atsogoleri)
.....Mafumu a Israeli (Ayuda)”

UBWINO WA CHOLINGA

Mau a cholinga ndi abwino chifukwa:

AMAPEREKA CHITSOGOZO:

Masomphenya ndi chifanifani m'maganizo anu cha zimene mukukufuna kukwaniritsa. Baibulo limati:

**Popanda chibvumbulutso anthu amasauka; koma wosunga chilamulo adalitsika.
(Miyambo 29:18)**

Mulungu anapereka masopenya ake m'au a Mulungu, koma mukuyeneraso kukhala ndi masopenya. Mukuyenera kukhala ndi chidziwitso chenicheni cha zinthu zenizeni zimene mukufuna kuzikwaniritsa mutumiki wanu. Mukuyenera kutumikira masopenya alipo kale.

Mulungu akakhazikitsa masopenya, samasintha maganizo ake monga m'mene anthu amachitira. Anthu akasiya masopenya amene Mulungu anawapatsa pamakhala chisokonezo, mavuto, ndi kulephera.

KULIMBIKITSA MAONEDWE A ZINTHU OGWIRIZANA NDI BAIBULO.

Cholinga chimalimbikitsa maonedwe abwino a zinthu chifukwa mumapanga kawuniwuni kaye wa malo ozungulira musanabwere ndi cholinga. Mukamapanga izi mumazindikira zosoweka zauzimu mdera lanu, mtundu wanu ndi dziko lonse lapansi.

Chitsanzo, Paulo anapanga kawuniwuni mumzinda wa Atene. Mtima wake unatakasika koma chifukwa cha kumvetsetsa cholinga cha utumiki, anagawana nawo Uthenga Wabwino anthu a mzindawu.

Cholinga chimalumikizana kwambiri ndi zofunika pakati pa anthu. Kuzindikira zofunika kumalimbikitsa mawonedwe azinthu ogwirizana ndi Baibulo. Mumayamba kuliona dziko monga m'mene Mulungu amalionera.

KUPEREKA MWAYI WOPANGA DONGOSOLO:

Cholinga chimapereka mwayi wopanga dongosolo. Mukadziwa cholinga chanu, mutha kupanga madongosolo amene atha kukuthandizani kuti mukwaniritse masopenya. Madongosolo anu amakhala osadziwika bwinobwino ngati cholinga chanu chili chosamveka bwinonso.

Pali ntchito zabwino zambiri zimene mutha kupanga. Mutha kukhala otanganidwa chifukwa cha Mulungu, koma ntchito yeniyeni imene munapatsidwa kuti mukwaniritse ndi itiyo. Chimenechi ndi chimene mukuyenera mukafotokozere m'mene munachitira. Ndi zofunika kwambiri kuti muzipanga zimene Mulungu anakuitanirani kuti muchite, ndipo muzichita bwino kusiyana ndi kukwaniritsa zinthu zambiri.

Yesu anatsindika cholinga chimene chikuyenera kukhala choyambirira kwa Malita pamene anati:

Koma Ambuye anayankha nati kwa iye, Marita, marita, uda nkhawa nubvutika ndi zinthu zambiri. (Luka 10:41)

Cholinga ndi maziko othandiza kapezedwe ka zinthu zoyenera kuikidwa poyambirira. Ngati zinthu zanu zoyambirira zifanana ndi za Ufumu wa Mulungu zinthu zonse zofunika kuti mukwaniritse masopenya anu chidzaperekedwa:

Koma muthange mwafuna Ufumu wache ndi chilungamo chache, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu. (Mateyu 6:33)

Ufumu wa Mulungu ukakhala patsogolo chuma, anthu, zinthu ndi chirichonse mungachifune kuti utumiki uyenende bwino chidzaperekedwa.

Utumiki uliwonse uli ndi zinthu zimene zimayenera kuikidwa patsogolo. Utumiki umene ulibe zinthu zoyambirira umatha kukhala nacho chifukwa cha kukakamizika ndi zofuna za anthu kapena chizolowezi. Mumalola kuti dziko likupangireni zinthu m'malo mwakuti Mulungu akupangileni.

Moyo wanu ukuyenera kukhala ndi cholinga chifukwa nthawi yatsala pang'ono kuti Yesu azibwera, zofuna ndi zambiri, komanso masiku ndi oyipa.

Potero, penyani bwino umo muyendera, si monga opanda nzeru, koma monga anzeru; akuchita machawi, popeza masiku ali oipa. (Aefeso 5:15-16)

Madongosolo a Paulo, konse kumene anayenda ndikutumikira, anagwirizana ndi cholinga chimene Mulungu anamuitanira. Sanapange ntchito zabwino chabe. Anapereka moyo wake kugwira ntchito imene anamuitanira.

KUPEWA CHISOKONEZO

Pamene masophenya asoweka chisokonezo chimadza. Ngwirizano sumatheka m'maganizo kapena mzochitika, nthawi zambiri kusamvetsetsana kumadza.

M'chipangano chakale, atsogoleri amagwiritsa ntchito zitoliro kubweretsa anthu pamodzi nthawi ya nkondo. Maliridwe a chitoliro amayenera kukhala okweza ngati chizindikiro, kupanda kutero pamakhala chisokonezo pakati pa Asilikali a Mulungu. (Numeli 10:9 ndi 1 Akolinto 14:8). Cholinga chenicheni chiri ngati chitoliro cha nkondo. Chimaitana anthu kuntchito. Koma ntsogoleri amene akuitana anthu kunkhondo akuyenera kukhala ndi cholinga choveka bwino.

KULOLA KAUNIUNI:

Ngati mukudziwa cholinga cha utumiki wanu, mutha kupanga kauniuni kuti muwone ngati mukukwaniritsa dongosolo la Mulungu. Chifukwa chakuti Paulo anadziwa ndikuvetsetsa cholinga chake, amatha kupanga kauniuni wa utumiki wake ndi kunena kuti:

.....**Sindinanyozere masophenya a Kumwamba (Machitidwe 26:19)**

Muphuzirabe za kawuniwuni m'maphunziro otsatirawa.

UTUMIKI UMAKHALA NDI KUDZOZA KOMANSO MPHAMVU.

Chifukwa mukudziwa kuti cholinga chanu chikufanana ndi cholinga cha Mulungu mu utumiki wanu, Mulungu amadzoza utumiki wanu. Mutha kutumikira mwa mphamvu ndi ulamuliro chifukwa mukudziwa bwino lomwe chimene Mulungu anakuitanirani.

KUPANGA MAWU A CHOLINGA

Tsopano mupanga mawu a cholinga cha utumiki wanu chimene chikugwirizana ndi cholinga komanso madongosolo a Mulungu. Mukuyenera kukhala ndi mau anu a cholinga amene ayankhe funso iri: “Kodi utumiki wanga ukugwirizana bwanji ndi cholinga komanso madongosolo a Mulungu?”

Mukuyeneraso kukhala ndi mawu a cholinga amene akuyankha funso iri: “Kodi pali kugwirizana kotani pakati pa bungwe, chiyanjanao kapena mpingo ndi dongosolo la Mulungu?”

Ngati bungwe, chiyanjano kapena mpingo muli kale ndi mau a cholinga, onaniso pogwiritsa ntchito kalozera opatsidwa m’gawo la “Kupitiriza Kuphunzira” kumapeto kwa phunziroli.

Pakuti Yehova abwezeranso akulu wache wa Yakobo ngati ukulu wache wa Israeli; pakuti okhuthula anawakhuthula, naipsa nthambi zache za mpesa. (Habakuku 2:2)

Mukuyenera kulemba chifukwa cha Kutu....

1. Zimveke bwino: ngati ali maganizo chabe a cholinga m’mutu mwanu sizomveka. Kulemba “Mawu a Cholinga” kumafotokozera bwino chenicheni chimene Mulungu anakuitanirani kuti muchite.
2. Mutha kulumikizana ndi ena: anthu atha kulimbikitsika kukwaniritsa masophenya ndi kuwakaniritsa pokhapokhapo akwanitsa kuwerenga ndi kumvetsetsa.

Ndondomeko zimene mukhoza kupangira mawu a cholinga cha utumiki wanu nazi:

PEMPHERANI:

Mukuyenera kulumikizana ndi Mulungu kuti mupeze cholinga chanu mu utumiki. M’pempheni kuti akutsogolereni pamene mukuwerenga mau ndi kupanga kawuniwuni m’ malo akuzungulirani.

PANGANI KAWUNIWUNI WA MALO OKUZUNGULIRANI:

Kuti ntchito iyende bwino, cholinga chanu sichikuyenera kungogwirizana ndi cholinga cha Mulungu, pakuyenera kukhalanso mgwirizano ndi malo ozungulira. Cholinga chanu chikuyenera kugwirizana ndi zofuna za anthu amene Mulungu anakuitanani kuti muwatumikire.

Kawuniwuni wa malo ozungulira ndi maphuziro a anthu ndi malo amdera limene inu mukutumikirako. Chifukwa chakuti ndizofunika kwambiri, pali maphuziro okhazikika okhudzana ndi kawuniwuni ku **Harvestime International Institute**.

Ngati mukupanga maphunziro Institute monga mwa dongosolo lake ndiye kuti munamalizitsa kale phunziro la “Kawuniwuni wa Malo Ozungulira.” Onaniso uthenga umene munawupeza nthawi ya kawuniwuni ndipo ugwiritsani ntchito mukamalemba mawu a cholinga.

Ngati simunaphuzire maphunziro a “kawuniwuni wa malo ozungulira” ndibwino kuti muchite musanalembe mawu a cholinga cha utumiki wanu.

Mukamalemba mwachidule kawuniwuni wa malo ozungulira zidzakuthandizani kumvetsetsa anthu amene mukuwatumikira, moyo wawo wauzimu, zofuna zawo, maganizidwe awo, chikhalidwe ndi malo amene akukhala. Ndi chidziwitso chimenechi mutha kufalitsa bwino Uthenga Wabwino.

Cholinga ndi madongosolo sizikuyenera kupangidwa pa chifukwa chakuti ndi maganizo abwino kapena zochitika zabwino chabe. Zikuyenera kukhudzana ndi zofunika pa moyo

wauzimu, monga cholinga cha Mulungu chimagwirizana ndizofunika ku dziko lauchimo. Mawutumiki ambiri amalephera ngakhale amakhala ndi ndondomeko zabwino, koma zosagwirizana ndi malo amene akutumikira.

Ndibwinonso kupanga kawuniwuni chifukwa mukukhala mudziko limene likusinthana ngati mukufuna kukhala ndi mayankho pa mavuto auzimu koma mukuyenera kumvetsetsa malo amene mukutumikira.

Chabwino kwambiri, ndichakuti ubwino wa kawuniwuni ndiwakuti umawonetsa mphamvu zoipa za uzimu zimene zimagwira ntchito pakati pa anthu m'dera lanu. Mutha kupemphera, kumanga ndikuthana nazo mphamvu zoipa zimenezi.

Kawuniwuni wa malo amakhudzaso kuwunikira moyo wanu wa Uzimu, mphamvu zake kapena kufooka kwake. Utumiki uliwonse uli ndi zinthu komanso mphatso zimene zimapanga utumiki kukhala osiyana ndi ena. Anthu ndi mawutumiki ali ndi zofoka, zimene zimasokoneza kuthekera kokwaniritsa ntchito yawo.

Simaganizo olakwika kuganiza za zofooka zanu, kuchita kawuniwuni wanu nokha kumateteza kulephera. Ngati Israeli akanapemphera ndi kupanga kawuniwuni za zinthu ku Ai, sakanagonja. Mulungu akanaulula mavuto ndipo akanathana nawo asanapite kukamenya nkondo ndi adani: (Onani Yoswa 7).

Koma simumapambana mukaima kwambiri pa zofooka zanu. Mumapambana poima kwambiri pa zimene mumachita bwino ndikuzigwiritsa ntchito ku ulemelero wa Ambuye. Muzindikirenso kuti zofooka zanu zimapereka mpata kuti mphamvu ya Mulungu iwonetsedwe.

Mukamachita kawuniwuni wa zofooka zanu, ganizirani izi:

Kwa wina cikulupiro, mwa Mzimu yemweyo; ndi kwa wina mphatso za machitritso, mwa Mzimu mmodziyo (1 Akolinto 12:9)

Mukamapanga kawuniwuni wa zimene mumachita bwino, ganizirani zi:

Pakuti ndi chisomo chapatsidwa kwa ine, ndiuza munthu aliyense wa inu, kuti asadziyese koposa kumene ayenera kudziyese; koma aganize modziletsa yekha, monga Mulungu anagawira kwa munthu ali yense muyeso wa chikhulupiro. (Aroma 12:3)

WERENGANI MALEMBA AMENE ALI NDI MAWU A CHOLINGA:

Mawu a cholinga akuyenera kukhala a m'Baibulo. Izi zikutanthawuza kuti zikuyenera kugwirizana ndi cholinga chachikulu cha Mulungu chimene chinakambidwa m'chaputala chachiwiri.

Ndime zina za M'baibulo zimene mukuyenera kuziwonanso mukamphunzira za cholinga. Mukamawerenga ndime zimenezi, lembani mawu ndi maganizo amene akuthandizeni kulemba Mawu anu a Cholinga.

- Yesaya 1:1-20

- Mateyu 7:33; 9:37-38; 10:7-8,38-39; 16:24-25; 28:18-20

- Marko 1:17; 8:34-35; 11:25-26; 16:15-18
- Luka 4:16-19; 5:10; 9:2; 10:2-9; 12:29; 14:26-27; 22:29; 24:46-49
- Yohane 2:21; 4:35; 6:27; 15:16; 20:21-22
- Machitidwe 1:1-14; 2:42-47; 12:5,12; 14:27
- Aroma 10:13-15
- I Akorinto 13
- 2 Akorinto 4:3-4
- Aefeso 1:21; 2:1-9, 19-22; 4:14-16; 5:25
- Akolose 1:2, 18; 4:5-6; 3:12-16
- 1 Atesalonika 2:12
- I Timoteo 6:17-19
- Tito 2:14; 3:1, 8, 14
- Ahebri 9:12; 10:25
- Yakobo 1:17-27
- 1 Petro 2:1-12

LEMBANI MAWU A CHOLINGA

Ngati mwatsatira ndondomeko za pemphero, kawuniwuni wa mdela lanu, kuwerenga cholinga chachikulu cha Mulungu monga mwa mawu a Mulungu, muli okozeka kulemba mawu anu a cholinga.

Malizani chiganizo ichi:

Cholinga cha utumiki wanga ndi:

Ndi ndime iti imene munawerenga pamene mawu cholinga chanu ayimapo? Lembani m'musimu ndimeyo:

Tsopano lembani Mawu a Cholinga cha utumiki umene inu mumatumikirako (Tchalitchi, bungwe la uzimu, chipembedzo kapena kufalitsa ndi zina)

“Cholinga cha utumiki ndi”

__ Ndimawu ati amene munawerenga amene Mawu a Cholinga cha Utumiki wanu ayimapo:

PANGANI KAWUNIWUNI WA MAWU A CHOLINGA:

Pangani kawuniwuni wa chiganizo chimene mwalembe:

1. Kodi chikugwirizana ndi cholinga chachikulu? Chikugwirizana ndi Baibulo? Kodi munapeza malemba amene Mau anu ayimapo?
2. Kodi Mawu a Cholinga alembedwa momveka bwino kuti akumveka bwino?
3. Kodi Mawu a Cholinga chanu akugwirizana ndi dela limene inu mukutumikirako? Kodi abweretsa mayankho pa zosoweka?
4. Kodi akunena chifukwa chimene utumiki ulipo osati kufotokoza zochitika, zimene mumachita kapena mafikiridwe?
5. Kodi ikupereka mwayi wawukulu kwa mawutumiki amtsogolo? Ngati iyayi ndekuti mwayi ndiwochepa. M'musimu muli chitsanzo chimodzi cha chiganizo chimene chiri ndi mwayi ochepa:

“Cholinga cha Harvest International Network ndi kuphunzitsa anthu wamba okwanira 100 kukhala atsogoleri a Chikhristu”

Tikaphuzitsa atsogoleri 100 cholinga chathu chakwaniritsidwa. Tilibenso masophenya kwa mawutumiki akubwera kutsogolo. Tafupikitsa cholinga chathu ndipo ndi chaching'ono.

6. Kodi chanenedwa mwachindunji? Ngati iyayi kudzakhala kovuta kuti mudziwe ngati mukukwaniritsa cholinga chanu.

Chitsanzo cha Mawu a Cholinga amene sananenedwe mwachindunji ndi awa:

“Cholinga cha Harvestime International Network ndi kuphunzitsa Akhristu wamba”
Ndikovuta kupanga kawuniwuni kuti ziwoneke ngati utumiki ukukwaniritsa cholinga chake chifukwa cha kuti sanalembedwe mwachindunji. Kuwaphuzitsa chani? Ndi cholinga chani? Nanga maphunziro atsindika mbali iti?

Tsopano tiwone gawo la “Kudziwa Zambiri” ndipo tiwerenge Mawu a cholinga a Harvestime International Network amene anatengedwa. Analembedwa mwa chindunji ndipo siapafupi. Chifukwa analembedwa mwatsatanetsatane ndikosavuta kupanga kawuniwuni kuti ziwoneke ngati cholinga chikukwaniritsidwa. Ngati Mawu a cholinga chanu ali osamveka bwino, osaima pa malemba, osatsindika pa zosowa, ndi afupi mukuyenera kuwalembanso.

MGWIRIZANO PA CHOLINGA

Motsogozedwa ndi Mulungu, atsogoleri ayenera kukhazikitsa cholinga cha utumiki wonse, tchalitchi, kapena bungwe. Magawo onse amutumiki ayenera kuwuzidwa za cholinga chimenechi. Munthu aliyese m'magawo awutumiki, ayenera kumvetsetsa cholingachi.

Anthu onse okhulupirira ayenera kuwuzidwa cholingachi. Munthu aliyese ayenera kudziwa cholinga kuti pakhale mgwirizano pokwaniritsa cholingachi. Ngati onse akudziwa cholinga, aliyese atha kuchitapo kanthu pogwiritsa ntchito madongosolo kuti cholinga chikwaniritsidwe.

Mogwirizana anthu amagwira ntchito pamodzi kuti akwaniritse mbali yawo m'cholinga ndi madongosolo a Mulungu.

Masophenya amene afalitsidwa bwino ndiofunika kwambiri pobweretsa anthu pamodzi komaso chuma zokwaniritsira ntchito ya Ambuye. Izi ndi njira zimene mungazigwiritse ntchito pa chiyanjano chonse cha okhulupirira:

1. Lembani mawu a cholinga ndipo gawani kwa wina aliyense tsamba lake.
2. Phunzitsani kapena lalikirani kosachepera kamodzi pa chaka.
3. Kambiranani za cholinga m'misonkhano kapena pamene mukupanga madongosolo.
4. Khalani otsimikizika kuti atsogoleri onse mutumiki akuwonanso cholinga pafupipafupi.

Izi zimapanga kuti masomphenya akhalebe atsopano m'maganizo awo.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osaonera.
2. Kodi Mau a Cholinga ndi chiyani?
3. Mau a cholinga ndi ofunika bwanji?
4. Kodi cholinga ndi chokhumba zimasiyana bwanji?
5. Kusiyana kwa Mau a cholinga ndi Mau a C hiphunzitso ndi kuti?
6. Lembani njira zitatu zimene cholinga chikhoza kufalitsidwira mu chiyanjano chonse cha abale.
7. Ngati mbali imodzi ya kuphunzira phunziroli, munalemba mawu a cholinga utumiki wanu ngati munthu? Munalemba mau a cholinga cha tchalitchi kapena bungwe la chikhristu limene inu muli mbali imodzi?

(Mayankho a mafusowa anaperekedwa kumapeto kwa chaputala m’bukuli)

KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

1. Ngati utumiki wanu uli kale ndi Mau a Cholinga, pangani kawuniwuni poyankha mafunso awa:

- Kodi Mawu a Cholinga alembedwa momveka bwino kuti atha kumvetsetseka mosavuta?
- Kodi analembedwa liti?
- Kodi mawu a Cholinga akuwonetsa chithunzithunzi chimene utumiki wanu ukupanga panopa?
- Kodi chikugwirizana ndi mau a Mulungu?
- Kodi utumiki wapambana bwanji pokwaniritsa?
- Kodi utumiki walephera bwanji pokwaniritsa?
- Kodi walemphera bwanji kukwaniritsa cholinga?
- Walephera chifukwa chani? Chikhoza kuchitika ndi chani kuti zolakwika zikonzedwe?
- Kodi munafotokozera momveka bwino pa chiyanjano cha okhululipilira?

Kuti muwone zimenezi ganizirani mafuso awa:

- Kodi atsogoleri anu aphunzira za cholingachi zaka ziwiri zapitazi?
- Kodi uthenga walakikidwapo zaka ziwiri zapitazo?
- Kodi Mau a Cholinga alembedwa ndipo mwagawa masamba ake kwa okhulupirira?
- Funsani anthu angapo mgulu lanu kuti akuwuzeni Mau a Cholinga cha utumiki wanu?

Kodi atha kukwanitsa kupanga izi?

- Ngati utumiki wanu uli ndi madongosolo, zochitika, kapena bajeti, kodi zikugwirizana ndi Mau a cholinga? Kodi Mau a cholinga akufanana ndi dela limene mukutumikira? Kodi zikwanitsa kupereka zofunika za kuuzimu?
- Kodi zikufotokozza chifukwa chani utumiki ulipo osati kungofotokozza za zochitika?
- Kodi ikupereka mwayi waukulu ku mautumiki amtsogolo, kapena mwayi ndi wochepea?
- Kodi anenedwa mwa chindunji? Ngati ayi, simungadziwe ngati mukupambana?
- Kodi cholinga chikuyenera kulembedwanso? Ngati ndi choncho tsatilani ndondomeko zimene zapatsidwa m'gawo lakumapeto kwa phuziroli lotchedwa “(Kupanga Mau a Cholinga)”

2. Machitidwe 13:35 ikuwonetsa kuti mfumu davide anatumikira cholinga cha Mulungu mthawi ya moyo wake wawutumiki. Werengai za moyo wa Davide pa 1 ndi 2 Samueli ndikuyankha mafuso awa:

- Kodi Davide anazindikira bwanji cholinga chake?
- Kodi anapanga chani kuti akwaniritse cholinga?
- Ngati Davide akanalemba Mau a Cholinga kodi akanakhala otani?
- Davide akanalemba ndondomeko yokwaniritsira cholinga chake, kodi ikanakhala yotani?

3. Apa pali Mau a Cholinga a Harvestime International Network:

HARVESTIME INTERNATIONAL NETWORK
MAU A CHOLINGA

Yesu anayika chidwi chake pa Ophunzira chifukwa cha m'mene malo akholola aliri:
(Yohane 4:35)

Ntchito imene inapatsidwa ndi Ambuye ndi ya ogwira ntchito, amuna komanso akazi amene akudziwa kukolola kholola la uzimu m'dziko lapasi kupititsa patsogolo ufumu wa Mulungu. Ndi chifukwa cha cholinga ichi, a Harvestime Internantional Network ndiyodzipereka, kupeza anthu, kuwaphuzitsa, ndikuwabweretsa pamodzi anthu okolola amene adzakwanitsa ku:

1. Kupempherera kholola pa dziko lonse lapansi.
..... (Mateyu 9:37-38)
2. Kufotokoza bwino mfundo za kholola la uzimu:
(2 Timoteo 2:2)
3. Kuwonetsa mfundo za kholola la uzimu:
(1 Akolinto 2:4-5)
4. Kufotokozera bwino kuti kholola la uzimu likuyenera kuchitika mwachangu.
(Yeremiya 8:20)
5. Kumema anthu m'thupi la Khristu kukolola mbali yawo mukholola limene likuchitika masiku ano otsiriza:
(Yeremiya 5:24)

CHAPUTALA 4

KUKONZA DONGOSOLO

ZOLINGA

Mukamaliza chaputala chino muzikwanitsa kuchita izi:

- Kutanthauzira mau oti “cholinga.”
- Kufotokozera kusiyana kwa mau oti cholinga ndi
- Kudziwa mitundu iwiri ya objectives
- Kudziwa kusiyana kwa pakati pa zolinga za
- Kufotokozera momwe mungasankhire objectives
- Kulemba objectives za utumiki
- Kuunika objective zomwe mwalemba

VESI LOTSOGOLERA

Ndipo kapolo uyo, wodziwa chifuniro cha mbuye wache, ndipo sanakonza, ndi kusachita zonga za chifuniro chachecho, adzakwaplidwa mikwapulo yambiri. (Luke 12:47)

MAU OYAMBA

M’maphunziro awiri apitawo mwaphunzira za kufunika kwa cholinga mu utumiki. Koma mutha kumangolankhula za cholinga ndi masomphenya mpaka kalekale osawakwaniritsa. Kudziwa cholinga cha Mulungu pa utumiki wanu kokha sikokwanira, mukuyenera kudzikonzekeretsa nokha kuti muwakwaniritse.

Mu chaputala chino muphunzira momwe mungapangire dongosolo. Chaputala 5 chikufotokozera za momwe mungakwaniritsire mapulani anu ndipo Chaputala 6 chikufotokozera momwe mungathe kuunikira mapulani anu.

ZOKHUMBA

“Chokhumba” ndi chotsatira chomaliza chomwe munthu amafuna kuchiona kumapeto a ntchito yomwe wakonza. Munthu akakhazikitsa “zokhumba” za utumiki amakhala panso nakonza dongosolo la momwe angakwaniritsire zolinga za Mulungu. Amakonza dongosololi akudziwa kapena ayi. Tsiku ndi tsiku mumagwira ntchito ina yake. Ili limakhala dongosolo lanu pa tsiku limenelo, kaya mwakonza dala kapena zikungochitika.

Kukonza dongosolo mokhazikitsa zokhumba ndi njira yochitira zomwe munthu amachita tsiku ndi tsiku koma moyenera. Zimathandizira kuti munthu azichita zinthu zokhazo zomwe zikugwirizana ndi zolinga za utumiki wake. Kukonza dongosolo ndi njira imodzi yomvera Mulungu ndi kukwaniritsa zolinga zake pa moyo ndi utumiki wanu.

Zokhumba si malamulo osasinthika ayi koma zomwe munthu umaika kuti zikutsogolere pa tsogolo la utumiki. Sizipanga tsogolo la utumiki koma ndi njira yoikira m’ malo anthu a Mulungu kuti agwire ntchito ya Mulungu. Pali kusiyana pakati pa zolinga ndi zokhumba. Mwaphunzira kale kuti zolinga ndi masomphenya auzimu. Kudziwa cholinga chako chenicheni mu utumiki – mbali yanu mu dongosolo la Mulungu.

Zokhumba ndi masitepe amene munthu amatenga kuti akakwaniritse zolinga zomwe Mulungu wampatsa. Ndi madongosolo okwaniritsira cholinga. Zolinga ndi masomphenya sizikwaniriitsidwa chifukwa chakuti zilipo. Mukuyenera kuchitapo kanthu kuti zitheke. Cholinga chimakupatsani mphamvu, koma zokhumba zimakukankhani kuti mupite chitsogolo kukwaniritsa masomphenya. Cholinga chiri ngati chikhulupiriro. Pamene zokhumba ziri ngati ntchito. Cholinga chopanda dongosolo chimakhala chopanda tanthauzo chimodzimodzi chikhulupiriro chopanda ntchito chimakhala chakufa. Cholinga chanu m'dongosolo la Mulungu ndi chachikulu kotero kuti chitha kukutengerani moyo wanu wonse kuti mukachikwaniritse. Madongosolo ndi masitepe ang'onoang'ono okutengerani kukukwaniritsa masomphenya omwe Mulungu wakupatsani. Onani dongosolo liri m'musili:

Zokhumba

Cholinga chapadera chimodzi

Cholinga chachikhulu cha Mulungu

Kufikira Dziko lonse.

Onani mosamalitsa chojambulachi. Chikuonetsera momwe zokhumba zimakhuthandizirani kuti mukwaniritse cholinga chanu chomwe chiri mbali imodzi ya cholinga cha Mulungu. Mbali iri yonse ya Thupi la Khristu imakwaniritsa cholinga chake chapaderadera, kenako cholinga chachikulu cha Mulungu chofikira dziko lonse ndi Uthenga chidzakwaniritsidwa.

ZOKHUMBA ZA PAULO

Tiyeni tione “mau a cholinga” a Paulo omwe mwaphunzira mu Chaputala 3. Iye anati:

“Cholinga changa mu utumiki ndicho kutenga dzina la Ambuye Yesu Khristu ku:

Amitundu (mitundu ina osati Israel)

Mafumu (atsogoleri)

Fuko la Israel” (Machitidwe 9:15)

Zokhumba zomwe Mulungu anapereka kwa Paulo kuti akakwaniritse cholinga chake:

“Ndidzatumikira ndi kuchitira umboni kuti:

- a. Ndikatsegule maso awo.
- b. Ndikawatembenuze kuchoka ku mdima kunka kukuunika.
- c. Ndikawatembenuze kuchoka kwa Satana kunka kwa Mulungu.
- d. Ndikawatsogolere kukukhululukidwa kwa machimo.
- e. Ndikawatsogolere m'cholowa chawo chazimu... (Onani Machitidwe 26:15-16)

MITUNDU YA ZOKHUMBA

Pali mitundu iwiri ya zokhumba:

Zokhumba za munthu payekha: Awa ndiwo madongosolo omwe munthu amakonza kuti akakwaniritse cholinga chake mu utumiki.

Zokhumba za gulu: Awa ndi madongosolo omwe munthu mumakonza pamodzi ndi anthu ena okhuthandizani kukwaniritsa cholinga cha gulu, mpingo, kapena bungwe.

MFUNDO YA CHIKHULUPIRIRO

Popeza kuti zokhumba ndi zomwe mukufuna mutachita mtsogolo, izo ndi mfundo za chikhulupiriro zopangidwa molingana ndi chifuniro cha Mulungu:

Koma chikhulupiriro ndicho chikhazikitso cha zinthu zoyembekezereka, chiyesero cha zinthu zosapenyeka. (Ahebri 11:1)

Simukuyenera kupanga madongosolo odzikonda inu nokha. Amakhala madongosolo ofuna kukwaniritsa cholinga cha Mulungu. Mumakhala omasuka nthawi zonse ku chitsogozo chake.

Inu amene simudziwa chimene chidzagwa mawa. Moyo wanu uli wotani? Pakuti muli utsi wakuonekera kanthawi, ndi pamenepo ukanganuka. Mukadanena inu akalola Mulungu, ndipo tikakhala ndi moyo, udzachita kakuti kakuti (**Yakobo 4:14-15**)

Popeza kuti zokhumba ndi mfundo za chikhulupiriro, zimafunika kulimba mtima. Mukuyenera kuima m'chikhulupiriro ndi kuyamba kugwira ntchito. Chifukwa chakuti Mulungu amadziwa za mtsogolo, atha kukupatsani nzeru pamene mukupanga madongosolo amenewa.

KUFUNIKA KWA ZOKHUMBA

Zokhumba zimakulolani kuti mukwaniritse zolinga za Mulungu zapaderadera za utumiki wanu. Cholinga chachikulu chokhalira ndi zokhumba ndicho kukuthandizani kuchita zomwe zikuyenera kuchitika pokwaniritsa cholinga chanu. Madongosolo amakulolani kuti muzichita zinthu molingana ndi zolinga osati kumangodzidzimukira zinthu.

Zokhumba zimapereka chitsogozo. Popeza kuti zokhumba zimapangitsa kuti zochitika zidziwika, aliyense amadziwa dongosolo lomwe liripo. Chisokonezo chimachoka. Chitsogozo sichikhalapo ngati munthu sadziwa komwe akupita. Zokhumba zimapereka chidziwitso cha komwe mukupita. Munthu akamakonzza madongosolo amtsogolo, amatha kudziwa mavuto omwe angapezeke ndikupezeratu njira zothanirana ndi mavutowo akachitika. Mumatha kumenya nkondo yopalamula osati yongodziteza.

Kukonzza dongosolo kumathandiza anthu kuti apeze malo awo mu utumiki wa Thupi la Khristu. Chifukwa chakuti zokhumba zimadziwitsa zochitika ndi anthu omwe achite, aliyense amadziwa chomwe akuyenera kuchita. Mutha kusonkhanitsa gulu lonse la okhulupirira kuchita cholinga chimodzi ndi madongosolo amodzi.

Zokhumba zimathandizira kuunikira zochitika mu utumiki. Mutha kuunika madongosolo anu ndi kuona ngati akukwaniritsa cholinga cha Mulungu mu utumiki wanu. Muphunzira zambiri za izi mu Chaputala 6. Zokhumba zimakuteteza kuti musachoke pa masomphenya a utumiki. Popanda zokhumba mutha kukhala moyo wanu wonse popanda chochitika cha nzeru ndipo mudzati, "Sindinakwaniritse cholinga cha Mulungu." Mwapatuka popanda madongosolo ndi chilinganizo, popanda kauniuni wa utumiki, kenako mwalephera.

Kukonzza madongosolo kumakuthandizani kudziwa zolinga kapena zifukwa zomwe mukuchitira zomwe mukuchitazo. Muzidzaunikaunika zokhumba ndi zifukwa zochitira utumiki m'gawo liri lonse la utumiki wanu. Mudzayamba kudzifunsa kuti, "Kodi zokhumba zanga pokhala ndi zokambirana izi ndi zotani?" "Kodi zokhumba zanga pophunzitsa phunziro ili ndi zotani?" "Kodi zokhumba zanga popereka uphungu kwa munthu uyu kapena

kulemba kalata uyu ndi zotani?” Mudzayamba kuunika chochitika chiri chonse chomwe mukuchita molingana ndi cholinga cha utumiki wanu.

KUSANKHA ZOKHUMBA

Zokhumba zimabadwa kudzera m’pemphero, chitsogozo cha Mzimu Woyera, kusanthula Mau a Mulungu, komanso kuzindikira cholinga chanu cha paderadera mu dongosolo lake la Mulungu. Kukonza madongosolo kusatenge malo a pemphero kapena kusanthula Mau m’moyo wanu. Koma kuti zokhumba zanu zanu zichokere m’pemphero ndi nkusanthula Mau. Ndipo kukonza madongosolo kukuyeneranso kugwirizana ndi cholinga chomwe chiripo.

Mwaphunzira kale momwe “Kauniuni wa Zozungulira Utumiki Wanu” amabvumbulutsira zosowa zauzimu za anthu ndi dera lomwe mukutumikira. Mwaphunzira momwe cholinga cha utumiki chimayenera kugwirizanira ndi zosowazi komanso cholinga cha Mulungu.

Pemphero, kusanthula Mau, ndi kudziwa cholinga ndi zofunika kwambiri pokonza dongosolo kapena pulani ya utumiki. Popanda izi, mukonza madongosolo anu ndi nzeru za umunthu. Musaiwale kuti njira zanu si njira za Mulungu:

Pakuti maganizo anga Sali maganizo anu, ngakhale njira zanu siziri njira zanga, ati Yehova. Pakuti monga kumwamaba kuli kutari ndi dziko lapasi, momwemo njira zanga ziri zazitari kupambana njira zanu, ndi maganizo anga kuapambana maganizo anu. Yesapya (55:8-9)

Vuto la lalikuru la madongosolo a mwini chuma wa pa Luka 12:16-20 ndi lakuti, “anaganiza mwa iye yekha.” Anapanga madongosolo popanda chitsogozo cha Mulungu. Mulungu amadziwa kale mapulani omwe ali nawo pa inu. Udindo wanu ndiwo kumvetisa ndi kuchita molingana ndi madongosolo akewo:

Pakuti ndidziwa malingiriro amene ndilingiririra inu, ati yehova, malingiririo a mtendere, si a choipa, akukupatsani inu adzukululu ndi chiyembekezero. (Yeremiya 29:11)

Popeza kuti mwasankha zokhumba, kukonza dongosolo kumafunika kupanga ziganizo. Mumapanga chisankho chochita zinthu zina ndi kusachita zinthu zina. Muika zinthu zofunikira kwambiri m’ malo. Kusanthula Luka 12:16:20 mu gawo la “Kupitiriza Kuphunzira” kukufotokozera bwino kufunika koika zinthu zofunikira kwambiri zomwense ndi zoyenera.

Mutha kuonanso mfundo za kupanga ziganizo molingana ndi Mau a Mulungu zomwe zaperekedwa mu maphunziro a Harvestime International Institute otchedwa, “Mfundo za Kupanga Ziganizo Molingana ndi Mau” ndi “Kudziwa Liu la Mulungu.” Izi zikuthandizani popanga ziganizo pamene mukukonza madongosolo.

KUIKA ZOKHUMBA

Mfundo ziri m’musizi zikuthandizani pamene mukuika zokhumba za utumiki m’ malo mwake:

LEMBANI ZOKHUMBA ZANU:

Pakuti Yehova abwezeranso akulu wache wa Yakobo ngati ukulu wache wa Istraiei; pakuti okhuthula awakhuthula, naipsa nthambi zache za mpesa. (Habakuku 2:2)

Mukalemba zokhumba, mumatha kukumbukira mosavuta, kukwaniritsa komanso kuunika mapulani anu. Izi ndi zomwe Davide anachita pamene anakonza dongosolo la kachisi mothandizidwa ndi Mulungu. Iye anati:

Pakuti Yehova anachepetsa Yuda chifukwa cha Ahazi mfumu ya Israeli; popeza iye anachita chomasuka pakati pa Yuda, nalakwira Yehoba kwambiri. (2 Mbiri 28:19)

ZOKHUMBA ZIKUYENERA KUGWIRIZANA NDI CHOLINGA

Ili ndi gawo lofunikira kwambiri la kukonza madongosolo. Mukapanga madongosolo omwe sakugwirizana ndi cholinga cha utumiki wanu, mukhala mukuchita ntchito yabwino inde, koma osati yomwe Mulungu anakonza kuti muchite. Ngati zokhumba zanu zonse zikugwirizana ndi cholinga chanu, ndiye kuti zonse zigwirizana pamodzi mu dongosolo lalikuru la utumiki. Dongosolo liri lonse lomwe mungapange likhala logwirizana ndi cholinga chanu.

Ngati cholinga chanu chikugwirizana ndi cholinga cha Mulungu, ndi madongosolo omwe mukupanga akugwirizana ndi cholinga chanu, ndiye kuti zokhumba zanu zikhala zogwirizana ndi Mau a Mulungu.

ZOKHUMBA ZIKUYENERA KUKHALA ZOMVEKA BWINO

Ngati zokhumba sizinalembedwe momveka bwino, palibe yemwe adzazimvetse. Lembani chokhumba chanu chiri chonse momveka bwino. Khalani ndi chofuna kukwaniritsa chimodzi pa chokhumba chiri chonse. Pangani dongosolo lanu kukhala lomveka mosavuta. Kumbukirani Habakuku 2:2 akuonetsa kuti masomphenya omveka bwino okha omwe amapatsa anthu mphamvu zakuchita.

ZOKHUMBA ZIZIKHALA CHIKATIKATI.

Madongosolo amayenera azikhala chikatikati cha chikhulupiriro ndi zinthu zotheka. Ngati angaonjeze kukhala owoneka osatheka, madongosolo anu sakwaniritsidwa. Komanso, musayang'anire panso zomwe muli nazo, kuganiza kwanu, anthu anu ndi chuma chanu. Pangani mapulani opanda malire a chikhulupiriro. Kumbukirani...

Yesu anawayang'ana iwo nati, Sikutheka ndi anthu, koma kutheka ndi Mulungu; pakuti zinthu zose zitheka ndi Mulungu. (Marko 10:27).

ZOKHUMBA ZIZIKHALA ZOLUNJIKA

Madongosolo akuyenera kukhala olunjika. Izi zikutanthauza kuti akuyenera kuyankha mafunso ali m'musiwa:

- Kodi tichita chiyani? Lembani chenicheni chomwe muchite.
- Kodi tichita motani? Lembani ndondomeko ndi njira zomwe mugwiritse ntchito pokwaniritsa dongosolo lanu.

- Kodi tichiti liti? Ikani nthawi yoyambira, yomalizira, ndi yokhala pansu ndi kuunika ngati mwakwaniritsa zomwe munakonza.
- Kodi achite ndi ndani? Onani anthu omwe agwire ntchitoyo komanso chiwerengero chawo. Onaninso omwe ali ndi mphatso ya Mzimu wochitira chinthu chimenecho. Onaninso momwe anthu angagwilire ntchito limodzi.
- Kodi zifunike ndi zotani? Onani kuti pafunika ndalama zochuruka motani kuti mukwaniritse dongosolo lanu.

Mukakonza bajeti ya ndalama za utumiki mogwirizana ndi zokhumba zomwe ziripo, ndipo kuti zokhumbazo zikugwirizana ndi cholinga chanu, ndiye kuti mukhala mukugwiritsa ntchito ndalama za utumiki kukwaniritsa cholinga chanu. Ngati simutero, simungathe kugwiritsa ntchito ndalama moyenera.

Phunziro la Harvestime International Institute lotchedwa “Mfundo za Kayendetsedwe Bwino ka Zinthu Molingana ndi Mau a Mulungu” limapereka mfundo zachuma za Baibulo zomwe zingakuthandizeni kugwiritsa bwino ntchito ndalama za utumiki. Chitsanzo cha bajeti chaperekedwa kumapeto kwa bukhu lino.

ZOKHUMBA ZIKHALE ZOTHA KUYESEDWA

Zokhumba zikuyenera kulembedwa kuti nthawi ina mutha kuunikira ngati zikukwaniritsidwa kapena ayi. Muphunzira zambiri za kuunikira dongosolo mu Chaputala 6.

Chokhumba chimaonetsera kwenikweni chimene mukufuna mutaona kumapeto kwa chochitika chanu. Kotero kumakhala kosavuta kudziwa ngati zokhumba zanu zakwaniritsidwa kapena ayi. Simungayese zotsatira za utumiki popanda zinthu zomwe munazikhazikitsa pachiyambi pomwe zokuthandizani kudziwa ngati mukuchita bwino kapena ayi.

ZOKHUMBA ZIKHAZIKITSIDWE MOLINGANA NDI KUFUNIKA KWAKE

Mukamaika zokhumba m'malo zokhumba za utumiki, nkofunika kuzisanja molingana ndi kufunika kwake kwa zokhumbazo. Kodi ndi dongosolo liti lomwe mukufuna kuti mukwaniritse poyamba. Nanga ndi zokhumba ziti zomwe mukufuna zitakwaniritsidwa koyamba musanakwaniritse zinazo? Mwachitsanzo, nkofunika kulalikira pamudzi kaye musanabvale mpingo pamudzipo.

IKANI ZOKHUMBA ZAPAFUPI KOMANSO ZAPATALI

Kukonza dongosolo kumatenga nthawi. Chifukwa cha ichi, mukuyenera kuika zinthu m'malo mudakali patali ndithu. Kukonza dongosolo kumakhuzana ndi zinthu za mtsogolo. Pali mitundu iwiri ya tsogolo:

Tsogolo la posachedwapa: masiku, masabata kapena miyezi ingapo ikubwerayi ndi tsogolo la pafupi. Mukhale ndi madongosolo a nthawi yapafupi ngati imeneyi. Izi ndi zomwe mukhale mukuchita panopa.

Tsogolo la patali: Chaka chamawa kapena zaka zingapo zotsatirazo. Mukhale ndi madongosolo a patali a tsogolo lapatalinso. Awa ndi madongosolo am'tsogolo omwe mukhale mukuwapemphelera kuyambira tsopano. Mudzayamba kukwaniritsa madongosolowo nthawi inayake mtsogolo muno.

Kuti muchite bwino pa utumiki, mukuyenera kukhala ndi madongosolo a pafupi komanso amtsogolo. Mukatero, mukhala mukudziwa chochita lero komanso zeni zeni zomwe mukhale mukuchita patsogolopa. Baibulo limatiphunzitsa kuti “tikhale ochitachita kufikira Iye atabwera.” Kutanthauza kuti tikhale ndi madongosolo oti tiziwakwaniritsa okhuza Ufumu wa Mulungu, apafupi ngakhale apatali kufikira Ambuye Yesu atadza natitenga kunka kumwamba.

KUKONZA DONGOSOLO NDI NTCHITO YAPANG’ONO PANG’ONO.

Madongosolo akhale omasuka ndi osavuta kuwasintha. Iyi ndi ntchito yochita motsogozedwa ndi Mzimu Woyera kotero mukuyenera kukhala omasuka kuti Mzimu atha kukutsogolerani mwatsopano. Mtumwi Paulo anakonza dongosolo lopita ku Asiya nthawi inayake, koma Mzimu Woyera anamubvumbulutsira kuti imeneyo sinali nthawi yoyenera. Paulo anasintha dongosolo lake ndipo anapita nthawi ina (Machitidwe 16:6).

Mutatha kukonza dongosolo, zinthu zina zitha kuoneka kuti zikusintha pa moyo kapena utumiki wanu. Mwina mutha kukhala ndi dongosolo labwino latsopano. Nthawi zina mavuto atha kukupangitsani kuganiza zosintha dongosolo lanu. Izi ndi zina mwa zifukwa zomwe dongosolo lanu likuyenera kukhala lomasuka. Mukuyenera kukhala wokonzeka kusintha dongosolo la kachitidwe ka zinthu molingana ndi nyengo komanso momwe Mulungu angakutsogolerani. Mukuyenera kukonzanso zokhumba zanu ndi kuika zina chifukwa:

- a. Zochitika pamalo omwe mukutumikira zitha kusintha ndipo mudzafunika kuti nanunso musinthe madongosolo anu. Mwachitsanzo, ngati gulu lalikuru la anthu othawa kwao litabwera ku dera lanu mukuyenera kusintha madongosolo anu kuti mukhalenso ndi utumiki wofikira anthuwa.
- b. Mukhala mukukwaniritsa madongosolo anu ndipo muzidzafunika kukonza ena. Mwachitsanzo, mutha kufikira chokhumba chofuna kubvala mpingo pa mudzi. Ndiyeno muchita chiyani?
- c. Mzimu Woyera atha kukutsogolerani kusintha madongosolo.
- d. Mutha kuzindikira kuti madongosolo omwe munapanga sakukwaniritsa cholinga cha Mulungu m’ moyo kapena mu utumiki wanu. Mukuyenera kuwasintha.

CHITSANZO CHA ZOKHUMBA

M’chigawo cha “Kupiriza Kuphunzira” cha phunziro lino muli zitsanzo zina za zokhumba zoti musanthule. Muli zitsanzo zoyenera komanso zosayenera. Pitani tsopano pa tsamba limeneli mukasanthuliretu zitsanzozzi musanapitirize phunziro lino. Zikuthandizani kumvetsa bwino zomwe mwaphunzira kufikira tsopano.

KULEMBA ZOKHUMBA ZANU NGATI MUNTHU

1. Pitani ku Chaputala 3 kuti mukaonenso Mfundo ya Cholinga ya utumiki wanu yomwe munalembe.
2. Lembani zokhumba zitatu zapafupi za utumiki wanu.
3. Lembani zokhumba zitatu zapatali za utumiki wanu.

KULEMBA ZOKHUMBA ZA UTUMIKI

1. Pitani ku Chaputala 3 kuti mukaonenso Mfundo ya Cholinga ya utumiki mpingo kapena bungwe lanu yomwe munalembe.

2. Lembani zokhumba zitatu zapafupi za utumiki wa gulu lomwe inu mukutumikira. Mutha kukumana ndi atsogoleri ena m'gulu lanulo kuti akuthandizeni kukonza zokhumba zimenezi.
3. Lembani zokhumba zapatali zitatu za utumiki wa gulu lomwe inu mukutumikira. Mutha kukumana ndi atsogoleri ena m'gulu lanulo kuti akuthandizeni kukonza zokhumba zimenezi. Gwiritsani ntchito fomu yomwe yaperekedwa m'gawo la "Kupitiriza Kuphunzira" la phunziro lino kuti mulembe zokhumba zanu.

KUUNIKIRA ZOKHUMBA

Unikirani zokhumba zomwe mwalemba pogwiritsa ntchito ndondondomeko yotsatirayi:

1. Kodi zokhumba zanu ndi zomveka bwino, ndi zosavuta kuzimvetsa?
2. Kodi chokhumba chiri chonse chiri ndi chinthu chimodzi chokha chofunika kufikiridwa?
3. Kodi chokhumba chiri chonse chiri ndi dongosolo lodziwika bwino lofunika kuchitika?
 - a. Motani? (zochitika ndi njira zokwaniritsira zokhumbazo)
 - b. Liti? (kuyamba, kumaliza ndi masiku owonera ngati zikuyenda bwino kapena ayi)
 - c. Ndi ndani?
 - d. Pafunika ndalama zotani?
4. Kodi chokhumba chirichonse ndi choyezeka? Mutha kuunikira zokhumba zanu bwino lomwe kuti mudziwe ngati mukukwaniritsa dongosolo lanu kapena ayi?
5. Kodi mwaika madongosolo apafupi komanso apatali?
6. Kodi zokhumba zanzu zikugwirizana ndi zolinga za utumiki wanu?
7. Kodi zokhumba zanu ngati munthu zikugwirizana ndi zokhumba za mpingo kapena bungwe lomwe inu mukutumikira?
8. Kodi muli okonzeka kulipira dipo la zomwe zifunike kuti mukwaniritse chokhumba chimenechi (ndalama, nthawi, kudzipereka nsembe).
9. Kodi mungathe kufunsa thandizo lochokera kwa Mulungu kuti mukwaniritse chokhumba chanu? Zitha kutero ngati zikugwirizana ndi cholinga chachikulu cha Mulungu komanso cholinga chapaderadera cha inu mu dongosolo lake.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osaonera.

2. Tanthauzirani mau oti “chokhumba.”

3. Kodi pali kusiyana kotani pakati pa cholinga ndi chokhumba?

4. Lembani mitundu iwiri ya zokhumba.

5. Chifukwa cha chiyani zokhumba ziri zofunika kwambiri?

6. Fotokozero kusiyana kwa pakati pa zokhumba zapafupi ndi zokhumba zapatali.

7. Kodi zokhumba timasankha motani?

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto a phunziro lino)

KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

1. Kusanthula chitsanzo cha zokhumba:

Mwachitsanzo, tiona dongosolo la mpingo waukulu mu mzinda wa Los Angeles, California ku America. Mpingowu umakhulupirira kuti cholinga chake ndi kufikira Los Angeles yense ndi Uthenga Wabwino.

Chitsanzo cha chokhumba chimene analemba koma chosayenera nachi:

“Tidzafikira mzinda wa Los Angeles ndi Uthenga Wabwino.”

Ichi si chokhumba choti angachiyese. Kodi angadziwe bwanji kuti akwaniritsa dongosolo lawo? Kodi amene adzagwire ntchito ndi ndani? Motani? Liti? Pafunika ndalama zingati? Adzayamba bwanji? Chokhumba ichi sicholunjika bwino popeza sichikufotokozerwa momveka bwino chomwe chikuyenera kuchitika.

Chitsanzo cha chokhumba chabwino ndi ichi:

“Tifikira anthu a chilankhulo cha ku Spain omwe akukhala makilomita asanu kuzungulira mpingo wathu.

Tidzayamba kukwaniritsa chokhumba ichi mu pa 1 January, 2000 ndipo tidzamaliza pa 31 Disembala chaka chomwecho. Tizidzakumana Lachitatu loyamba la mwezi uliwonse kukambirana za momwe zinthu zikuyendera.

Tidzadziwa kuti takwaniritsa cholingachi:

- a. Tikadzafikira banja liri lonse la anthu a chilankhulo cha ku Spain omwe akukhala makilomita asanu kuzungulira mpingo wathu ndi Uthenga Wabwino.
- b. Tikadzakhazikitsa mpingo womwe uli ndi mamembala osachepera 100 a chilankhulo cha ku Spain kuchokera mu utumiki umenewu.
- c. Tikadzaphunzitsa anthu omwe atembenuka mtimawo kuti nawonso apitirize kufikira anthu ena mderali.

Pali anthu amene agwire ntchito imeneyi:

A John Smith ndi amene adzatsogolere ntchito yonse pa utsogoleri wa abusa. Tidzagawa derali m’magawo awiri ndipo tidzasankha anthu awiri oyang’anira maderawa aliyense lakelake. Maderawo adzagawidwa kutengera momwe derali liliri.

Wapampando wa deralo adzafikira makomo omwe ali mderalo ndi Uthenga Wabwino. Adzalemba maina ndi ma adiresi a omwe atembenuka mtima kumene. Adzasiya kabuki kowerenga pa khomo liri lonse limene adzafikire. Aliyense amene adzalandire Yesu adzapatsidwa kabukhu ka Uthenga Wabwino wa Yohane. Adzawayendera onse amene atembenuka mtima ndi kuwalimbikitsa kuti akhale mbali imodzi ya mpingo. A John Smith adzaphunzitsa anthuwa ndi kusankha ena kuti akhale atsogoleri a mpingo watsopanowo. Zonse zikhatheka tidzakonzanso dongosolo lina lofikira dera lina la Los Angeles mpaka titafikira mzinda wonse.

Zomwe zifunike pa dongosololi ndi izi:

- a. Timabukhu ta Uthenga Wabwino K.....
- b. Timabukhu ta Uthenga Wabwino wa Yohane.
- c. Mapu omwe tidzagwiritse ntchito pogawa derali.
- d. Ma khadi olembapo maina ndi ma adiresi a anthu omwe atembenuka mtima.
- e. Kulengezetsa za kutsegula mpingo watsopano pa wayilesi.

- f. Kutumiza mauthenga oyitana anthu omwe atembenuka mtima ku mwambo wotsegula mpingo (mapemphero adzachitika m'nyumba kuti tisaononge ndalama kulipirira malo okumanapo).
- g. Zipangizo zophunzitsira anthu otembenukawo kukhala ophunzira a Khristu.

Izi zitithandiza kukwaniritsa cholinga chathu mu dongosolo la Mulungu lofikira Los Angeles ndi Uthenga Wabwino. Pofikira anthu a chilankhulo cha ku Spain omwe akukhala makilomita asanu kuzungulira mpingo wathu, tikukwaniritsa gawo limodzi la cholinga cha Mulungu pa mpingo wathu.

Dongosolo ili tiligwiritsa ntchito mobwereza bwereza mpaka titafikira mzinda wonse ndi Uthenga Wabwino.

- 2. Werengani Miyambo 1:2-6. Ndime iyi imafotokozera cholinga cha Bukhu la Miyambo. Chifukwa chimene bukhuli lidalembedwera. Kwina konseko ndi kufotokozera momwe cholinga cha bukhuli chingathe kukwaniritsidwira.
- 3. Zina mwa zomwe zokhumba zomwe anakonzera ana a Israel ali m'dziko la ukapolo wa ku Aigupto ndi izi:
 - a. Ndidzakuturutsani mu gori la ukapolo wa Aigupto.
 - b. Ndidzakupulumutsani m'manja mwa iwo akukuchitani ukapolo.
 - c. Ndidzakuombolani ndi mkono wotambasuka komanso ndi machitidwe aakuru.
 - d. Ndidzakutengani kukhala anthu anga.
 - e. Ndidzakhala Mulungu wanu.
 - f. Ndidzakulowetsani kuti dziko lomwe ndinalumbirira ndi mkono wokwezeka.
 - g. Ndidzakupatsa dzikolo likhale lanu.

Dongosolo la mtengo wapatali. Mose anafotokozera zonse pa maso anthu onse, koma Israel anakana kulandira dongosololo (Eksodo 6:9). Zimatheka kukhala ndi dongosolo la mtengo wapatali kuchokera kwa Mulungu koma nkumakumanabe ndi zotsutsa zambiri. Kumbukirani: Zolinga ndi madongoso a Mulungu salephereka. Mulungu anakwaniritsa zokhumba zake pa Israel, ngakhale zinamtengera kuti achite kudzutsa m'badwo wina.

- 4. Sankhani bungwe la Chikristu lomwe mukulidziwa. Kuchokera mu zomwe likuchita, mukuganiza kuti cholinga chawo ndi chotani? Nanga angakhale ndi zokhumba zotani?
- 5. Mukanadziwa kuti palibe chingakukanikeni ndi zokhumba zitatatu ziti zimene mukanakhazikitsa kuti muzikwaniritse? Mukazilemba, zipempherereni. Musamaopa kulephera. Mwina Mulungu akufunisitsa atakugwiritsani ntchito kuti mukakwaniritse zinthu zimenezi.
- 6. Kufunika koika zinthu zofunika kwambiri patsogolo pochita pogwira ntchito kwafotokozeredwa bwino mu fanizo la Munthu Mwini Chuma pa Luka 12:16-20. Munthu wachumayu:
 - a. Anadzikundikira chuma yekha osati anthu ena. Moyo wake ndi umene umaoneka kukhala wofunika kwambiri kuposa Ufumu wa Mulungu.
 - b. Anachita zonse kusamalira thupi lake koma osati moyo wake. Anaika zinthu za thupi patsogolo osati zauzimu.
 - c. Anachita zonse kusamalira wa padziko lapansi osati wakumwamba. Kodi zinthu zofunika kwambiri pa moyo wanu zimagwirizana ndi moyo wosatha? Kodi chinabvuta kwambiri pa munthu uyu chinali chiyani? Anaganizaganiza mwa

yekha (Luka 12:17). Sanakonze dongosolo lake molingana ndi cholinga cha Mulungu ndi zinthu zake zofunikira. Nthawi zonse mukaika zinthu zosafunika kwambiri patsogolo, zotsatira zake zimakhala zowawa (vesi 20).

- d. Gwiritsani ntchito timabokosi tili m'musiti kuti mukhazikitse zokhumba za utumiki wanu:

MALO OPANGIRA ZOKHUMBA

Lembani chimene mukufuna kudzachita. Ndidza...

Ndidzayamba kukwaniritsa chokhumbachi pa... Tsiku:

Ndidzamaliza kukwaniritsa chokhumbachi pa... Tsiku:

Ndidzakhala panso kuona m'mene zikuyendera masiku awa:

Tsiku: _____

Tsiku: _____

Tsiku: _____

Ndidzadziwa ngati ndakwaniritsa chokhumbachi chifukwa:

Anthu omwe adzagwire ntchito imeneyi ndi:

Ndipo aliyense adzagwira ntchito motere:

Chokhumba ichi chidzatithandiza kukwaniritsa cholinga chathu mu dongosolo la Mulungu chifukwa:

Ndalama zomwe zidzafunike ndi izi:

(Konzani dongosolo lanu la ndalama zomwe zidzafunike ndi momwe zidzagwirire ntchito)

CHAPUTALA 5

ANTHU NDI NDONDOMEKO: KUKWANIRITSA DONGOSOLO

ZOLINGA

Mukamaliza phunziro iri muzikwanitsa:

- a. Kupereka tanthauzo la mau oti “ndondomeko.”
- b. Kufotokozera zochitika chitika ziri m’musizi pokwaniritsa dongosolo:
 1. Kusankha
 2. Kulumikizana ndi ena
 3. Kugawa ntchito
 4. Kuphunzitsa anthu
 5. Kuika anthu m’ malo
 6. Kuika nthawi
 7. Kukonza dongosolo la ndalama
 8. Kupanga ziganizo
 9. Kuonanso zomwe zikuchitika
 10. Kauniuni wa zochitikazo
- c. Kufotokozera fanizo la zoikamo vinyo ndi zovala.

VESI LOTSOGOLERA

Pakuti mwa chidziwitso chako wofokayo atayika, ndi mbalame amene Khristu anamfera. (1 Akolinto 8:11)

MAU OYAMBA

M’maphunziro apitawa mwadziwa cholinga cha utumiki wanu ndi kuphunzira momwe mungapangire madongosolo. Koma madongosolo paokha siokwanira. Monga momwe chikhulupiriro chopanda ntchito chimakhalira chakufa chimodzimidzinso madongosolo opanda zochitika sakwaniritsa chirichonse.

M’phunziro lino muphunzira za kukwaniritsa dongosolo lanu. Kukwaniritsa dongosolo kumatanthauza kuchitapo kanthu pa zomwe mwakonza. Izi zimachitika kudzera mu ndondomeko zoyenera ndi anthu okhulupirika.

ANTHU NDI NDONDOMEKO

Ndondomeko ndi mndandanda wa zinthu zomwe munthu akuyenera kuchita pofuna kukwaniritsa dongosolo lake. Ndi njira komanso zochitika kapena ntchito yomwe mtsogoleri amachita kuti akwaniritse dongosolo lake. Anthu ndi zipangizo zomwe Mulungu amazigwiritsa ntchito mu ntchito ya utumiki pa dziko lonse lapansi. Ndondomeko zoyenera komanso anthu okhulupirika ndizofunika kuti dongosolo likakwaniritsidwe moyenera.

KUKWANIRITSA DONGOSOLO

Kuti mukwaniritse dongosolo moyenera, mukuyenera poyamba mulimvetse bwino dongosololo. Ichi ndicho chifukwa chimene mukuyenera kulemba dongosolo lanu monga momwe mwaphunzira mu Chaputala 4. Kumbukirani kuti dongosolo likuyenera kukhala ndi:

- Mfundo ya chenicheni chomwe chikuyenera kuchitika.

- Kafotokozeredwe ka momwe mugwirire ntchito yokwaniritsa (ndondomeko, zochitika).
- Omwe agwire ntchito (anthu omwe akufunika)
- Nthawi yomwe mukhale mukuchita zimenezi (masiku ndi nthawi zounikira ngati mukupita chitsogolo kapena ay)
- Dongosolo la ndalama zofunika

Kuti dongosolo likwaniritsidwe pali zinthu zomwe mtsogoleri akuyenera kuchita monga:

KUSANKHA

Mu nthawi ya utumiki wake wa pansi pano, Yesu anasankha anthu omwe agwire nawo ntchito, ophunzira. Izi ndi zina mwa ndondomeko zomwe mungatsate pamene mukusankha anthu oti mugwire nawo ntchito:

1. Amuna ndi akazi okhulupirika.
Sankhani amuna ndi akazi okhulupirika. Awa ndi iwo amene alandira Uthenga Wabwino ndipo miyoyo yawo yaonetsera kulapa ndi kusintha kwenikweni. Sankhani iwo amene ali ndi maitanidwe pa cholinga chomwe Mulungu ali nacho pa utumiki wanu. Ngati munthu alibe maitanidwe ndi mtundu wa utumiki womwe inu mukuchita, sakhala kuchoka chidwi kenako amasiya kutumikira mwa mphamvu. Mulungu ali ndi dongosolo lapaderadera ndi munthu wina aliyense, ndipo ngati ali pamalo poti Mulungu sakufuna kuti akhale, munthuyo sapambana konse mu utumiki. Pokhapokha cholinga cha utumiki wanu chiri cholinga chawonso. Sankhani iwo amene ali odzala ndi Mzimu Woyera ndipo ali ndi mbiri yabwino (Machitidwe 6:8). Iwo amene akutumikira ngati atsogoleri akhale ndi zoyenera za atsogoleri auzimu zomwe ziri pa Tito 1:5-9 ndi 1 Timoteyo 3:1-13.
2. Mphatso za Mzimu:
Sankhani anthu omwe ali ndi mphatso zogwirizana ndi ntchito yomwe mukuwapatsa. Umu ndi momwe mpingo woyamba umasankhira anthu maudindo. Mwachitsanzo, anthu omwe ali ndi mphatso yophunzitsa sangachite bwino kwenikweni ku utumiki wakutembenuka mtima. Ndipo omwe ali ndi mphatso yolalikira za kutembenuka mtima sangachite bwino kutumikira ngati abusa.
3. Maluso ndi kuthekera:
Pambali pa mphatso zauzimu, Mulungu amapereka maluso komanso kuthekera kosiyanasiyana. Ena amachita kuphunzira malusowa nkupita kwa nthawi. Onani kaye ntchito yomwe ikufunika kuchitika ndipo pezani anthu omwe ali ndi maluso ogwirizana ndi ntchito ya utumikiyo. Mwachitsanzo, Mose analandira dongosolo la mamangidwe a chihema kuchokera kwa Mulungu ndipo iye anapeza anthu omwe anali ndi maluso omanga. Onani Eksodo 35:30-34. Nthawi zonse kumbukirani kuti nkosavuta kutenga munthu wauzimu kuti mumphunzitse maluso omwe akusowekera pa ntchito yake kusiyanana ndi kutenga munthu wachikunja wotha bwino ntchito kuti mumphunzitse kukhulupirika.
4. Ukadaulo wa utumiki:
Onani zomwe munthu wachitapo kale mu utumiki. Ngati watumikira kale bwino mu utumiki wofanana ndi womwe mukumpatsa, ndiye kuti ali ndi mphatso ndi kudzodza kofunika pa udindowo.

5. Zabwino ndi Zofooka:

Onani zabwino ndi zofooka muuzimu za munthuyo. Kodi ndi ubwino uti womwe ali nawo womuyenereza udindowu? Nanga ndi zofooka ziti zomwe zitha kubweretsa mabvuto ndipo mungathane nawo bwanji mabvutowo?

KULUMIKIZANA NDI ENA

Mukuyenera kufotokozerana anthu ena za madongosolo anu momveka bwino. Anthu akadziwa zomwe mukufuna mutachita kumakhala kosavuta kuti atenge nawo mbali molingana ndi maudindo awo. Ubwino wakulumikizana ndi ena ukuonekera mu nkhani ya Nsanja ya Babelo pa Genesesi 11:1-9.

Anthu akuyenera kudziwa:

a. Dongosolo Lalikuru:

Akuyenera kumvetsa bwino dongosolo lanu lalikuru ndi momwe likukwaniritsira cholinga chachikuru cha Mulungu komanso cholinga chapaderadera cha bungwelo.

b. Tsatanetsatane wa Dongosolo:

Izi ndi monga anthu omwe akugwira ntchito m'malo osiyanasiyana, dongosolo la ndalama, nthawi yogwirira ntchito, zoyenera kuchitika, ndi momwe mudzachitire kauniuni wa zochitika zanu kuti muone ngati mwakwaniritsadi zomwe munakonza.

c. Mbali yawo yeniyeni mu Dongosolo:

Anthu amafunika kudziwa zenizeni zomwe akuyenera kuchita iwowo ngati munthu paokha, nthawi yake, ndalama zake, zipangizo, ndi anthu ena omwe agwire nawo ntchito.

Kufotokozerana ena kumalimbikitsa anthu pa ntchito ya utumiki. Anthu akalimbikitsika, mutha kuwadziwitsa za mavuto omwe akuyenera kuwayembekezera kuti ntchitoyo ichitike. Komanso pamakhala kuthekera kochita zinthu ndi zolinga zoyenera. Kumbukirani:

Mthenga wolakwa umanga mzoipa; Koma mtumiki wokhulupirika alamitsa.
(Miyambo 13:17)

KUGAWA NTCHITO

Mutatha kufotokozerana ena za dongosolo lanu, mukuyenera kugawa ntchito pa zomwe zichitikezo. “Kugawa ntchito” ndiko kupereka udindo ndi mphamvu kwa ena kuti atumikire. Mugawa ntchito, mumawapatsa ena udindo pa ntchito ina yake, mphamvu yogwirira ntchito, komanso udindo woonetsa kuti ntchito yagwirika moyenera.

Chitsanzo chabwino cha m'Baibulo chogawa ntchito chiri pa dongosolo lomwe Yetero anakonza Mose nalikwaniritsa. Werengani Eksodo 18:13-27. Mose analema ndi kugwira ntchito yekha popeza inali yaikuru. Yetero anamuza momwe angagawire ntchito ndi ulamuliro kuti ntchito ya utumiki igwirike.

Amuna omwe anagawiridwa ntchito amafotokozerana Mose momwe ntchito yawo ikuyendera.

Mtsogoleri amayenera kutanganidwa ndi ntchito zikuluzikulu pa dongosolo lomwe lakonzedwa monga kuona momwe anthu akugwirira ntchito ndi kupanga ziganizo. Kotero nkoyenera kufotokozerana bwino tsatanetsatane wa momwe ntchito ikuyenera kuyendera.

Mukupereka udindo kwa munthu, mumayeneranso kumpatsa ulamuliro kapena mphamvu yogwirira ntchitoyo. Izi zimatanthauza kupereka mphamvu ndi zipangizo zomwe zikufunika kuti ntchitoyo igwirike.

Kuti mukhazikitse ulamuliro ndi udindo, ndi bwino kulemba bwino lomwe zoyenera kuchita pamene mukupereka ntchito kwa munthu. Izi ndi zomwe zimatchulidwa kuti “zoyenera kuchita pa nthito” kapena “zoyenera kuchita pa utumiki.” Onani kumapeto kwa phunziro lino chitsanzo cha izi.

Mukalunjika bwino m’kafotokozeredwe ka udindo wa munthu, iye amadziwa choyenera kuchita. Amadziwanso kuti mudzaona ngati ntchitoyo yakwaniritsidwa komanso moyenera.

Poomba mkota

Kugawa ntchito ndiko kupatsa ena:

- Udindo: Kuti agwire ntchito ya utumiki.
- Mphamvu: Kuti ntchitoyo igwirike.
- Udindo woonetsa kuti ntchitoyo yagwirika bwino.

Kugawa ntchito nkofunika chifukwa:

- Kumapereka nthawi yokwanira kwa atsogoleri yochita zinthu zofunika kwambiri. Eksodo 18:13-27; Machitidwe 6:3-4.
- Kumalola anthu ena kuti akhale maphunziro ndi ukadaulo wa utumiki.
- Kumatsatira dongosolo la Mulungu lakuti Mpingo umagwira ntchito ngati “thupi limodzi” pamene aliyense akugwiritsa ntchito mphatso yake kutumikira Ambuye.
- Kumadzutsa atsogoleri atsopano

KUSULA ANTHU

Anthu ena omwe muwagawire kapena kuwapatsa ntchito akhala oti ali kale ndi maluso omwe akufunikira kugwira ntchitoyo. Koma ena afunika kuphunzitsidwa. Kuphunzitsaku kudzadalira mtundu wa ntchito komanso maluso omwe munthu akusowekera. Ena afunika maphunziro ambiri kuposa ena chifukwa cha kuperewera kwa maphunziro ndi ukadaulo wao pa ntchitoyo. Ntchito zina ndi zovuta kuposa zina ndipo zimafunika upangiri wochuruka.

Kusula anthu pa ntchito ya utumiki ndi ntchito yopitirira. Anthu amafunika kuti azikula m’chidziwitso, m’maluso komanso m’moyo wauzimu nthawi ndi nthawi.

KUIKA ANTHU M’MALO

Anthu amene aphunzitsidwawo akuyenera kuikidwa m’malo mwao kuti athe kugwira bwino ntchito ya utumiki limodzi.

Apa ndi pamene zimaonetsera kuti anthuwa ali ndi cholinga chimodzi. Nthawi zonse pamene anthu awiri agwirizana kuti agwire ntchito limodzi, mgwirizano umakhalapo. Kuika anthu m’malo ndi ntchito yobweretsa pamodzi gulu la anthu kuti achite ntchito ya utumiki pamodzi. Izi zimabweretsa kudziwa kuti akutsogolera ndi ndani ndipo akugwira ndi ndani pamene akukwaniritsa dongosolo. Pamakhala posavuta kudziwa kuti ntchito yakutiyakuti ili m’manja mwa wakutiwakuti.

Popanda dongosolo loika anthu m'malo mwake, pakhala chisokonezo chachikuru. Zotsatira zake zimakhala zakuti chimwemwe chimasowa, anthu amang'ung'uza komanso ntchito zofunikira sizichitika. Werengenani nkhani ya pa Machitidwe 6:1-7 kuti muone za bvuto lomwe linadzuka mu Mpingo woyamba ndi momwe atumwi anaikira anthu m'malo pothana ndi bvutolo.

Musaike anthu m'malo potengera zomwe anthu ena anachitira ku gulu lawo. Kachitidwe kanu ka zinthu kakhale kakugwirizana ndi zosowa, cholinga, ndi dongosolo lanu. Umu ndi m'mene mpingo woyamba unakonzerera zinthu. Si kuika zinthu m'malo kumene kunapangitsa kuti mpingo ndi utumuki zikhalepo. Koma kuti mpingo unabweretsa dongosolo loika anthu m'malo pamene kunafunika kutero. Izi zikufotokozeredwa bwino pa Machitidwe 6:1-7.

Mulungu Atate, Yesu Khristu, ndi Mzimu Woyera ali ndi dongosolo lotero nawo. Yense wa iwo ali ndi udindo ndi mautumiki apaderadera omwe afotokozeredwa m'Baibulo.

Chimodzi mwa zitsanzo za kuika zinthu m'malo mu chilengedwe cha Mulungu ndi thupi la munthu. Mulungu anagwiritsa ntchito chitsanzo cha chilengedwechi pofuna kufotokozerera za momwe mpingo umayenera kugwirira ntchito yauzimu.

Mukaika Yesu kukhala mutu wanu, mumagwira ntchito limodzi bwino kukwaniritsa zolinga ndi madongosolo auzimu.

Nthawi kufotokozerera za kuika anthu m'malo kumamveka bwino mukachita kujambula dongosololi. Pachingerezi chithunzi chimenechi chimatchedwa “organizational chart” ndipo muona zitsanzo zake m'chigawo cha “Kupiriza Kuphunzira.”

Kuonjezera apo, kuika anthu m'malo ogwira ntchito kumathandiza ogwira ntchitowo kuti akhale ndi mzimu womvana pakati pawo. Kuwabweretsa pamodzi mosavuta kuti achite ntchito ya utumiki komanso kukhazikitsa maubale abwino pakati pawo.

Kumbukirani kuti tikaika anthu mogwirizana ndi Mau a Mulungu, palibe munthu wina amene amakhala wamkulu kuposa mnzake. Tonsefe ndi ziwalo za Thupi la Khristu zomwe zikugwira ntchito limodzi kukwaniritsa zolinga za Mulungu. (Onani Aefeso 1:22-23; 4:15-16; Akolose 1:18; 1 Akorinto 12).

KUIKA NTHAWI YA KACHITIDWE KA ZINTHU

Mutakonza dongosolo lanu, munaika masiku omwe muyambe kukwaniritsa dongosolo lanulo, kuunika, komanso kumaliza. Ndiye mukufunika kuikanso nthawi ya zinthu zina mwatsatanetsate zomwe ziri mbali imodzi ya dongosololo.

Mwachitsanzo, mu chaputala chapitachi kunaperekedwa chitsanzo chofikira dera Asilamu omwe akukhala makilomita asanu kuzungulira mpingo wanu pofikira tsiku lakutilakuti. Masiku anaikidwa oyambira ntchito, kuiunika pamene ikugwirika, komanso kumaliza ntchitoyo.

Tiyerekeze kuti mukukwaniritsa dongosolo lotereli, mukuyenera tsopano kuika masiku amene muyambe kuyenda khomo ndi khomo kugawa Uthenga Wabwino. Masiku ena olengeza ndi kuchita mwambo woyamba wa mapemphero akuyeneranso kuikidwa.

Kuika nthawi kotereku kumakuthandizani kuti mugwiritse ntchito mwanzeru nthawi yanu. Mukuyenera kugwiritsa ntchito mwanzeru nthawi yanu chifukwa nthawi imene muli nayo kuti mugwire ntchito ya Mulungu ndi yochepa:

Tiyenera kugwira ntchito za Iye wondituma Ine, pokhala pali msana; ukudza usiku pamene palibe munthu angakhoze kugwira ntchito. (Yohane9:4)

Potero, penyani bwino umo muyendera, si monga opanda nzeru, koma monga anzeru; akuchita machawi, popeza masiku ali opipa. Aefeso 5:15-16)

Mukagwiritsa ntchito nthawi yanu mwanzeru, mumaika zinthu zofunikira kwambiri kukhala patsogolo. Kutanthauza kuti mumachita zokhazo zimene ziri zofunika kwambiri kusiya zina. Atsogoleri abwino amadziwa kukana kuchita zinthu zomwe sizikugwirizana ndi zolinga komanso zokhumba zawo.

Unikirani chiri chonse chomwe mukuchita molingana ndi cholinga chapaderadera chimene Mulungu wakuitanirani. Ikani maitanidwe anu kukhala patsogolo. Musatengeke ndi zinthu zina, ngakhale zikuoneka kuti ndi zofunika kwambiri.

Monga mwa fanizo la akapolo ndi matalente awo, Mulungu adzakuwerengerani mulandu pa utumiki wapaderadera umene wakupatsani pa tsiku la chiweruzo. Mutha kukhala otanganidwa kuchita zinthu zina ndi zina zabwino ndithu pamaso pa Mulungu koma nkusemphana ndi cholinga chomwe Mulungu wakudzutsirani mu utumiki.

Mukuyenera kukhala ndi kalendala kuti muike nthawi ya zomwe muchite. Muike zochitika za masabata komanso masiku:

1. Dongosolo la Sabata:

Kumayambiliro a sabata iriyonse, ikani dongosolo. Pemphererani sabata imeneyo kuti Mulungu akutsogolereni pamene mukuika nthawi ya zinthu zomwe mukufuna kuchita tsiku lililonse m'sabata imeneyo. Yankhani mafunso awa:

- a. Kodi chomwe chikuyenera kuchitika m'sabata imeneyi ndi chiyani? Uwu ndi mndandanda wa zinthu zofunika kwambiri kuti zichitike. Zinthu zomwe ngati sizichitika pakhala mavuto kapena kuchedwa pa zinthu zina.
- b. Kodi chikuyenera chitachitika ndi chiyani? Izi ndi ntchito zomwe zikubwera pambuyo pa ntchito zofunika kwambiri. Mutha kuzichita mukamaliza ntchito zofunika kwambiri zomwe ziri pa mndandanda woyamba uja.
- c. Kodi mutakhala ndi nthawi yokwanira mungachite chiyani? Izi ndi ntchito zomwe mutha kuzibweretsa m'sabata inayo popanda vuto liri lonse. Tsopano unikani mndandanda wanu kuti muone ngati pali ntchito ina imene mutha kuipereka kwa anthu ena. Mukatero, mukhala ndi mpata wochita zinthu zimene oyenera kuchita ndinu nokha.

2. Dongosolo la Tsiku

Kumayambiliro a tsiku liri lonse, m'pempheni Mulungu kuti akutsogolereni pa zomwe mukuyenera mutachita tsiku limenelo. Onani zomwe munakonza kuti muchite sabata imeneyo. M'pempheni Mulungu akuonetsereni zomwe mukuyenera kuchita tsiku limenelo. Lembani ndi kuzisanja molingana ndi kufunikira kwake. Yankhani mafunso omwe mumadzifunsa m'dongosolo la sabata aja. Kodi chikuyenera kuchitika lero ndi chiyani? Nanga muchite ziti mukamaliza ntchito

zofunikirazi? Kodi muchita ntchito ziti mukakhala ndi nthawi yokwanira? Nanga ntchito zoti mupereke kwa ena ndi ziti?
Onesetsani kuti mu zonsezi muli ndi nthawi yanu yapadera yokhala pamaso pa Mulungu m'pemphero ndi kusanthula Mau tsiku ndi tsiku. Izi ndi zofunika chifukwa...

**Kuopa Yehova kutanimpitsa masiku; koma zaka za oipa zindzafinimpha.
(Miyambo 10:27)**

**Umlemekeze m'njira zakozonse, Ndipo Iye adzaongola mayendedwe ako.
(Miyambo 3:6)**

Monga Mtumwi Paulo, nthawi zonse muzikhala wolola Mzimu Woyera kusintha zinthu. Kumbukiraninso nthawi zonse kuti utumiki timachitira anthu. Kotero, musanyalanyaze anthu chifukwa cha dongosolo kapena chifukwa chotanganidwa ndi utumiki.

Komanso, mukhale osamala kuti anthu omwewo asakupangitseni kuti mutanganidwe ndi zinthu zina kufika pa mulingo woononga nthawi ndi mphamvu zanu.

Kutanganidwa ndi zinthu zina, ngakhale zikhale ntchito zabwino, ndi chida chimene m'dierekezi amachigwiritsa ntchito kuti anthu asakwaniritse cholinga cha Mulungu pa moyo wao.

Werengani Nehemiya 6:10-12. “Mneneri wa Mulungu anayesa kunyengelera Nehemiya kuti asiye ntchito yomanga linga napite kukachisi ku zokambirana ponena kuti ndibwino kuti akabisale ku nyumba ya Mulungu kusiyana ndi kuphedwa ngati sabwera. Izi zikuoneka kuti ndi zauzimu ndithu!

Koma Nehemiya anazindikira kuti mneneriyu sanatumidwe ndi Mulungu. Sanapite ku zokambiranazo. Mulungu anamuuzza kuti amange kachisi, ndipo anadzipereka ku ntchitoyo.

3. Magawo Ena a Nthawi:

Mutha kuika nthawi yochitira zinthu molingana ndi magawo ena a nthawi.

Mwachitsanzo, ngati ndinu mphunzitsi mutha kugawa nthawi yanu molingana ndi materemu a sukulu yanu.

Ndi bwino kupanganso dongosolo la chaka la utumiki. M'pempheni Mulungu kuti akuthandizeni kuika zokhumba za chaka molingana ndi cholinga cha Mulungu.

Kudziwa zokhumba zanu za chaka zikuthandizani pamene mukupanga dongosolo la sabata lirilonse.

Pamene anthu angapo akugwira ntchito limodzi kukonza dongosolo, aliyense wa iwo akuyenera kukhala ndi kalendala woonetsa tsatanetsatane wa ntchito zonse zofunika kuchitika. Izi zimathandiza kuti wina aliyense kukumbukira chomwe chikuyenera kuchitika ndi nthawi yake.

KUKONZA DONGOSOLO LA NDALAMA

Nthawi imene mumakonza dongosolo la kagwiridwe ntchito kanu, munakonzanso dongosolo loonetsa ndalama zomwe zifunike komanso momwe zigwirire ntchito.

Pamene mukukwaniritsa dongosolo lanu, gwiritsani ntchito dongosolo limeneli kuti lizikutsogolerani kudziwa momwe mugwiritsire ntchito ndalama. Njira yachidule yodziwira momwe mukugwiritsira ntchito ndiyokhala ndi malo amene mwalembapo mtengo wa chinthu

chomwe mwakonza kuti mukagule, mtengo weniweni umene mwagulira, ndi ndalama zotsala ngati chenje. Chitsanzo chake nachi:

Dongosolo: Kugulira membala aliyense wa mumpingo Baibulo.

NDONDOMEKO YA NDALAMA

Katundu	Ndalama zoikidwa	Ndalama zomwe zagwira ntchito	Ndalama zotsala
Mabaibulo	70, 000	60, 000	10, 000

Mwina mutha kuona kufunika kosintha dongosolo lanu la ndalama loyamba. Popeza zinthu zina zitha kukhala zokwera mtengo kapena kutsika poyerekeza ndi mitengo imene munaika poyamba.

KUPANGA CHIGANIZO

Pamene mukukwaniritsa dongosolo lina lirilonse, mtsogoleri amayenera akhale akupanga ziganizo zosiyanasiyana zokhuzana ndi ntchitoyo. Njira yopangira ziganizo mogwirizana ndi Mau a Mulungu liri mu phunziro la Harvestime International Institute lotchedwa, “Mfundo za Baibulo Zoyendetsera Zinthu” ndi “Kudziwa Liu la Mulungu.” Wonani paphunziro amenewa ndipo akuthandizani kuti mupange ziganizo zoyenera.

KUONANSO ZOMWE ZIKUCHITIKA

Mutatha kukwaniritsa dongosolo lomwe munakonza, mukuyenera kukhala ndi nthawi yomaona momwe zinthu zikuyendera. Kumanani ndi omwe akugwira ntchitoyo:

- a. Kuti mutsimikizike ngati anthu akukwaniritsa maudindo omwe apatsidwa.
- b. Poonesetsa kuti anthu ali ndi ndalama komanso zipangizo zokwanira kugwira ntchito.
- c. Kuona ngati dongosolo likuyenda mogwirizana ndi nthawi imene yaikidwa.
- d. Kuona ngati mukuyenda mogwirizana ndi dongosolo lanu la ndalama.
- e. Kuti muthe kudziwa ngati mukufunika kusintha dongosolo lanu penapake.
- f. Kulumikizitsa magawo osiyanasiyana a dongosolo lanu pamodzi ndi anthu omwe akugwira ntchito.
- g. Kukonza mabvuto omwe ali mu dongosolo lanu kapena omwe adzuka pakati pa anthu omwe akugwira ntchito.

KUUNIKA DONGOSOLO

Iyi ndi ndondomeko younikira dongosolo lanu mosamalitsa kuti muone ngati ndiyothandiza pokwaniritsa cholinga cha utumiki. Muphunzira za kuunikira madongosolo mu phunziro linalo.

VINYO WATSOPANO NDI ZOTENGERAMO VINYO ZAKALE

Pamene Yesu anayamba kutumikira, anakumana ndi zotsutsa zambiri. Anthu ena sanalandire chiphunzitso chake chomwe chinali chachilendo kwa iwo posatengera kuti chimagonera pa ziphunzitso za m’Chipangano Chakale. Ndipo ena sanalandire zozizwa zimene Iye anachita.

Yesu atayitana anthu ena kuti akhale ophunzira ake, iwo anakana kumtsatira. Atsogoleri ambiri a chipembedzo anamangika pa miyambo ndipo anakana kusintha.

Satana nthawi zonse amatsutsa cholinga ndi madongosolo a Mulungu. Nthawi zonse mukayamba kukwaniritsa dongosolo latsopano mogwirizana ndi cholinga cha Mulungu, mudzakumana ndi zotsutsa. Yesu anapereka zitsanzo ziwiri za izi. Iye anati:

Ndipo kulibe munthu aphathika chigamba chan saru yaiwisi pa chopfunda chakale; pakuti chigamba chache chizomoka ku chopfundacho, ndipo chichita chiboo chachikuru. (Mateyu 9:16)

Kapena samathira vinyo watsopao mmatumba akale; akatero, matumba aphulika ndi vinyo atayika, ndi matumba aonongeka; kom athira vinyo wasopano m'matumba atsopano, ndi zonse ziwiri zisungika. (Mateyu 9: 17)

Kudzera mu zitsanzo izi, Yesu anaonetsera kuti nthawi zina kumakhala kovuta kuti anthu amene azikika mu miyambo ya chipembedzo chawo kuti alandire madongosolo ndi mabvumbulutso atsopano. Yesu komanso Mtumwi Paulo anakumana nazo izi mu utumiki wao. Inunso mukumana nazo. Mukumana ndi zotsutsa kuchokera mkati ngakhale kunjwa kwa mabungwe a chipembedzo amene alipo kale.

Mukakumana ndi zotsutsa zotere, tsatirani zomwe Yesu komanso Mtumwi Paulo anachita. Iwo anayesetsa kugwira ntchito mkati mwa madongosolo a chipembedzo omwe analipo kale. Amapita kukapemphera ku sunagoge pafupi pafupi ndi kutumikira mwayi ukapezeka. Sanalimbane ndi madongosolo a chipembedzo omwe anawapeza. Analola kuti madongosolowo apitirire. Koma sanalole kuti miyambo kapena kutsutsidwa ndi atsogoleri a chipembedzo kutsekereze zinthu zatsopano zomwe Mulungu amachita.

Atakanidwa ndi dongosolo la miyambo, Yesu ndi Paulo anatengera utumiki wao kunjwa kwa sunagoge. Anadzutsa “zotengeramo vinyo zatsopano.” Okhulupirira atsopanowa anali okonzeka kulandira bvumbulutso komanso dongosolo latsopano la kachitidwe ka zinthu (Mpingo woyamba). Anali nako kuthekera konyamula “vinyo watsopanoyu.” Mu njira ina, ndi zotheka kudzutsa munthu kwa akufa, ndipo Mulungu amachita zimenezo mu nthawi yake. Koma kubereka mwana watsopano ndiye kophweka kwambiri.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osaonera.

2. Kodi ndondomeko ndi chiyani?

3. Kodi fanizo la vinyo watsopano ndi zotengeramo vinyo zakale zikutiphunzitsa chiyani pa nkhani yothana ndi kutsutsidwa kwa madongosolo ndi zolinga za Mulungu.

4. Tengani pepala lapadera ndipo kufotokozerwa kwa maudindo ali m'musiwa omwe amagwiritsidwa ntchito pokwaniritsa dongosolo la Mulungu:

- Kusankha
- Kulumikizana ndi ena
- Kugawa ntchito
- Kuphunzitsa anthu
- Kuika anthu m'malo
- Kuika nthawi
- Kukonza dongosolo la ndalama
- Kupanga ziganizo
- Kuonanso zomwe zikuchitika
- Kauniuni wa zochitikazo

(Mayankho a mafunsowa aperekedwa ku mapeto a bukhu lino)

KUPIRIZA KUPHUNZIRA

M'musimu muli chitsanzo cha dongosolo la maudindo. Chitsanzo chayerekezedwa ndi nkhani yofikira mtundu wa anthu a chilankhulo cha ku Spain okhala mozungulira mpingo wina. Nkhaniyi ili Chaputala 4. Zitsanzo zina zaperekedwa m'magawo owonjezera a bukhu lino.

Joe Smith, wamkulu wa dongosolo, akugwira ntchito pa udindowu pansa pa utsogoleri wa Abusa a mpingo.

A pa mpando asanu asankhidwa kuti ayang'anire gawo lina lake la dera lozungulira mpingo.

Joe Smith amayang'anira atsogoleriwa pamene akukwaniritsa ntchito yofikira khomo ndi khomo kugawa Uthenga Wabwino, kusiya kalata za Uthenga Wabwino pa khomo liri lonse ndi kupereka kabuku ka Uthenga Wabwino wa Yohane kwa aliyense amene watembenuka kumene mtima.

Kumbukirani kuti m'bungwe liri lonse palibe amene ndi wofunika kwambiri kuposa mnzake. Tonse ndi ziwalo za Thupi limodzi la Khristu kugwira ntchito pamodzi kukwaniritsa zolinga za Mulungu. (Onani Aefeso 1:22-23; 4:15-16; Akolose 1:18; ndi 1 Akorinto 12).

Kodi mumadziwa kuti Baibulo limakhazikitsa dongosolo la kayendetsedwe ka zinthu m'banja la Chikristu? Umu ndi momwe dongosoli limaonekera:

Mulungu

Mwamuna

Mkazi

Ana

Mwamuna ndiye mutu wabanja. Mkazi ndi wothandizira. Ana akuyenera kumvera makolo.

M'musimu muli dongosolo lomwe Mose anagwiritsa ntchito kukwaniritsa cholinga cha Mulungu mu Eksodo 18:13-27

Mulungu

Mose

Olamulira zikwi

Olamulira mazana

Olamulira makumi

Otsogolera zikwi awa anali amuna oposa 100. Ndipo aliyense amayang'anira amuna okwana 50 amene amayang'anira gulu la amuna okwana khumi aliyense. Atsogoleri 50 amene amalamulira amuna khumiwa amapita kwa aja amalamulira magulu a amuna 50 ndi mavuto awo. Ndipo oyang'anira amuna 50 amapita kwa oyang'anira amuna 100 amene amapita kwa

amuna olamulira zikwi ndi mavuto awo. Nkhani yokhayo imene yakanika kwa amuna olamulira zikwiwa ndi imene imapita kwa Mose kuti akapereke chigamulo.

Mose atatenga utsogoleri wa Israel, Mulungu anampatsa maudindo okwana anayi. (Eksodo 18:19-21).

Poyamba, kubweretsa mavuto a anthu kwa Mulungu.

Kachiwiri, kuwaphunzitsa njira ya chilungamo pa maso pa Mulungu.

Kachitatu, kuwapatsa luso lofunika pa ntchito zomwe anali nazo.

Kachinayi, kusankha atsogoleri okhala ndi kuthekera kuti amuthandize pa ntchito yotsogoleri mtundu wa Israel.

Popeza kuti mwaona zina mwa zitsanzo za dongosolo la kachitidwe ka zinthu, konzani dongosolo lanu loti likuthandizeni kukwaniritsa cholinga chanu mu utumiki.

Zina mwa zinthu zomwe zimakhala zotchinga zikuluzikulu pa kulumikizana koyenera. Mukuyenera kugonjetsa zina mwa izo kuti muthe kulumizana bwino ndi anthu ena:

- Kusiyana chilankhulo
- Kusiyana kalankhulidwe
- Kupatula zina pamene mukulumikizana ndi ena
- Mantha
- Kuweruzana kosayenera
- Kusakhala ndi chidwi
- Uthenga wosamveka bwino
- Umbuli
- Miyambo
- Maphunziro osakwanira
- Kuuma mtima

Werengani ndime ziri m'musizi kuti muone kufunika komaliza ntchito imene mwaiyamba. Paulo akulankhula kwa anthu a mpingo wa ku Akorinto:

Ndipo m'menemo ondichula choyesa ine, pakuti chimene chindipindulira inu, amene munayamba kale chaka chapitachi, si kuchita kokha, komanso kufunira.

Koma tsopano tsirizani kufunaku; kuti monga kunali chibvomerezo cha kufunira, koteronso kukhale kutsiriza kwacha chimene muli nacho (2 Akorinto 8:10-11).

Limodzi mwa madongosolo omwe anaikidwa mwa tsatanetsatane ndi kukwaniritsidwa m'Baibulo ndi la kumangiddwa kwa chihema. Pamene mukuwerenga ndime zotsatirazi, lingalirani zomwe mwaphunzira mu bukhu lino la Kayendetsedwe ka Zinthu molingana ndi Mau a Mulungu:

- Kukhazikitsa cholinga: Exodus 25:8
- Kukonza madongosolo: Exodus 25-31
- Kukwaniritsa madongosolo:

a. Kusankha:	Exodus 35:30-35; 36:2
b. Kulumikizana:	Eksodo 35
c. Kugawa ntchito:	Eksodo 36:1-3
d. Kusula anthu:	Eksodo 35:34
e. Kuika zinthu m'malo:	Eksodo 36-40
f. Kuika nthawi ya ntchito:	Eksodo 36-40
h. Kukonza dongosolo la ndalama:	Eksodo 35; 36:5-7
i. Decision making:	Eksodo 36:6-7
j. Kuonanso ntchito:	Eksodo 39:43
- Kuunikira dongosolo la ntchito:	Eksodo 39:43; 40:33-35

CHAPUTALA 6

KUMALIZITSA: KUUNIKIRA DONGOSOLO

ZOLINGA

Mukamaliza chaputaala chino muzikwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kutanthauzira mau oti “kuunikira.”
- Kufotokozera ubwino wa kuunikira.
- Kukhazikitsa ndondomeko ya kaunikiridwe ka zinthu.
- Kuunikira madongosolo ndi ntchito yomwe yachitika.
- Kudziwa zifukwa zomwe zimapangitsa kuti madongosolo azikanika kukwaniritsidwa.
- Kugwiritsa ntchito zomwe mwapeza pa kuunikira madongosolo anu kuti mukonze madongosolo omwe alipo kale kapena omwe mukonze kumene.

VESI LOTSOGOLERA

Pakuti ndi chisomo chapatsidwa kwa ine, ndiuza munthu ali yense wainu, kuti asadziyese koposa kumene ayenera kudziyesa; koma aganize modziletsa yekha, monga Mulungu anagawira kwa munthu ali yense muyeso wa chikhulupiriro. (Aroma 12: 3)

MAU OYAMBA

Mu Chaputala 4 munaphunzira za kuika zokhumba ndi dongosolo molingana ndi cholinga komanso madongosolo a Mulungu. Mu Chaputala 5 mwaphunzira za kukwaniritsa madongosolo. Mu phunziro lino muphunzira za kuunikira madongosolo kuti muone ngati mwakwaniritsa zokhumba zanu kapena ayi.

KUUNIKIRA

Mukamaunikira chinthu ndiye kuti mumakhala mukusanthula mosamalitsa kuti muone phindu lake. Iyi ndondomeko yosanthula madongosolo bwino lomwe kuti muone ngati akwaniritsa zokhumba za utumiki wanu kapena ayi.

Zokhumba zimaonetsera zomwe mukulinga mutakwaniritsa. Ndipo kuunikira kumaonetsera ngati mwakwaniritsadi zokhumba zanzu. Ngakhale Mulungu anaunikira ntchito yake. Mu Genesisi 1, Iye anasanthula ntchito yomwe analenga ndipo anati, “Ziri bwino.”

KUFUNIKA KWA KUUNIKIRA NTCHITO

Kuunikira ntchito kumakupangitsani kuti kukhala munthu amene zochita zake zikudziwika pamaso pa Mulungu, amene mutumikira nawo, amene mukuwatumukira komanso ngakhale pamaso pa inu eni.

Kuyambira pachiyambi, Mulungu wakhala akuyang’ana momwe munthu akuchitira pokwaniritsa zolinga zake. Adam ndi Hava anali ndi maudio amene Mulungu amawerengera m’ munda wa Eden.

Baibulo limatilimbikitsa kuti tizikhala ndi nthawi younikira moyo ndi utumiki wathu..

Pakuti ndi chisomo chapatsidwa kwa ine, ndiuza munthu ali yense wainu, kuti asadziyese koposa kumene ayenera kudziyesa; koma aganize modziletsa yekha, monga Mulungu anagawira kwa munthu ali yense muyeso wa chikhulupiriro. (Aroma 12: 3)

Mtumwi Paulo anati:

Kuti mukayese inu zinthu zosiyana; kuti mukakhale a mtima wona ndi wosalakwa, ku=fikira tsiku la Khristu; (Afilipi 1:10)

Nkhani yakuti Mulungu adzatiwerengera mlandu pa zonse zomwe tikuchita mu utumiki ikupezeka mu fanizo la matalente pa Mateyu 25:14:30. Baibulo limatiphunzitsanso kuti tili ndi udindo wosamalira anthu amene tikuwatumikira:

Wetani gulu la Mulungu liri mwa inu, ndi kuliyan'ganira, osati mokangamiza, koma mwaufulu, kwa Mulungu; osatsata phindu lonyansa, oma mwachangu;

Osati monga ochita ufumu pa iwo a udindo wanu koma okhala zitsanzo za gululo (1 Petro 5:2-3).

Baibulo limatiphunzitsa kuti tili ndi udindo woonetsera zomwe tikuchita pamaso pa omwe tikugwira nawo ntchito limodzi. Timagwira ntchito ngati thupi limodzi:

Ndipo diso silingathe kunenakwa dzanja, Sindikufuna ie=we, kapenanso mutu kwa mapazi, Sindikufunani inu. (1 Akolinto 12:21).

Mukadzaima pamaso pa Mulungu pa tsiku la chiweruziro, ntchito yanu idzaunikiridwa kuti aone phindu lake:

Koma ngati wina amanga pa mazikowo, golidi, siliva, miyala ya mtengo wache, mtengo, maudzu, dziputu, ntchito ya yense idzaonetsedwa; pakuti tsikulo lidzaisonyeza, chifukwa kuti yabvumbuluka m'moto; ndipo moto wokha udzayesera ntchito ya yense ikhala yotani. (1 Akolinto 3: 12-13)

Mulungu ali ndi madongosolo abwino, koma amagwiritsa ntchito anthu okhala ndi zofooka ngati ife kuti madongosolo akewo akwaniritsidwe. Popeza simuli angwiro, mukuyenera nthawi zonse kuunikira zomwe mukuchita. Izi zikuthandizani kudziwa ngati mukukwaniritsa cholinga ndi madongosolo a Mulungu moyenera. Ndipo kuunikira ntchito yanu kumakuthandizani kuphunzira kuchokera ku zopambana ndi zolephera zanu, kuonanso madongosolo omwe muli nawo, komanso madongosolo omwe mukhale mukukonza. Ngati mukuchitadi madongosolo a Mulungu, nkofunika kuwachita moyenera.

NDONDOMEKO YA KUUNIKIRA NTCHITO YOMWE YAGWIRIKA

Pamene mumaphunzira za kuika zokhumba, munazilemba mu njira yakuti mutha kuziunikira komanso kuziyesa kuti mudzakhale nako kuthekera kodziwa ngati zakwaniritsidwa kapena ayi. Munaikanso masiku omwe muzidzaonera momwe zinthu zikuyendera. Ndongomeko younikira zinthu ndi njira yosanthulira madongosolo anu.

Zinthu zomwe muchite pokhazikitsa ndondomeko za kuunikira ntchito nazi:

1. Lembani zokhumba zanu munjira yoti ndi zoyeseka ndipo mudzadziwa ngati mwawakwaniritsa.
2. Ikani masiku owonera momwe zinthu zikuyendera.
3. Pempherani musanayambe kuchita kauniuni. Mfusenani Mulungu akuonetsereni zofooka zomwe zikufunika kukonzedwa ndi kutsogolerani kupanga madongosolo ena ngati nkoyenera kutero.
4. Unikirani kuti muone ngati dongosolo lanu likuyenda mogwirizana ndi nthawi yomwe munaika komanso ngati likukwaniritsa zofunika kukwaniritsidwa. Ngati ziri choncho, pitirizani monga momwe munakonzero. Ngati siziri choncho:
 - a. Sinthani chokhumbacho: Lembaninso magawo ena a dongosolo lanulo, kapena kuchotseratu ndi kulemba lina. Popeza kuti simudziwiratu dongosolo lonse la mtsogolo la Mulungu, mukuyenera kukhala okonzeka kusintha zinthu. Kukonzanso madongosolo ndi mbali imodzi ya ntchito yokonza madongosolo mwa chikhulupiro.
 - b. Sinthani zinthu pakati pa ogwira ntchito: Mwina mufunika kuonjezera kapena kuchotsera chiwerengero cha anthu ogwira ntchito. Makamaka iwo amene chidwi chawo pa ntchito chazilara.
 - c. Sinthani tsiku lomwe munakonza lomalizira ntchito. Mwina mufunika nthawi yochuruka kuposa imene munakonza pachiyambi. Onjezeraninso nthawi younikira dongosolo lanu kuti muzidzaona momwe zinthu zikuyendera.
 - d. Sinthani kachitidwe ka zinthu: Mwina chokhumba chanu ndi chabwinobwino, koma bvuto litha kukhala njira zomwe mukugwiritsa ntchito mwina sizikuthandiza.
 - e. Sinthani dongosolo la ndalama mwina ndi mwina makamaka ngati mitengo ikusemphana ndi yomwe munakonza pachiyambi.
5. Mukamaliza dongosolo, liunikireni kuti muyankhe mafunso awa:
 - a. Kodi munafikira chokhumba chanu? Kodi mwamaliza zomwe munayamba? Kapena munatengeka ndi zinthu zina? Musaunike dongosolo lanu molingana ndi zochitikachitika zomwe zinalipo koma molingana ndi zotsatira za zochitikazo. Kodi zochitikachitika zanu zinakuthandizani kufikira chenicheni chomwe munakhumba?
 - b. Kodi dongosolo lanu linathandizira pa kufikira cholinga chanu monga momwe munaganizira?
 - Kodi munalephera pati, motani, chifukwa chiyani? Ndi zifukwa ziti zomwe zinakupangitsani kuti mulephere? Kumbukirani, musakhumudwitsidwe ndi zofooka zanu koma zigwiritseni ntchito ngati mwayi woti Mulungu aonetsera ukulu wake.
 - Kodi munachita bwino pati, motani, chifukwa cha chiyani? Nanga ndi zinthu ziti zomwe zakuthandizirani kuti muchite bwino.
 - Kodi ndi chiyani chomwe mukadakonda mutasintha? Anthu? Njira? Kapena dongosolo lenilenilo?
 - Nanga anthu omwe analipo anagwiritsidwa ntchito moyenera? Kodi ntchito zomwe anapatsidwa zimagwirizana ndi mphatso zawo zauzimu? Kodi amaoneka kuti anamvetsa cholinga cha dongosolo ndipo kuti analimbikitsidwa mokwanira kukwaniritsa dongosolo?

- Kodi mungagwiritse ntchito dongosololi kawirinso. Mpempheni Ambuye kuti akutsogolereni pa chiganizo chimenechi. Madongosolo ena atha kugwiritsidwanso ntchito kawiri, koma nthawi zina Mulungu amakhala ndi dongosolo latsopano.
- Kodi mwaphunzira chiyani chomwe chingakuthandizeni pamene mukhale mukukonza madongosolo ena mtsogolomu?

CHIFUKWA CHIYANI MADONGOSOLO AMAKANIKA

Madongosolo a Mulungu amakhala abwino nthawi zonse, koma popeza kuti amagwiritsa ntchito zotengeramo zofooka (anthu) madongosolo ena amakanika.

Mwachitsanzo:

- Munda wa Eden unali dongosolo la Mulungu pa munthu. Koma munthu analephera.
- Dongosolo la Mulungu pa Israel linali lakuti achitire umboni za Iye ku maiko a amitundu, koma Israel analephera.
- Dongosolo la Mulungu pa Mfumu Sauli, Samson, ndi ena linalilephera chifukwa chakuti anthuwa anali ndi zofooka zawo za umunthu.

Kulephera kumachitika nthawi zambiri chifukwa cha kusafuna kwa munthu kuti agwire ntchito mogwirizana ndi Mulungu.

Zina mwa zifukwa zomwe zimapangitsa kuti madongosolo akanike nazi:

1. Kusowekera kwa Masomphenya: Anthu sanamvetse cholinga kapena masomphenya omwe anali mu dongosolo lanu.
2. Kusowerekerera maphunziro: Mwina anthu sanaphunzitsidwe maluso ofunikira pa ntchito yomwe anapatsidwa ngati mbali imodzi ya dongosolo. Mulungu nthawi zonse amakonzekeretsa anthu pa ntchito yomwe akufuna atachita. Atsogoleri akuyenera kutengera chitsanzo chimenechi.
3. Kugwiritsa ntchito mphatso zauzimu molakwika: Anthu anaikidwa malo oti si awo. Mwachitsanzo, mwina munaika mlaliki pa udindo wa ubusa.
4. Kusakhala wokonzeka kulipira dipo: Anthu kapena utsogoleri umakana kudzipereka ku moyo wa pemphero, kupereka nthawi, mphamvu kapena chuma chimene chikusowekera kuti dongosolo likwaniritsidwe.
5. Kusowekera Pemphero: Mwina dongosolo linapangidwa popanda chitsogozo cha Ambuye.
6. Madongosolo Osamveka Bwino: Mwina dongosolo sinalembedwe momveka bwino.
7. Kusalumikizana: Mwina anthu omwe akukhuzidwa sanauzidwe za dongosolo momveka bwino.
8. Kusowekera kwa Kauniuni: Mwina palibe amene amadzaona momwe zinthu zikuyendera, ndiye mabvuto akadzuka, dongosolo lonse limakhuzidwa. Tsiku lomaliza kukwaniritsa dongosolo litafika palibe amene anali wokonzeka. Popeza kuti panalibe kuunikira, panalibenso kuthekera kothana ndi mabvuto omwe analipo.
9. Mantha: Kuopa kunenedwa, kulephera ndi kuopa anthu.
10. Kukaikira: Kukaikira kuthekera kwa Mulungu kugwira ntchito kudzera mwa inu.
11. Kuzengereza: Uku ndiko kuchedwetsa zinthu, kumangodikira. Kumangoti tikapeza nthawi kapena mwayi wina, masiku nkumapita osachita kanthu.

12. Kupeza zifukwa: Kupeza zifukwa zosagwirira ntchito m'malo mobvomereza ndi kukonza zinthu.
13. Ulesi: Kumangokhala osakhuzika nkomwe kuti pali zoti muchite.
14. Kudzikonda: Mukuyenera kudzipereka nokha kuti muthe kukwaniritsa zinthu. Kudzikonda ndi kukhala munthu waumbombo ndi zosathandiza. Mukhale ndi mtima wamataya.
15. Kusowa kwa umodzi: Aliyense kumachita zinthu payekha m'malo mogwira ntchito limodzi kuti mukwaniritse cholinga ndi dongosolo la Mulungu.
16. Kusamvera: Anthu sanamvere iwo amene anali m'maudindo akuluakulu.
17. Kukanika kusintha dongosolo: Dongosolo silinasinthidwe monga momwe limafunikira. Kukhala kuti ulendo wapitawu zinayenda bwino sizitanthauza kuti ulendo uno ziyendanso bwino m'dongosolo la Mulungu.
18. Kulephera kuphunzira kuchokera ku zolephera za m'mbuyo: Kulakwitsa sikumatha ngati anthu akukanika kuunikira dongosolo ndi kuphunzira ku zolakwika za m'mbuyo.
19. Kukhala wopanda chidwi ku tsatanetsatane wa zinthu: Nthawi zambiri dongosolo limakhala ndi tsatanetsatane wa zinthu zambiri. Ndipo ngati zimenezi sizionedwa bwino, dongosolo limakanika.
20. Kukana kutumikira modzichepetsa: Munaitanidwa kuti mukatumikire ena. Mukaiwala chinthu ichi nimukhala munthu wadzikweza, dongosolo limakanika kukwaniritsidwa.
21. Maganizo olakwika okhuzana ndi kukonza dongosolo: Izi zimaonekera pamene anthu ayamba kulankhula mau ngati awa:
 - "Timachita zimenezi nthawi zonse."
 - "Ife zomakhala ndi ndongosolo si kwenikweni."
 - "Zomakonza madongosolo siziri m'Malemba."
 - "Izi zakhala zikugwira ntchito kwa zaka 40 tsopano."
 - "Ife timayendera chikhulupiriro osati madongosolo."
 - "Tiribe nthawi yomakhala pansu nkumati tikukonza dongosolo."
 - "Sindikuona chifukwa choti tisinthire zinthu, lero lokha latani?"
22. Kusowekera utsogoleri woyenera: Kutu dongosolo litheke limafunika utsogoleri wamphamvu.
23. Kusowekera kwa ndalama.
24. Kusowa kwa ogwira ntchito kuti dongosolo litheke.
25. Kukanika kukhala owona mtima nthawi ya kuunikira zinthu.
26. Mphamvu za mdani: Satana nthawi zonse amafuna kukulepheretsani kukwaniritsa cholinga chanu.
27. Kudandaula: Mukayamba kukonza kapena kukwaniritsa dongosolo la Mulungu, mumayenera ndithu kuti mudutse m'masiteji odziwikiratu.

Mwachitsanzo, mu Mpingo woyamba:

 - Machitidwe 1: Mulungu anasankha amuna ena.
 - Machitidwe 2: Anthuwo anawapatsa utumiki.
 - Machitidwe 3: Panali kuchurukana.
 - Machitidwe 4: Mpingo unayamba.
 - Machitidwe 5: Kudandaula kunayambika

Nkhani yomweyi imapezekanso mu bukhu la Nehemiya:

- Nehemiya 1: Mulungu anasankha munthu.
- Nehemiya 2: Munthuyo anampatsa utumiki.
- Nehemiya 2-3: Ogwira ntchito anachuruka.
- Nehemiya 2-4: Dongosolo linakhazikitsidwa.
- Nehemiya 5: Kudandaula kunabuka pakati pa anthu.

Madongosolo ndi mautumiki akafika pa siteji yodandaula, mukuyenera kuthana ndi bvutolo, mukapanda kutero dongosolo lanu silitheka. Nehemiya anathana ndi kudandaula kudzera m'pemphero ndi kuika bwino zinthu m'malo (Nehemiya 5).

Ndipo atumwi anathana ndi kudandaula kudzera m'pemphero ndi kuika bwino zinthu m'malo (Machitidwe 6).

Kudandaula kwa ana a Israel sikunatheretu kwatunthu. Chifukwa cha ichi, dongosolo la Mulungu linachedwetsedwa kufikira m'badwo watsopano unadzuka.

KUGWIRITSA NTCHITO ZOTSATIRA ZA KUUNIKIRA NTCHITO

Mutha kugwiritsa ntchito zotsatira za kuunikira kwanu mu njira zingapo:

1. Kuunikira zinthu kumabvumbulutsa zofooka mu zokhumba. Mumasintha ndi kukonzanso madongosolo omwe alipo kale kuti mukonze zofookazo.
2. Mumakhala mukukonza madongosolo atsopano pamene akale aja akufika kumapeto.
3. Mumaphunzira kuchokera ku zomwe munachita bwino. Mulungu atha kukutsogolerani kubwereza dongosolo lomwe lachita bwino.
4. Mumaphunzira kuchokera ku zomwe mwalakwitsa. Mumadziwa chifukwa chomwe chakulepheretsani kuchita bwino ndi kukonza zinthu musabwerezenso zomwe munalakwitsazo.

NTCHITO YOPITILIRA

Kukonza dongosolo ndi ntchito yomwe ndi yopitilira. Mukakonza dongosolo, mumalikwaniritsa, kuliunikira, ndi kupanganso dongosolo lina. Ngati mukufuna kuchita bwino mu utumiki, mukhala mukupitiriza kuchita zinthu motere kufikira cholinga chanu chitakwaniritsidwa mpaka cholinga cha moyo wanu chitakwaniritsidwa.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osaonera.

2. Perekani tanthauzo la mau oti “kuunikira ntchito.”

3. Chifukwa chiyani kuunikira zinthu nkofunika?

4. Lembani masitepe okhazikitsira ndondomeko za kuunikira.

5. Lembani zifukwa zosachepera zisanu zomwe zimapangitsa anthu kulephera kukwaniritsa dongosolo.

6. Lembani njira zinayi za momwe mungagwiritsire ntchito zotsatira za kuunikira.

7. Unikirani madongosolo ena omwe mwakwaniritsa. Gwiritsani ntchito zotsatira za kuunikirazo kuti mukonzenso madongosolo omwe alipo kale komanso kukonza madongosolo atsopano.

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto a bukhu lino)

KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

1. Werengani Yohani 17. M’pempheero ili, Yesu anaukira utumiki wake wa pa dziko lapansi.
2. Mu Chipangano Chakale, Mulungu anapereka ntchito kwa Nehemiya yomanganso linga la Yerusalemu. Anatenga nthawi kufufuza zofunika, kuika zokhumba, ndi kukwaniritsa dongosolo. M’mene amapitiriza, amakhala ndi nthawonso youkinikira ntchito kuti aone momwe zinthu zikuyendera nathana ndi mabvuto omwe amadzuka mkatimkati. Mabvutowa anali monga kusagwirizana, kusowa kwa mphamvu ndi masomphenya, komanso zolimkana za adani. Utsogoleri weniweni umaonekera pamene wakwaniritsa dongosolo ndi zokhumba zomwe zinaikidwa. Kwa Nehemiya, nkhani imati, “Ndipo linga linatha kumangidwa” (Nehemiya 6:15).
3. Nkhani ya Mfumu Hezekiya imaonetsanso kufunika kwa kuyendetsa bwino mwa zolinga. Imaphatikizapo kauniuni wa zozungulira utumiki wanu, kukonza madongosolo, kukwaniritsa madongosolo, ndi kuunikanso ntchito yomwe yachitika. Yambani mwawerenga kaye nkhani ya Mfumu Hezekiya pa 2 Mafumu 16-20 ndi 2 Mbiri 28-32.

ZOMWE ZIMACHITIKA

Hezekiya anachokera kwa mfumu yoipa yotchedwa Ahag. Mafumu a Yuda ndi Israel anali ogawikana komanso pa udani. Fuko la Yuda linali laling’ono kwambiri pa mafuko onse koma linali patsogolo pa nkhani za kutsata njira za Mulungu. Mafuko ena khumi ndi limodzi anabvomereza zipembedzo za chikunja za maiko owazungulira. Hezekiya ndiye anali mfumu ya Yuda. Mdani wawo wamkulu linali dziko la Asiriya. Dzikoli linali lamphamvu koposa mu nthawi ya Hezekiya pa dziko lonse lapansi ndi la chipembedzo cha ziwanda.

Zabwino za Hezekiya

1. Wolimba mtima komanso woona mtima pamaso pa Mulungu.
2. Munthu wokhala panso pa ulamuliro komanso wa ulamuliro.
3. Wachifundo
4. Amadziwa ndi kukhulupirira kupemphera
5. Amasunga mau ake.
6. Amaika patsogolo chiyero chake.

Mabvuto a Hezekiya

1. Anazunguliridwa ndi adani ambiri naposedwa mphamvu.
2. Anali pa ya kudzitamandira.
3. Anali wakhama pa ndale.

Cholinga cha Hezekiya: Kulunzanitsa Israel yense ngati dziko limodzi panso pa Mulungu m’modzi woona.

Zokhumba za Hezekiya:

1. Kukonza kachisi
2. Kubwezeretsa utsogoleri woopa Mulungu.
3. Kubwezeretsa kutumikira mnyumba ya Mulungu.
4. Kukhazikitsanso Pasaka

5. Kumanga ngalande za madzi mu mzinda wa Yerusalemu.
6. Kuthana ndi malimba a mdierekezi pa dziko lomwe Mulungu anapereka kwa Israel.

Dongosolo lake:

Ili ndi dongosolo lomwe anaika m'malo kuti akwaniritse zokhumba zake:

1. Anabweretsa pamodzi anseme ndi Alevi kuti akonze Kachisi ndi kumuyeretsa.
2. Anakhala chitsanzo chabwino kwa olamulira potsatira zonse zomwe Mfumu Davide anachita.
3. Analimbikitsa Alevi ndi ena onse pamene amamanganso Kachisi.
4. Anapangitsa Pasaka woyamba patadutsa zaka 260.
5. Anaitanitsa onse okhulupirira kuchokera ku Israel yense kudzakhala nawo pa Pasaka.
6. Anapereka zakudya za ku mwambowu.
7. Anapemphera chikhululukiro cha pa anthu a Mulungu.
8. Analimbikitsa gulu la asilikari mwa mphamvu ya Mzimu Woyera ndi kulalikira Mau a Mulungu.
9. Anagwiritsa ntchito chuma cha ku nyumba ya ufumu kumangira ngalande za madzi mu Yerusalemu.

Kuunika Nthito

Hezekiya anakwaniritsa zokhumba zake. Anakhala nazo nzeru za kudzichepetsa pamaso pa Mulungu nalapa pokhala wodzikuzana ndi wakhama pa ndale. Analapa chifukwa cha maubale amseri ndi adani a Mulungu, ngakhale tchimo lake linabweretsa mabvuto aakulu pa mibadwo ya mtsogolo (2 Mafumu 20:16-18). Mwa zonse, Hezekiya anakhala m'gulu la mafumu atatu a Israel omwe anachita zazikulu.

ZOONJEZERA 1

MAU A CHIKHULUPIRIRO CHA MPINGO

Mwaphunzira kale kuti Mau a Chiphunzitso cha Mpingo ndi osiyana ndi Mau a Cholinga cha Mpingo. Mau a Cholinga cha Mpingo amafotokozerwa chifukwa chimene utumiki wanu ulipo. Pamene Mau a Chiphunzitso cha Mpingo amafotokozerwa zomwe mpingowo umakhulupirira. Imapereka chithunzithunzi cha pomwe inu mwakhazikikapo kumbali ya chiphunzitso ngati mpingo zomwe zimaonekera pa zophunzitsa, zolalikira, ngakhale utumiki wanu. Onani chitsanzo ichi:

HARVESTIME INTERNATIONAL NETWORK

Mau a Chiphunzitso cha Utumiki

Cholinga ndi zokhumba za utumiki wa Harvestime International Network zimakhazikika pa mfundo zauzimu za kholola molingana ndi Mau a Mulungu. Mau a Chikhulupiriro cha utumikiwu amatsindika masomphenya awa:

MAU A MULUNGU

Mbeu

Mbeu ndi Mau a Mulungu... (Luka 8:11)

Malemba a m'Chipangano Chakale ngakhale Chipangano Chatsopano ndi Mau a Mulungu oona, maziko a chikhulupiriro cha Chikristu, kumvesetsa, moyo ndi utumiki. Mau a Mulungu alibe banga ndipo sakuyenera kuonjezedwa, kuchotseredwa, kapena kusinthidwa ndi miyambo kapena kuti wina akalandira bvumbulutso.

Kwa muyaya, Ambuye, Mau anu anakhazikika Kumwamba.

Mau anu aikika kumwamba kosatha, Yehova (Masalimo 119:89)

UTATU WA MULUNGU

Ambuye wa Kholola

Kotero pemphani inu kwa Mbuye wa Kholola (Mateyu 9:38)

Utatu wa Mulungu uli ndi Mulungu Atate, Mulungu Mwana, ndi Mulungu Mzimu Woyera.

Pakuti pali atatu akucita umboni, Mzimu, ndi madzi, ndi mwazi; ndipo iwo atatu ali mmodzi (1 Yohane 5:8)

MULUNGU TATE

Kuli Mulungu m'modzi, wopanda malire, wamuyaya ndi wangwiro, Mlengi wa Kumwamba ndi Dziko lapansi:

Pakuti atero Yehova amene analenga kumwamba, Iye ndiye Mulungu amene anaumba dziko lapansi, nalipanga; Iye analikhazikitsa, sanalilenga mwacabe; Iye analiumba akhalemo anthu; Ine ndine Yehova; ndipo palibenso wina. Yesaya 45:18

MULUNGU MWANA: YESU KHRISTU

Yesu Khristu anakhala ndi kubadwa mwa Maria namwaliyo kudzera mu mphamvu ya Mzimu Woyera. Iye anakhala nsembe yangwiro yolipira tchimo la mtundu wa anthu kudzera mu imfa yake ndi kukhetsa mwazi wake.

Anauka kwa akufa m'thupi lake la ulemelero, anaonekera kwa ochuruka, nakwera kumwamba, ndipo adzabweranso ku dziko lapansi mu mphamvu ndi ulemelero. Iye tsopano ndi mutu wa thupi lake, Mpingo, naposa mphamvu zonse za ku mdima, ndipo ali ku dzanja lamanja la Mulungu napembedzera oyera mtima onse:

Mwa icinso Mulungu anamkwezetsa iye, nampatsa dzina limene liposa maina onse, 10kuti m'dzina la Yesu bondo liri lonse lipinde, la za m'mwamba ndi za padziko, ndi za pansu pa dziko, 11ndi malilime onse abvomere kuti Yesu Kristu ali Ambuye, kucitira ulemu Mulungu Atate. Afilipi 2:9-11

MULUNGU MZIMU WOYERA:

Mzimu Woyera anauzira Mau a Mulungu, nadzodza Yesu Khristu pa utumiki wake, nadzadza mpingo ndi mphamvu ya Pentekosite, ndipo adzasandulitsa matupi akufa a okhulupirira mu ulemwero wa chiukitso.

Mzimu Woyera amatsutsa dziko pa uchimo, chilungamo ndi chiweruzo, amalumikizitsa Yesu Khristu m'chikhulupiriro, napangitsa kubadwa mwatsopano, ndi kukhazikika mwa okhulupirira.

Ubatizo wa Mzimu Woyera waperekedwa kwa onse okhulupirira mwa Khristu Yesu ndipo umaonekera kudzera mkukhala wochitira umboni wamphamvu wa Ambuye wathu woukitsidwa komanso ndi zizindikiro zotsimikizira za Machitidwe 2-4

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko Machitidwe 1:8

Mphatso za Mzimu Woyera zaperekedwa kwa okhulupirira kudzera mu utumiki wa Mzimu Woyera, yemwe amapereka kwa yense amene amfuna:

Koma zonse izi acita Mzimu mmodzi yemweyo, nagawira yense payekha monga afuna 1 Akorinto 12:11

Mzimu Woyera amathandiziranso kuthekera kwa chipatso cha Mzimu, kuti wokhulupirira akule m'chiyeretso:

Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, icikhulupiriro, 23cipatso, ciletso; pokana zimenezi palibe lamulo. Agalatiya 5:22-23

MUNTHU

Wofesa Mbeu

Mverani: Taonani; wofesa anaturuka kukafesa (Marko 4:3)

Munthu analengedwa ndi m'chikhalidwe ndi m'chifanizo cha Mulungu. Kudzera mu tchimo loyamba la Adam ndi Hava, anthu onse anakhala wochimwa mwa chikhalidwe chawo.

Munthu payekha alibe kuthekera kobwelera kwa Mulungu, ndipo ndi wotayika ndi wopanda chiyembekezo popanda chipulumutso cha mwa Khristu Yesu:

Koteronso kwalembedwa, 11 Munthu woyamba, Adamu, anakhala mzimu wamoyo. 12 Adamu wotsirizayo anakhala mzimu wakulenga moyo. 46Koma cauzimu siciri coyamba, koma cacibadwidwe; pamenepo cauzimu. 1 Akorinto 15:45-47

CHIPULUMUTSO

Kholola

Ndipo iye amene afesedwa pa nthaka yabwino, uyu ndiye wakumva mau nawadziwitsa; amene abaladi zipatso, nazifitsa, ena za makumi khumi, ena za makumi asanu ndi limodzi, ena za makumi atatu. Mateyu 13:23

Chipulumutso ndi mphatso ya Mulungu kudzera m'chisomo ndi chikhulupiriro cha mwa Khristu Yesu. Palibe dzina lina kupatula la Khristu limene munthu angapulumsidwe nalo.

Munthu amabadwa mwatsopano pamene watumbenuka kuchoka ku uchimo, naonetsera chipatso cha kutembenuka mtima, ndi kukhulupirira mwa Khristu ndi mu imfa yake yofera machimo.

Kudzera mu ntchito ya chiombolo chikhulukiro chimapezeka, kumasulidwa ku ukapolo wa dziko, ndi ufulu mwa Mzimu wa Mulungu.

Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiriro, ndipo ici cosacokera kwa inu: ciri mphatso ya Mulungu; 9cosacokera kunchito, kuti asadzitamandire munthu ali yense Aefeso 2:8-9

MPINGO

Ogwira Ntchito M'munda

Chifukwa chace pempherani kwa Mwini zotuta kuti akokose antchito kukututa kwace Mateyu 9:38

Mpingo ndilo thupi ndi mkwatibwi wa Khristu. Ntchito yaikulu ya mpingo ndiyo kukaphunzitsa maiko onse ndi kuwapanga kukhala ophunzira, kutengera Uthenga Wabwino ku maiko kwa anthu onse ndi zizindikiro zotsatirapo:

Ndipo ananena nao, mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse. 16Amene akhulupirira nabatizidwa, adzapulumutsidwa; koma amene sakhulupirira adzalangidwa. 17Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano Marko 16:15-18

PACHIMAKE

Kholola Lomaliza

Ndipo mngelo wina anaturuka m'Kacisi, wopfuulandi mau akuru kwa iye wakukhala pamtambo, Tumiza zenga lako ndi kumweta, pakuti yafika nthawi yakumweta; popeza dzinthu za dziko zacetsa Chibvumbulutso 14:15

Chimake chenicheni cha zinthu chidzafika pamene Yesu Khristu adzaonekera mu ulemelero wake, akufa adzaukitsidwa, ndi kusandulizidwa kwa amoyo mwa Khristu kunka ku chiweruzo cha olungama ndi osalungama. Ndipo Satana ndi amithenga ake onse pamodzi ndi onse ali kunjira kwa Khristu adzasiyanitsidwa ndi Mulungu nalowa m'chilango chosatha pamene iwo owomboledwa adzalowa m'chikondwerero cha muyaya cha Mulungu:

Koma sitifuna, abale, kuti mukhale osadziwa za iwo akugona; kuti mungalire monganso otsalawo, amene alibe ciyembekezo. 14Pakuti ngati tikhulupirira kuti Yesu adamwalira, nauka, koteronso Mulungu adzatenga pamodzi ndi iye iwo akugona mwa Yesu. 15Pakuti ici tinena kwa inu m'mau a Ambuye, kuti ife okhala ndi moyo, otsalira kufikira kufikanso kwa Ambuye, sitidzatsogolera ogonawo. 16Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mpfuu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka; 17pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse. 2 Atesalonika 4:13-17

Ndipo ndinaona akufa, akuru ndi ang'ono alinkuima ku mpando wacifumu; ndipo mabuku anatsegulidwa; ndipo buku lina Iinatsegulidwa, ndilo la moyo; ndipo akufa anaweruzidwa mwa zolembedwa m'mabuku, monga mwa nchito zao Chibvumbulutso 20:12

ZOONJEZERA 2 MAU A CHOLINGA

Mphuziroli mwaphunzira kalembedwe ka mau a cholinga. Mau a cholinga a Harvesttime International Network anaperekedwa mu chaputala 3 ngati chitsanzo. Pano pali zitsanzo zina zoti tizionenso bwino. Mau amenewa analembedwa ndi mipingo yosiyanasiyana akufotokoza m'mene cholinga chawo chiriri mudongosolo la Mulungu.

SANFRANCISCO CHRISTIAN CENTER: MAU A CHOLINGA

Mau a cholinga cha Sanfrancisco Christian Center ndi kulemekeza Mulungu ndi...

1. Kudziwitsa cholinga chaumulungu polalikira uthenga.
2. Kuphuzitsa gulu la okhulupirira amene amavetsetsa malemba; amene makulidwe a moyo waWo wa uzimu akuwoneka ndi moyo komanso khalidwe la Kristu; komaso amene anadzipereka kufalitsa uthenga wa Mulungu.
3. Kulimbikitsa amai ndi abambo kuti azindikire, akuze, ndi kugwiritsa ntchito Mphatso zao mufumu wa Mulungu.
4. Kulalikira anthu osatembenuka kuti afikile chidziwitso chopulumutsa cha Kristu Yesu (mdera lawo komanso kunjia).
5. Kupulumutsa anthu powapatsa zinthu zofunika kuthupi, chikhalidwe ndi maganizidwe awo.

LOCAL CHRISTIAN FELLOWSHIP: MAU A CHOLINGA

Choling cha Local Christian fellowship ndi kukulitsa thupi la Kristu (mpingo). Tifuna kugonjera kuulamuliro wa Ambuye Yesu Kristu m'zinthu zonse, kutengera m'mene mpingo wa chipangano chatsopano umapangira, ndikudzipereka, kudzera mphavu ya Mzimu Woyera:

1. Kulalikira osapulumsidwa kuchikhulupiro chopulumutsa mwa Yesu Kristu.
2. Kugwiritsa ntchito uthenga opulumutsa wa Yesu Kristu ku zinthu zonse zapa umunthu ndi machimo, matenda komaso zovuta.
3. Kubweretsa moyo ndi khalidwe la Kristu owukitsidwa.
4. Kuphuzitsa ma membala kutulutsa mwa iwo unthuthu wa makulidwe.
5. Kuphuzitsa atsogoleri a Uzimu amene akhoza kuchulukana okhaokha ndi kufikira zosowa za ena.
6. Kulambira ndi kulemekeza Mulungu mwaufulu wa Mzimu Oyera kudzera munkupembeda kwa pagulu kapena mseli.
7. Kuzindikiratsa, kukulitsa ndi kutuma anthu amene Mzimu waitana kuti awatumikire.

MPINGO WA FIRST FOURSQUARE: MAU A CHOLINGA

Cholinga cha mpingo wa First Foursquare ndi kudzutsa ntundu wa anthu achikhulupiriro ndi kutulutsa kudziko ulemmerero wa ufumu wa Mulungu pokhala chitsanzo cha utumiki wa Yesu Khristu.

Tidzadalira mphavu ya Mzimu Woyera ndi kugwiritsa ntchito chirichonse mu utumiki okhazikika pa Khristu;

Kulambira

1. Kudzutsa ntundu wa olambira Mulungu wa moyo, kulemekeza Mwana wake, Yesu Kristu, ndikulemekeza Mzimu Woyera.

Mau

2. Kulalikira uthenga ndi kuphuzitsa Mau a Mulungu ndikupanga malo amene anthu azikumana ndi chisomo cha Mulungu.

Kuphunzira Utumiki

3. Kuphuzitsa anthu amene azindikire maitanidwe awo ndi agulu mwa Kristu. Kuwathandiza kuzindikira, kukuza, ndi kupereka kuthekera kwao kwa utumiki.

Kusala kudywa ndi Kupephera

4. Kusungabe mwambo nkupemphera ndi kusala kudywa paokha komanso ndi anthu ena zimene ziri zogwirizana ndi mawu a Mulungu. Kupembedzera kuchotsa mphavu zaku gahena zimene zikulamulirabe zochitika pakati pa anthu...ngati munthu, mdela lake, mziko ndi m'maiko ena onse.

Kufalitsa Uthenga

5. Kulimbikitsa a Kristu kukonda anthu ndi kudzipereka ku ntchito imene Yesu anapereka; ya kukonzekeretsa magulu onse kuti azigawa mawu a Mulungu bwino ndi umboni wao; kupereka nthawi yao, maluso, ndi zinthu zina kuti afikire zofunika za anthu mdela lawo.

Umodzi wa Okhulupirira

6. Kugwira ntchito m'chijanano cha okhulupirira mwa Yesu Khristu.

Chuma

7. Kulimbikitsa okhulupirira kuti akhale adindo okhulupirira ndikugwiritsa ntchito zimene munthu anapereka kuti apititse patsogolo zolinga.

ZOONJEZERA 3

MAIKIDWE A ZINTHU MCHIMAKE

Chigawo ichi chiri ndi uthenga wamaikidwe a zinthu mchimake a mumpingo

MAPEPALA A MALAMULO:

Mpingo siwochitira malonda. Ndi utumiki. Koma chifukwa cha malamulo a dziko, mipingo imayenera kuyendetsedwa mokhalika ngati magulu a malonda.

Mukayamba mpingo watsopano, fufuzani kuti kumbali ya malamulo chimafunika ndi chani kumbali ya dziko. Mayiko, mizinda, ndi zigawo amakhala ndi malamulo osiyanasiyana.

Maiko ena alibe zoyenera pamene maiko ena ali ndi malamulo okhwima.

1. Kodi ndichoyenera kuchita kalemba wa mpingo ndi mboma?
2. Kodi mumafunika chilolezo cha boma kuti muyendetse mpingo?
3. Kodi pali malamulo akuti misonkhano mumpingo wanu ikuyenera kuchitika kuti?
4. Kodi mukuyenera kumaliza (form) kuti musamalipira misonkho pa Katundu amene mulinaye?
5. Kodi mukuyenera kupereka tsatanetsatane wa m'mene mwayendetsera zinthu chaka chikamatha ku boma?
6. Kodi mukufunika malamulo olembedwa kapena (by laws for the church)? Ngati ndi choncho boma kapena likulu la mpingo wanu liyenera kunena chimene chiyenera kuchitika)

Ngati ziri zotheka kwaniritsani zonse zimene boma limafuna. Koma ngati boma silimalola kufalitsa uthenga wabwino kapena mipingo, sizikuyenera kukukhazikani pansu. Mukuyenera kuchita zinthu mobisa ngakhale kuti simunaloledwe. (Onani Mac. 4:16-20; 5:29).

ZOYENEREZA KUKHALA MEMBALA

Ngati munthu anabadwadi mwatsopano, amalowa mgulu la thupi la khristu m'dziko lonse lapansi.

Koma magulu ena a okhulupirira amasankha kukhala ndi zimene zimayenera anthu kukhala ma membala a m'matchalitchi. Kodi mpingo:

1. Chiyanjano, chimene onse amene anabadwadi mwatsopano amakhala mbali imodzi: Palibe njira yokhazikika yokhalira membala?

KAPENA NDI.....

2. Khalani membela okhazikika: Pamene okhulupirira amafunsa chilolezo chokhala membala m'gulu la m'dela lanu.

Mipingo imene inapanga ziyenera zokhala ndi ziyenera amawonjezera zina mwaziwonjezero izi kapena zonse:

-Kubandwa mwatsopano

- Ubatizo wa madzi
- Ubatizo wa mzimu woyenera
- Kugwirizana ndi mawu a chiphuzitso, ndi mau a cholinga a mpingo wa m'dela lanu.
- Lonjezo lothandiza mpingo mwakupezeka, maluso awo, chakhumi ndi chopereka.

DONGOSOLO LA NDALAMA (BAJETI):

Pa dongosolo lirironse munaphuzira kapangidwe ka bajeti yake. Kuwonjezera apo munaphuziranso kapangidwe ka madongosolo anu ngati munthu, kuti muyendetse mpingo mumafunika kuwonetsa ndandanda wa m'mene mugwiritsire zinthu zanu.

Mukangoyamba mpingo wanu, mumafunika ndalama kuti muchite izi:

1. Muthandize mbusa.
2. Kulipira malo amene mpingo mumakumanapo.
3. Kulipira magetsi, madzi, ndi zina zofunika.
4. Zida zamaphunziro (Baibulo, uthenga wa m'mapepala, ndi zipangizo zophuzitsira).
5. Zida za mayimbidwe, gome, mipando ndi zina zimene zingafunike.

Pamene mpingo ukukula mukhoza kukhala ndi zofuna zina. (Onani mndandanda uli pa lipoti ya kagwiritsidwe ntchito ka chuma imene iri m'musimu.

Ndimaganizo abwino kuti ma membala a mpingo kudziwa m'mene chuma cha mpingo chimagwirira ntchito. Onani chitsanzo cha repoloti ya kagwiritsidwe ka chuma pa tsamba lotsatirari imene mukhoza kuigwiritsa ntchito popanga lipoti yanu.

Dzina la Mpingo kapena

Lipoti ya chuma

Mwezi _____ Chaka _____

Kukonza ndi: _____

Sayini ya munthu olemba lipoti)

Ndalama zoyamba nazo: K_____ (Lembani ndandanda wa ndalama zimene munali nazo koyambilira kwa mwezi).

Malisiti

(Lembani ndalama zimene zinapezeka pa njira ina iriyonse)

1. K_____ Chopereka
2. K_____ Ndalama zopezeka mutagulitsa mabuku
3. K_____ Zochitika zopezera chuma
4. K_____ Zina

Zonse: _____

Tsamba lachiwiri lipoti la zachuma

Zimene munagwiritsa ntchito:

(Lembani mndandanda wa m'mene munagwiritsira ntchito. M'musimu muli magawo ena amene mukhoza kugwiritsira ntchito).

1. K_____ Obweretsa zinthu ku ofesi
2. K_____ Kukonzanso, zinthu zokozerera pa malo.
3. K_____ Zinthu zophuzitsira (Baibulo mathiraki ndi maphunziro ena)
4. K_____ Zipangizo zoverela komanso zowonerera (tape, filimu, nyinbo ndi zina)
5. K_____ Kufalitsa (Missions)
6. K_____ Malipiro a ogwira ntchito
7. K_____ Malipiro a malo a tchalitchi
8. K_____ Malipilo a (Madzi, magetsi ndi zina)
9. K_____ Makalata
10. K_____ Ngongole
11. K_____ Chopereka cha padera cha Olalikira oitanidwa
12. K_____ Zolengezetsa
13. K_____ Insurance (Pa Katundu wa mpingo)
14. K_____ Printing
15. K_____ Zinga

Zonse zimene munagwiritsa ntchito: K_____

Zotsala: K_____

Umu ndi m'mene mungapezere ndalama zotsala:

1. Lembani zimene munayamba nazo.
2. Phatikizani ndalama zonse pa ma licit.
3. Kuchokela kuzimene mupeze chotsani zimene munagwiritsa ntchito
4. Zikupatsani ndalama zotsala

KUPANGA MISONKHANO

Utumiki kuti uyende bwino umafunika misonkhano yambirimbiri kuti mupange dongosolo, kuika zinthu m'malo ake, kupeza mayankho a Mavuto, ndi kupanga kawuniwuni.

Sitingakambirane ntundu wina uliwonse wa misonkhano umene mukuyenera kukhala nawo, koma pali akalozera a misonkhano iriyonse ngakhale ya malonda.

1. Khalani ndi cholinga cha msonkhano: ndichifukwa chani tikuyenera kukumana? Cholinga chanu ndi chani? Mukufuna kukwaniritsa chani? Zolinga zina za misonkhano ndi:
 - Kupanga madongosolo
 - Kupeza mayankho a mavuto
 - Kupanga zisankho zimene zikufunika
 - Kupanga kawuniwuni
 - Kuwuza anthu zochitika kapena zinthu zimene akuyenera kudziwa.
 - Kukonzekera chochitika china.
 - Kukambirana za dongosolo la zachuma
 - Kukambirana zinthu zina monga m'mene mumachitira nthawi zonse.
 - Kusungitsa mwambo mumpingo.
2. Pangani cholinga cha msonkhano:
 - Lembani ndandanda wazokambirana poyambira chofunika kwambiri.
 - Mukuyenera kuphatikizapo nthawi yapemphero kuti mupeze chitsogozo cha Mulungu.

3. Pangani ndandanda wa zonse zofunika pa msonkhano. Zikhoza kukhala zinthu monga pensulo, pepala, reporoti, zowonetsera, zitsanzo, ndi zina. Bweretsani zinthu zonse pamodzi nthawi ya nsokhano isanakwane.
4. Ikani tsiku, nthawi, ndi malo a msonkhano.
5. Dziwitsani anthu amene mufuna kuti adzapezeke pa msonkhano. Apatseni tsiku, nthawi, malo ndi cholinga cha msonkhano. Wina aliyese adziwitsidwe ngati akuyenera kubweretsa china chirichonse, chitsanzo, zodziwitsa, reporoti, chimangirizo cha m'mene zinthu zikuyendera.
6. Yambani ndi kumaliza msonkhano wanu nthawi yabwino.
7. Khalani ndi wapampando amene atsogolere msonkhano.
8. Khalani ndi njira yoyamkhulira: Kodi anthu aziyimika manja awo ndi kuitanidwa dzina ndi mtsogoleri, kodi aliyese aziyankhula m'mene angayankhulire.
9. Khalani ndi njira yopangira zisankho. Kodi mupephera mpaka mutagwirizana? Kodi abusa ndi atsogoleri ena awuzimu azipanga zisankho atava kumbali zonse?
10. Imani pa cholinga. Musasokonezedwa ndi zokambirana.
11. Lembani zisankho zimene mwapanga pa msonkhano, makamaka pa zimene zikuyenera kuchitika nanga ndindani nanga liti. Mukamaliza msonkhano lembaniso zimene munalemba molongosola ndipo gawani pepala lake kwa wina aliyese amene anabwera ku msonkhano. Izi zikuthandizani kukumbukira ntchito imene apatsidwa kuti akwaniritse.

TIMAKALATA ZODZIWITSA ZA MPINGO WANU

Ngati nkotheka komanso ngati chuma chingalole, mutha kufuna kubweretsa pamodzi zithu zimene zingafotokoze mwachidule mpingo wanu kwa alendo ndi anthu am'madera ozungulira. Muphatikize mau ngati awa:

“(Timakalata iti tinapangidwa kuti tifotokoze mwachidule “dzina” mpingo. Tikukhulupirira kuti uthenga uwu ukuthandizani kupeza malo awutumiki ndi chiyanjano mumpingo uno. Kwa inu amene simuli ochitachita, tikukuitanani kuti mugwirizane nafe mu chiyanjano cha Ufumu wa Mulungu.

Khalani otsimikizika kuonjezera gawo la mau a cholinga ndi mau a chimphuzitso kuti anthu adziwe chifukwa chani mulipo ngati mpingo ndipo mumakhulupirira chani. Mukhozanso kuwonjezera uthenga wa abusa ndi zochitika zosiyanasiyana amene pa tchalitchi panu amachitika.

Apa pali mau amodzi amene mukuyenera kuonjezera:

Kwa onse amene akulira ndipo afunika chitonthonzo; kwa onse olema ndi othodwa; kwa onse osowa abwezi ndipo afuna abwezi; kwa onse amene ali okha ndipo afuna anza; kwa onse ochimwa ndipo afuna mpulumutsi; ndi kwa “wina aliyense amene” makomo a tchalitchi atsekulidwa ndikunena kwa inu m'dzina la ambuye Yesu Khristu “mwalandiridwa”

ALENDO:

Atsatileni alendo onse amene abwera kumwambo wa mapemphero. Cholinga chanu ndi chowabweretsa kwa Ambuye ndikuwapanga kukhala ma membala ochitachita a tchalitchi.

Khalani ndi mlendo aliyense kumalizitsa kadi yokhala ndi uthenga othandiza kulumikizana ndi utumiki.

M'musimu muli chitsanzo cha kadi:

CHITSANZO CHA KADI LA KALEMBERA:

Dzina _____

Adiresi _____

Nambala ya Foni _____

Maina ndi zaka za ana

Dzina	Zaka
_____	_____
_____	_____
_____	_____
_____	_____

___ Ndinabwera _____ ku tchalitchi _____

(Dzina la tchalitchi) (Mzinda)

___ Ndiribe mpingo wa ku mudzi

Pemphererani pepho iri:

___ Ndingakondwere nditamalumikizana ndi abusa.

Nthawi yabwino kuimba ndi: Tsiku: _____ Nthawi: _____

___ Ndine okondweretsedwa kukhala mbali imodzi ya chiyanjano cha mpingo.

ZOONJEZERA 4

KULOGOSOLA ANTHU MUTUMIKI

Mphuziroli munaphunzira kuti ndizofunika kulongosola anthu ndikugawa ntchito ngati mungakwaniritse madongosolo awutumiki. Njira imodzi yolongosolera anthu ndi kulemba cholinga chofotokoza ntchito kapena utumikiki umene apatsidwa. Pofotokoza muyenera kuonjezera izi:

1. Mutu wa utumiki.
2. Cholinga cha undindo; Lembani mau a cholinga kuti chifukwa chani utumiki ulipo.
3. Ntchito ya utumiki. Yankhani mafuso awa; -Kodi ntchito yanga ndi chani? -Ndi mphavu yanji ndiri nayo?
-Kodi ndimayang'anira ndani pa chitsogozo (amayang'anira ndani)?
-Amayang'anira kwa ine ndani pa chitsogozo (Ndimayang'anira ndani)?
4. Ubale wa undindowu. Ndi udundo wa ndani?. Amamupatsa malangizo ndani? Amapanga kawuniwuni ndani?
5. Zoyenera munthu amene akuyenera kutenga udindowu

Tawonjezera chitsanzo cha mafotokozedwe a ntchito ya mawundindo osiyanasiyana amene atha kufunika mu tchalitchi. Ntchito zimene zapatsidwa sizachindunji. Mukuyenera kumalizitsa kufotokoza utumiki uliwonse kuti muwonjezere zinthu zina zimene mungazifune mu tchalitchi mwanu. Mukuyeneranso kuwonjezera zauzimu, maphuziro, ndi zoyenera zina zimene mungawone kuti ndizofunika komanso mawu a cholinga pa undindo uliwonse.

Tchalitchi ngati chiri cha ching'ono komanso atsogoleri ndi ochepa maudindo ambiri akhoza kuphatikizidwa. Mwachitsanzo, akulu ampingo atha kugwira ntchito ngati atumiki ndi olandira alendo. Othandizira abusa atha kukhala nkulu wa maphuziro. Tchalitchi ngati chiri chachikulu mawudindo ena atha kuwonjezereka. Mwachitsanzo, patha kukhala kufunika kwakukulu pakupereka ulangizi, mutha kufuna undindo wake wa
“nkulu wa malangizo”. Ichi ndi chitsanzo cha kafotokozedwe ka udindo wa mutumiki.

MAUDINDO AUTSOGOLERI

Mbusa:

Mbusa akuyenera kukhala oyitanidwa ndi Mulungu kuti atsogolere mpingo. Maudindo onse ali pansu pa ulamuliro wake mumpingo.

Ntchito yake ndi:

1. Kukhala ndi nthawi yaitali yosamalira moyo wauzimu wa gulu la okhulupilira.
2. Kusamalalira zinthu ndikuyang'anira utumiki onse mu tchalitchi.

3. Kutsogolera popanga madongosolo, kuwagwiritsa ntchito, ndi popanga kawuniwuni wa madongosolo.
4. Kupereka utsogoleri popembedza, kupemphera, kuphuzitsa, kupereka, kufalitsa, chiyanjano, ndi zochitika zina zauzimu mu tchalitchi.
5. Kusonkhanitsa ndi kukonzekeretsa anthu ku ntchito ya utumiki.
6. Kuchita kapena kugawa ntchito monga kulangiza, kuyendera, maukwati, maliro, mgonero ndi zina.
7. Kusungitsa mwambo mumpingo.

Othandizira Mbusa:

Mipingo yaikulu itha kufuna othandizira mbusa. Othandizira mbusa akuyenera kukhala ndi maitanidwe ngati mbusa.

Othandizira mbusa amathandiza mbusa m'magawo onse akafunika ndi kumfusidwa. Atha kupatsidwa ntchito ndi mbusa. Mwachitsanzo, mbusa atha kumpatsa ntchito yonse ya malangizo kapena kumfusa kuti ayendere anthu. Mwachidule, ntchito yake ndi kuthandiza mbusa:

1. Kuitana ma membala onse a m'chiyanjano.
2. Kuika zinthu m'malo ndi kuyang'anira utumiki onse.
3. Kupanga madongosolo, kuwagwiritsa ntchito, ndi kupanga kawuniwuni pa madongosolo.
4. Kupereka utsogoleri popembedza, kupemphera, kuphuzitsa, kupereka, kufalitsa, chiyanjano, ndi zochitika zina zauzimu mu tchalitchi.
5. Kusonkhanitsa ndi kukonzekeretsa anthu ku ntchito ya utumiki.
6. Kuchita kapena kugawa ntchito monga kulangiza, kuyendera, maukwati, maliro, mgonero ndi zina.
7. Kusungitsa mwambo mumpingo.

Atumwi:

Tanthawuzo lake: Ntumwi ndi munthu amene ali ndi kuthekera kokhazikitsa mipingo m'madela komaso zikhalidwe zosiyanasianaso. Ndikuyang'anira zochitika m'mipingo ingapo.

Ntumwi atanthawuza “nthumwi yotumidwa ndi mphavu komanso ulamuliro kukagwira ntchito m'malo a munthu wina”. Ntumwi ali ndi mphavu ina yake kapena kuthekera kwina kwake kopititsa patsogolo uthenga wabwino kudziko lapasi pokonzanso magulu a okhulupirira.

Aneneri:

Tanthawuzo: Pali Mphatso ziwiri za uneneri. Ina ndi Mphatso yapadera ya uneneri pamene ina imakhala yongoloseru chabe. Kunena mwachidule uneneri ndi “kulankhula motsogozedwa ndi Mulungu. Ndikuthekera kwapadera kolandira ndi kunena uthenga

ongopatsidwa kumene ndi kuwupereka kwa anthu ndi mafotokozedwe odzozedwa awuzimu”.

Aphunzitsi:

Tanthauzo: Amphuzitsi ndi okhulupirira amene ali ndi kuthekera kofotokoza uthenga wa Mulungu bwino kufikira kuti ena amaphuzira ndi kugwiritsa ntchito zimene aphuzira.

Alaliki:

Tanthauzo: Mlaliki ali ndi kuthekera kogawa uthenga wa Mulungu ndi anthu osakhulupirira mjira zosiyana siyana. Izi zimachitika mjira yakuti anthu amakhulupirira ndikukhala okhulupirira odziwa udindo wawo munthupi la Khristu. Mau akuti mlakiki atanthawuza munthu amene amabweretsa uthenga wabwino.

MAUTUMIKI OTUMIKIRA:

Mautumiki awa amatumikira atumwi, alaliki, ndi aphuzitsi mutumiki wawo wa mumpingo.

Akulu Ampingo:

Akulu ampingo amathandiza abusa pamene akutsogolera mpingo. Akulu ampingo ayenera kusakhidwa ndi mbusa. Mpingo ina amawatchula “ogwira ntchito pansi pa mbusa” kapena “Atsogoleri am’madera”.

Mutha kuwerenga zokhudzana ndi akulu ampingo M’baibulo m’malo awa: Tito 11:6; Akolose 1:25; I Timoteo 3:1-7; 4:5-6; 5:17; Machitidwe 14:23; 20:17,28-32; I Petro 5:1-4; Yakobo 5:14.

Akulu ampingo ndi abwino pamene mpingo ukukula kwambiri kufikira kuti ndikovuta kuti abusa apereke chisamaliro kwa nkristu aliyese. Nkulu wampingo aliyese atha kukhala ndi udindo wosamalira anthu ochepa mumpingo. M’musimu, mbusa ali ndi akulu ampingo okwanira asanu ndi awiri. Nkulu wa mpingo aliyese ali ndi gulu la anthu khumi amene mumawasamalira:

Mbusa

Nkhulu wa mpingo	Nkulu wa Mpingo	Nkhulu wa mpingo	Nkhulu wa mpingo	Nkulu wa mpingo	Nkulu wa Mpingo
00000	00000	00000	00000	00000	00000
00000	00000	00000	00000	00000	00000

Nthito za akulu ampingo ndi izi:

1. Nkani zonze zokhudzana ndi uzimu mumpingo.
2. Kulimbikitsa mbusa pa ntchito ya utumiki.
3. Kupempherera pafupi pafupi mbusa ndi mpingo wonse.
4. Kuthandiza mbusa nthawi ya mavuto awutumiki.

5. Kuyanganira zinthu zauzimu m'magulu ang'ono ang'ono mumpingo monga m'mene mbusa anagawira. Pafupipafupi kukumana ndi magulu ake, kuwatsogolera m'makulidwe amoyo wawuzimu, Mphatso za uzumu, kupereka malangizo, ndi kuyenedera okhulupirika m'makomo awo.
6. Kulangiza mbusa pa imfa, mavuto, matenda mumpingo amene akufunika kupezeka kuti achitepo kanthu.
7. Kuthandiza mbusa popanga zisankho zokhudzana ndi kayendetsedwe ka mpingo ndi zochitika zina ndi zina.
8. Kuthandiza kusungitsa mwambo.

Atumiki:

Atumiki ndi anthu amene amagwira ntchito mumpingo. (Onani Machitidwe 6:1-7). Atha kusankhidwa ndi anthu koma mbusa akuyenera kuvomereza.

Mutha kuwerenga za atumiki M'baibulo m'malo awa: 1 Timoteo 3:8-13; Afilipi 1:1; Machitidwe 61-7.

1. Ntchito zawo ndi: Kusamalira ma membala mokhudzana ndi zofunika zakuthupi ndi zinthu zina.
2. Kukonza ndi kugawa ngonero.
3. Kuika zinthu m'malo mwake m'magulu kuti ntchito imalizike m'mutumiki wa Mulungu.
4. Kupereka mayendedwe popita komanso kubwera ku church kwa okalamba ndi anthu a mawulumali.
5. Nthawi ya ngozi kupereka chakudya ndi malo.

Wapampando wa Mapephero:

Ntchito yake ndi:

1. Kukonza nthawi yapadera ya mapephero monga misonkhano ya mapephero.
2. Kukonza ndi kuyendetsa misonkhano ya mapephero.
3. Kulandira zopempherera zapadera kuchokera kwa ma membala a mpingo ndikuwonetsetsa kuti zasungidwe pamaso pa Ambuye.
4. Kupanga ndandanda wa opembedzera mutumiki. (Okhulupirira aliyese akuyenera kupephera, koma opembedzera ndi amene anaitanidwa kuti apembedzere utumiki).

Otsogolera Maphunziro a Chikristu:

Ntchito yake ndi:

1. Kukonza zochitika zokhudzana ndi maphunziro monga, kuphunzira kukhala otsatira khristu, maphunziro ampingo onse.

Ndibwino kukonza poyang'ana zaka, kuthekera kophunzira kumakhudzananso ndi zaka. Apa pali magawo ena amene mukhoza kuwalingalira:

- Ana (ana ang'onoang'ono nthawi ya mapephero)
- Ana (Okonzedwa poyang'ana zaka kapena kilasi ku sukulu)
- Anyamata (amene zaka zao ndizosadutsa 19)
- Achinyamata amene asanakwatire
- Achinyamata amene anakwatira
- Amene ali msukulu za ukachenjede
- Anthu akulu akulu kapena okwatira - Okalamba
- Atsogoleri amagulu am'makomo

2. Kupeza ndi kuphunzitsa atsogoleri agulu lina lilironse. Maphuziro a “Njira zophuzitsira” a (Harvestime International Institute) antha kukuthandizani.
3. Kuyang'anira aphunzitsi pa ntchito yawo. Izi zingakukhudzane ndi ku:

- Kuphuzitsa anthu pa ntchito ya utumiki.
- Kupempherera membala aliyese wa kulasi.
- Kusamalira mamembala (kuwayendera akapanda kubwera, akadwala, kupereka malangizo, kuthandiza ndi zofunika za kuthupi komanso (material needs). - Kupereka mwayi wa chiyanjano.

4. Kuika dongosolo la maphuziro pa gulu lililonse la anthu.
5. Ngati nthawi chuma zingalole, pezani zinthu zothandizira zochitika za maphuziro monga mapepala, zothandizira kuwona, zinthu za luso, ndi zina. Mtsogoleri wa Kufalitsa

Ntchito yake ndi:

1. Kukonza ndi kuyang'anira mawulendo a kufalitsa mumpingo kuphatikizirapo kuyendera alendo ndi otembenuka mtima kumene.
2. Kukonza ndi kuyang'anira maulendo akufalitsa a m'mizinda ndi m'maiko ena. 3. Kuphuzitsa, kulimbikitsa ma membala ampingo ku ntchito ya kufalitsa
4. Kukonza misonkhano ya maphuziro akufalitsa.
5. Kulumikizirana ndi atumiki amene akuthanizidwa ndi mpingo
6. Kuika atumiki amene akutumikira madera ena kuti adzalankhule ku mpingo pankhani ya kufalitsa.
7. Kupeza chuma cha ntchito ya kufalitsa

Wapampando wa utumiki wa abambo:

Ntchito yawo ndi kupanga dongosolo, kukonza zinthu, ndikutsogolera mautumiki a bambo mumpingo.

Izi zikhoza kukhudzana ndi:

1. Kupangitsa misonkhano ya mapephero, kukambirana mau a Mulungu, kuphuzitsa ndi chiyanjano cha abambo.

2. Kuwaika abambo m'mautumiki amumpingo ngati mapephero, kukambirana mawu a Mulungu, kupereka, kutumikira, kuchitira umboni.
3. Kupangitsa misonkhano ya abambo okhaokha.
4. Kupereka malangizo abambo amene ali ndi zosowa.

Wapampando wa utumiki wa amayi:

Ntchito yawo ndikupanga dongosolo, kukoza ndi kuyang'anira mautumiki amayi mumpingo. Izi ndi zinthu monga:

1. Kupangitsa misonkhano ya mapephero, kukambirana mau a Mulungu, kuphuzitsa ndi chiyanjano cha amayi.
2. Kuwaika amayi m'mautumiki amumpingo ngati mapephero, kukambirana mawu a Mulungu, kupereka, kutumikira, kuchitira umboni.
3. Kupangitsa misonkhano ya amayi okhaokha.
4. Kupereka malangizo amayi amene ali ndi zosowa.

Wotsogolera Maimbidwe:

Ntchito zawo ndi:

1. Kukonza dongosolo la maimbidwe m'zipembedzo zonse.
2. Kulongosola magulu a maimbidwe monga magulu ana, achinyamata, akulu. Wotsogolera maimbidwe atha kusankha ndi kuphuzitsa atsogoleri a gulu lililonse, kapena kuwatsogolera enkha.
3. Kukonza dongosolo la nyimbo.
4. Kulongosola ndi kutsogolera oyimba.
5. Kulongosola ndi kutsogolera zochitika zina za maimbidwe.
6. Kuyang'anira oyambitsa nyimbo.
7. Kupanga dongosolo ndi kutsogolera maimbidwe a ukwati, maliro, ochitikira ku chalitchi.
8. Kusamallira zida za maimbidwe monga zovala za magulu a maimbidwe, zida, nyimbo ndi zina.

Mlembi wa Mpingo:

Ntchito yake ndi:

1. Kulemba makalata
2. Kutumiza makalata kwa alendo onse.
3. Kuyang'anira malo ogwirira ntchito a mpingo, alendo,(lamy) ndi zina.
4. Kusunga uthenga wa mpingo (Mabuku akawundula wa alendo, ma membala ampingo ndi zina)
5. Kugula zinthu zofunika.
6. Kuyang'anira anthu ogwira ntchito modzipereka amene amathandiza ku tchalitchi.
7. Kukonza ma lipoti.

8. Kusunga ndandanda wa zochitika wa mpingo pamene pamakhala misonkhano yonse ndi zochitika zina.
9. Kukonzanso zipangizo zogwirira ntchito ndi zinthu zina kuti zikhale bwino.
10. Kulemba nthawi imene misonkhano iri mkati.

Mtsogoleri wa chuma:

Ntchito zake ndi monga:

1. Kuwerengera, kusunga, ndi kukonza zitsimikizo za zopereka, (Anthu osachepera awiri akhalepo pamene chopereka chikuwerengedwa. Izi zimathandiza kuwonetsetsa chilungamo).
2. Kukonzanso kaundula wa zachuma.
3. Kusunga uthenga wa ku Banki
4. Kugula zinthu ndi kulipira motsogozedwa ndi mbusa.
(Mukuyenera kuganiza kuti kupatula mbusa ndi ndani wina amene akuyenera kukhala ndi ulamuliro wogula zinthu m'malo mwa mpingo).
5. Kukonza dongosolondi kutsogolera zochitika zina zopezera ndalama.
6. Kukonza ma liporoti a miyezi ndi chaka.
7. Kuyerekeza ndi kuyang'anira ndondomeko yakagwiritsidwe ntchito ka chuma.
8. Kulimbikitsa chakhumi ndi chopereka.

Mtsogoleri wokonzanso zinthu:

Ntchito yake ndi zinthu ngati:

1. Kuyang'anira ntchito yokonzanso malo ozungulira ndi zomangamanga za pa tchalitchi.
2. Kuyang'anira ntchito yokonzanso zinthu zimene zinawonongeka pa tchalitchi.
3. Kuyang'anira zothenthetsera ndi zoziziritsira zipinda, madzi, magetsi ndi zina.
4. Kutsekula ndi kutseka malo misonkhano ikatha.
5. Kugula ndi kusunga katundu wogwiritsa ntchito kukonza pa mpingo.
6. Kuyang'anira ogwira ntchito pa tchalitchi.
7. Kuyang'anira ogwira ntchito modziperaka ku tchalitchi.

Woyang'anira Za Kanema

Ngati mpingo uli ndi kuthekera kokhala ndi zipangizo zowonera ndi kuverera, wina ayenera kukhala ndi ntchito yoyang'anira zinthu zimenezi. Ntchito ikhoza kukhala yoyang'anira zinthu ngati:

1. Zipinda za mpingo zosungiramo mabuku.
2. Zipangizo zomverera ndi kuwonera monga zamayimbidwe.
3. Utumiki wa matepi ndi kanema.
4. Kugula ndi kukonzanso zomverera ndi kuwonera.

Ma Asha

Ntchito yake ndi:

1. Kulandira anthu akamafika kumapephero.
2. Kutolera kapena kupereka zinthu monga m'mene zafusidwira m'mapephero.
3. Kulandira chopereka ndikuthandiza mtsogoleri wachuma powerenga.
4. Kugawa ndi kutorera ma kadi alendo.
5. Kutsogolera anthu makhalidwe a mtchalitchi nthawi ya mapephero.
6. Kuwonetsetsetsa mbali ya phokozo ndi zosokoneza nthawi ya mapephero.
7. Kuwona malo ozungulira (kutentha, kuwala, mavuto anjira ndi zina). Kufotokozerana kwa nkulu woyang'ana zokozanso zinthu pa mpingo.
8. Kuwona mabuku anyimbo ndi zinthu zina pa mipando ya mutchalitchi.
9. Kuwona mayalidwe azinthu (mipando ya abusa, olalikira, madzi, mafuta odzoza, mabuku anyimbo, ndi zina)
10. Kupeza chiwerengero cha anthu (Ngati kaundula amasungidwa)
11. Kuthandizira ndandanda wa mapephero.
12. Kutumikira (Kuthandiza akulu ampingo paene akutumikira) m'gonero.

Wapambando wa zolengeza:

Ntchito yake ndi kudziwitsa zochitika za pa mpingo m'njira za:

1. Makalata a mwezi ndi mwezi
2. Zolembalemba ndi zolengezetsa
3. Wailesi ndi mawayilesi akanema
4. Zolengeza nthawi ya mapephero
5. Nkhani za pa mpingo.

Komiti ya padera:

Komiti ndi gulu la anthu osapitilira makumi awiri loikidwa kuti zinthu ziikidwe ntchimake chifukwa cha cholinga. Chitsanzo, mutha kuika komiti kuti ikozekere maphuziro akufalitsa. Kapena mutha kuika komiti kuti mukonzekere za ulendo olalikira uthenga munzinda kapena kufuna malo oti pakhale tchalitchi.

Sitingakwanitse kukambirana za komiti ina iliyonse imene mukhoza chifwa cha mautumiki osiyanasiyana pa mpingo, koma m'musimu muli mfundo zotsogolera ma komiti onse:

1. Komiti ina iliyonse iyenera kugonjera kwa mbusa. Mulungu anaika mbusa ngati mtsogoleri wa mpingo pa dera. Ma komiti amaikidwa kuti amuthandize iye pa ntchito ya utumiki osati kuti ilamulire kapena kunena chochita.
2. Membala aliyese wa komiti akuyenera kudziwa cholinga cha komiti: chifukwa chani anakhazikitsidwa ngati komiti? Cholinga chawo ndi chani? Chimene ayenera kukwaniritsa ndi chani?
3. Mukhale ndi anthu okhao amene afunike kukhala ma membala a komiti
4. Ma komiti membala ayenera kudziwa malire a ntchito yawo. Akuyenera kukhala ndi mphavu kuchita kuchita ntchito yawo mogwirizana ndi malile awo.
5. Kumanani pokhapokha ziri zoyenerera. Onetsetsani kuti m'sonkhano uliwonse wakonzedwa bwino (onani ndondomeko zopangira misonkhano m'gawo lino). Membala aliyese akuyenera kupezeka mthawi yake komanso okonzeka. Akuyenera

kumalemba zinthu zimene wapatsidwa kuti achite ndikufusa mafuso pa achina chilichonse chimene wapatsidwa kuti achite.

6. Komiti iriyonse ikuyenera kukhal andi wapampando. Iyeyu ali ndi ntchito yokoza misonkhano ndi kuwuzabusa m'mene zokozekera zikuyendera kapena Mavuto.
7. Komiti membala aliyese akuyenera kukhala ndi ntchito ndipo akuyenera kudziwa chimene akuyenera kuchita.
8. M'nsokhano ukatha, membala aliyese ayenera ku:
 - Kuchita ntchito imene wapatsidwa.
 - Kupereka kwa ena amena akugwira nao ntchito zisankho, uthenga umene angafune kudziwa.
 - Kusunga chisisi china chilichonse chimene chachitika komanso chimene chianafunsidwa choncho.
9. Komiti iyenera kutha pamene cholinga komanso ntchito yake yatha.

KUSANKHA ANTHU KUTI AGWIRE NTCHITO YA UTUMIKI:

Maganizo ena osankhira anthu ku ntchito zosiyanasiyana ndi:

1. Pangani ndandanda wa zinthu zimene mukufuna kuchita.
2. Pangani ndandanda wa anthu amene atha kuchita ntchito imene mwasankha. Musankho powona Mphatso zauzimu zowoneka m'mowo wawo wa uzimu.
3. Pephererani ndandanda kuti ambuye akutsogolererani posankha.
4. Pangani kawuniwuni wa munthu aliyese poyang'ana:
 - Umboni wa uzumi
 - Mphavu
 - Zofoka
 - Maphuziro
 - Kukhalitsa mutumiki
 - Mphatso zauzimu
 - Mlingo wa mawu amulungu osankhira athu
5. Sankhani munthu pa ntchito iriyonse
6. Lembani mofotokoza ntchito ya utumiki uliwonse
7. Sankhani anthu ndipo apatseni ntchito. Onenetsetsani kuti munthu aliyese ali ndi pepala lofotokoza ntchito yake. Gwiritsani ntchito udindo wa utumiki mgawo lino kukuthandizani polemba izi.

Perekani maphuziro okwanira pokozekeretsa munthu aliyese kukwaniritsa udindo wake.

ZOONJEZERA 5

KUKONZA DONGOSOLO

MADONGOSOLO A CHITSANZO

Phunziro lino lafotokozera njira za kukonza dongosolo mwa tsatanetsatane. Gwiritsa ntchito Chaputala 4 kuti ikuthandizeni pamene mukukonza madongosolo. Chaputala 5 pamene mukukwaniritsa ndipo Chaputala 6 pamene mukuunikira momwe mwagwirira ntchito.

Ena mwa magawo omwe mpingo ukuyenera utakonza madongosolo nawa:

- Kuchitira umboni
- Kupereka
- Kuphunzitsa/Kupanga ophunzira
- Chiyanjano
- Kupembedza
- Pemphero
- Mautumiki apadera ofikira anthu

Zina mwa zitsanzo za zokhumba zomwe mipingo ina inakhazikitsa nayi: Tsatane tsatane wa madongosolo onse (ngati maudindo, masiku ndi mitengo ya zinthu) sizinaikidwe. Zokhumba zikuluzikulu zokhazokha ndi zomwe zalembedwa komanso mwachidule kuti zikupatseni chithunzithunzi cha mitundu ya madongosolo yomwe mipingo ina inakonza.

1. Kuonjezera anthu obwera ku mpingo 20 pa anthu 100 aliwonse chaka chirichonse kwa zaka zisanu.
2. Kuonjezera ziwalo zokhazikika zokwana 50 pa 100 aliwonse kwa zaka zisanu zikubwerazi.
3. Kuonjezera anthu obwera ku mwambo wa mapemphero ndi 300 mu zaka zisanu zikubwerazi ndi kugawa gululo kuti tiyambenso mpingo watsopano.
4. Kuyamba timagulu ting'ono ting'ono titatu mu chaka chikubwerachi.
5. Kuonjezera anthu obwera ku Sunday sukulu okwana 15 pa 100 aliwonse m'chaka chikubwerachi.
6. Kuphunzitsa atsogoleri a miraga asanu m'chaka chikubwerachi.
7. Kuonjezera ndalama zomwe timapereka ku ntchito ya mishoni ndi 40 peresenti mzaka zisanu zikubwerazi.
8. Kuphunzitsa atsogoleri khumi a Sunday sukulu zaka zisanu zikubwerazi.
9. Tigule malo athu athu ndi kumanga tchalitchi zaka khumbi zikubwerazi.
10. Kukonza misankhano yosachepera 6 chaka chamawa
11. Kukonza gulu la chiyanjano cha abambo m'chaka chamawa.
12. Kuonjezera mabanja khumi atsopano ku mpingo chaka chikubwerachi.
13. Kukonza gulu lothandizira utumiki wochitira umboni chaka chamawa.

KUKONZA DONGOSOLO LA MSONKHANO

Sitingakwanitse kufotokozera dongosolo la msonkhano uliwonse womwe mungakhale nawo pa mpingo. Mutha kuchita misonkhano yosiyana. Koma pali zinthu zingapo zomwe zitha kukuthandizani pa kakonzedwe ka msonkhano uliwonse womwe mungakhale nawo.

1. Khazikitsani cholinga cha msonkhano wanu monga momwe mwaphunzirira za kukhazikitsa cholinga.
2. Ikani masiku ndi nthawi za msonkhano wanu.
3. Sankhani malo ochitira msonkhano.
Zinthu zofunika kuziyang'ana pamene mukusankha malo nazi:
 - a. Kukula kwa malo: Malowo akhale ogwirizana ndi chiwerengero cha anthu omwe mukuwayembekezera.
 - b. Zofunikira: Izi ndi monga ma kitchen, tizipinda tokumaniramo timagulu ting'onoting'ono nthawi ya msonkhano, zimbuzi ndi mabafa okwanira.
 - c. Dera: Musankhe dera lomwe anthu sangavutike mayendedwe kuti afike pamalopo.
 - d. Mtengo: Ukhale mtengo woti mutha kukwanitsa kulipira malo a msonkhano wanuwo.
4. Mukhazikitse komiti yoyendetsa msonkhano ndi kugawa ntchito zosiyana siyana kuti:
 - Kuyendetsa dongosolo: Mtsogoleri amayang'anira anthu pa ntchito zawo zonse ndi kulumikizitsa zochitika zonse.
 - Kuika nthawi: Nthawi yoikidwa ikuyenera iphatikizapo izi:
 1. Zonse zofunika kuchitika pa msonkhano: Agwire ntchito ndani, ndipo igwirika nthawi yanji.
 2. Nthawi yeniyeni ya chochitikacho: Kodi chichitike ndi chiani ndipo chichitika nthawi yanji pa tsiku lenilenilo.
 3. Zofunika kulongosola msonkhano ukatha.
 - Dongosolo la ndalama: Kuika dongosolo la ndalama zomwe zifunike pa msonkhano, kusonkhetsa ndalama, kulipira mabilu, kutolera chopereka nthawi ya msonkhano, ndi kutolera mphatso ya mlaliki woitanidwayo.
 - Kukonza malo a msonkhano: Zina mwa zinthu zofunika kulongosola pa malo a msonkhano nazi: mipando, gome, tebulo, mbale za chopereka, zida zoimbira, zipangizo zolembetsera maina ndi kupereka uphungu kwa anthu.
 - Kulembetsa maina: Kodi mudzalemba maina a anthu? Ngati ndi inde, kodi anthuwo mudzawapatsa zipangizo zotani akalembetsa dzina? Nanga mizere ya anthu olembetsa maina idzayenda motani? Kodi anthu adzayenera kupereka ndalama yolembetsera? Kodi padzafunika ma bachi? Nanga mudzafuna mafomu ndipo anthu amene adzagwire ntchitoyo ndi ndani?
 - Kulengezetsa msonkhano: Kodi msonkhano wanu mudzaulengezetsa motani? Sankhani munthu amene adzayendetsa dongosolo la kulengeza – kaya ndi mumseu, pa TV, pa wailesi, mu nyuzipepala ndi njira zina zotero.
 - Kupereka uphungu: Pezani munthu woti aphunzitse anthu omwe azidzathandizana ndi anthu pa zosowa zawo za moyo wauzimu. Iwowa akuyenera kudziwa momwe angatsogolere munthu wina kulandira Yesu, kupempherera odwala, ndi kuchita mamasulidwe. Akhale ndi ma Baibulo, timathiraki, komanso timakhadi tolembapo maina a iwo ofunika thandizo lauzimu. Timakhaditi tidzakuthandizani pomadzayendera anthuwo msonkhano utatha.
 - Mlaliki woitanidwa: Kodi mudzakhala ndi mlaliki wochita kuitanidwa? Ngati ndi choncho, mukuyenera kupeza munthu woti agwire ntchito imeneyi kuonesetsa kuti munthuyo wadziwitsidwa za dongosolo lonse ngakhale kumkumbutsa pamene masiku akuyandikira. Kukonza mayendedwe komanso malo ogona. Ndi kuonesetsa kuti zosowa zawo zikukwaniritsidwa nthawi yonse ya msonkhano.

- Nyimbo: Sankhani munthu amene aziona za mayimbidwe oyimba. Nyimbo zodzaimba ndi kutsogolera mwambo wa nyimbo.
- Utumiki wa ana: Kodi mudzasamalira motani ana nthawi ya msonkhano? Mufunika munthu amene adzakonze malo osamalirira ana ndi kusankha anthu odzasamalira anawo.
- Zogulitsagulitsa: Ngati muli ndi dongosolo logulitsa ma Baibulo, mabuku a Chikhristu, zakudya ndi zinthu zina sankhani munthu amene ayang'anire ntchito yonseyo.
- Otumikira: Pakhale munthu amene ayang'anire ntchito ya otumikira, kugawa ndi kutolera zipangizo, kutolera zopereka, ndi kukonza zovuta komanso zosokoneza zina ndi zina nthawi ya msonkhano.
- Zida: Ngati mukukonza zokhala ndi mwambo waukulu, mukuyenera kukhala ndi zida zamphamvu. Pakhalenso munthu yemwe akudziwa bwino kagwiritsidwe ntchito kake.
- Anthu obwera ku msonkhano: Mukuyenera kukhala ndi munthu yemwe adzidzaona za anthu omwe adzabwere ku msonkhano. Mwa chitsanzo, dongosolo la mayendedwe, zakudya, malo ogona ngati afunike, ndi kuona zosowa zawo zina ndi zina monga mafunso, nthawi ya msonkhano.
- Kukonza zinthu mwambo utatha: Mukuyenera kukhala ndi munthu yemwe akhale alondoleze zinthu msonkhano ukatha. Izi ndi monga kutolera katundu wa pamalopo ndi kuonesetsa kuti katundu wobwerekedwa wabwezedwa. Kukonza malowo komanso kuthokoza anthu amene anakuthandizani ntchito.

Kukonza mapepala okonzera dongosolo

Mupeza mafomu omwe mungagwiritse ntchito pokonza dongosolo la pa tsiku komanso la pa tsiku m'musimu.

DONGOSOLO LA PA TSIKU

Tsiku: _____

Makalata ofunika kulembedwa:

Mafoni ofunika kuimba:

Anthu ofunika kukumana nawo:

6:30 am: _____

7:00 am: _____

7:30 am: _____

8:00 am: _____

8:30 am: _____

9:00 am: _____

9:30 am: _____

10:00 am: _____

Zofunika Kuchita:

Zofunika kulongoledwa

10:30 am: _____

11:30 am: _____

12:00 pm: _____

12:30 pm: _____

1:00 am: _____

1:30 pm: _____

2:00 pm: _____

2:30 pm: _____

3:00 pm: _____

3:30 pm: _____

4:00 pm: _____

4:30 pm: _____

5:00 pm: _____

5:30 pm: _____

6:00 pm: _____

6:30 pm: _____

7:00 pm: _____

7:30 pm: _____

8:00 pm: _____

Zinthu zofunika kutengedwa

Anthu ofunika kuonedwa

Lamulungu	Lolemba	Lachiwiri	Lachitatu	Lachinayi	Lachisanu	Loweruka

MAYANKHO A MAFUNSO

CHAPUTALA 1

1. Koma zonse zichitike koyenera ndi kolongosoka (1 Akorinto 14:40)
2. Kuyendetsa bwino zinthu mwa zolinga ndi dongosolo lotenga udindo pa utumiki kudzera kudzera kukonza dongosolo ndi kuika zinthu m'malo.
3. Yerekezani m'ndandanda wanu ndi womwe wafotokozeredwa mu Chaputala 1.
4. Yerekezani kufotokozerera kwanu ndi komwe kuli mu Chaputala 1

CHAPUTALA 2

1. Anatzindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, 10kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. (Aefeso 1:9-10)
2. Cholinga cha Mulungu ndi chakuti anthu onse apeze chikhulupiriro mwa Khristu Yesu, nakhala pa ubale wabwino ndi Iye ndi kukhala mbali imodzi ya Ufumu wa Mulungu. Onani Aefeso 3:11 ndi 1:9-10; and Yohane 3.
3. Ngati sukumvetsa cholinga cha Mulungu, moyo kapena utumiki wanu sukhala wogwirizana ndi Iye.
4. Mulungu amagwiritsa ntchito, maiko, Yesu, Mzimu Woyera, ndi Mpingo ngati chida chokwaniritsira zolinga ndi madongosolo ake.
5. Yerekezani ndemanga yanu ndi zomwe zakambidwa mu Chaputala 2.
6. Yerekezani ndemanga yanu ndi zomwe zakambidwa ndi mu Chaputala 2
7. Yerekezani ndemanga yanu ndi zomwe zakambidwa mu Chaputala 2.

CHAPUTALA 3

1. Potero, penyani bwino umo muyendera, si monga opanda nzeru, koma monga anzeru; 16 akucita macawi, popeza masiku ali oipa (Aefeso 5:15-16)
2. Mau a Cholinga amafotokozerera chifukwa chenicheni chimene chokhalira ndi utumiki wanu. Amaonetsera malo anu eni eni mu ntchito ya Mulungu.
3. Onaninso m'ndandanda wa zifukwa zomwe zaperekedwa mu Chaputala 3.
4. Cholinga ndi mau ofotokozerera chifukwa chimene utumiki wanu ulipo. Pamene zokhumba ndi mau a madongosolo omwe utumiki wakonza kuti ukwaniritsa cholingacho.
5. Mau a Chiphunzitso ndi amafotokozerera ziphunzitso zomwe mumakhulupirira.
6. Yerekezani m'ndandanda wanu ndi zomwe zalembedwa mu Chaputala 3.
7. Ngati simulemba Mau a Cholinga a utumiki wanu ndi utumiki womwe mukutumikira, pangani zimenezo musanapitilire ndi phunziro lino.

CHAPUTALA 4

1. Ndipo kapolo uyo, wodziwa cifuniro ca mbuye wace, ndipo sanakonza, ndi kusacita zonga za cifuniro caceco, adzakwapulidwa mikwapulo yambiri (Luka 12:47)
2. Chokhumba ndi ganizo la mapeto a ntchito omwe mumafuna mutafika. Ndi dongosolo. Mukaika zokhumba m'malo, zimakuthandizani kupanga madongosolo okwaniritsira cholinga cha Mulungu.

3. Cholinga ndi masomphenya auzimu. Ndiko kudziwa cholinga chako cheni cheni mu utumiki. Gawo lako mu ntchito ya Mulungu. Zokhumba ndi ndondomeko zokutengerani ku zomwe Mulungu akufuna mutakwaniritsa pa cholinga chomwe wakupatsani. Ndi madongosolo okwaniritsira cholinga.
4. Magulu awiri a zokhumba ndi zako ngati munthu pawekha komanso za gulu.
5. Yerekezani yankho lanu ndi zomwe ziri mu Chaputala 4.
6. Zokhumba za nthawi ya patali ndi zokhumba za mtsogolo kwambiri, pamene zokhumba za nthawi yapafupi ndi zokhumba tsogolo lapafupi.
7. Mumasankha zokhumba kudzera m'pempheo, kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera, kusanthu Mau a Mulungu, ndi kumvetsa cholinga chanu chenicheni mu dongosolo la Mulungu.

CHAPUTALA 5

1. Koma tsopano tsirizani kucitaku; kuti monga kunali cibvomerezo ca kufunira, koteronso kukhale kutsiriza kwacem'cimene muli naco. (2 Akorinto 8:11)
2. Ndondomeko ndi masitepe omwe mtsogoleri amatega kuti akwaniritse dongosolo. Ndi njira kapena ntchito yomwe mtsogoleri amachita kuti akwaniritse madongosolo.
3. Kudzera m'mafanizo awa, Yesu anaonetsera kuti nthawi zina nkovuta kuti madongosolo a miyambo ya chipembedzo a anthu akale amakana kulandira madongosolo ndi mabvumbulutso atsopano.
4. Yerekezani ndemanga zanu ndi kukambirana kwa udindo uliwonse wa utsogoleri womwe wakambidwa m'phunziro lino.

CHAPUTALA 6

1. Pakuti ndi cisomo capatsidwa kwa ine, ndiuza munthu ali yense wa inu, kuti asadziyese koposa kumene ayenera kudziyesa; koma aganize modziletsa yekha, monga, Mulungu anagawira kwa munthu ali yense muyeso wa cikhulupiriro. Aroma 12:3
2. Mukamaunikira kanthu mumakasanthula mosamalitsa kuti muone phindu lake. Kuunikira zinthu ndi ntchito yosanthula madongosolo kuti muone ngati akukwaniritsa cholinga. Zokhumba zimakhazikitsa zomwe mukukonza kuchita. Ndipo kuunikira kumaonetsera ngati mwakwaniritsadi zomwe mumayembekezera.
3. Kuunikiraku kumakuthandizani kukhala munthu amene ntchito yake iri pa mbalambanda panda pamaso pa Mulungu, omwe mukugwira nawo ntchito, omwe mukuwatumikira, komanso pamaso pa inu eni. Kumakuthandizanso kuti muphunzire kuchokera ku zomwe mwachita bwino, komanso zomwe simunachite bwino, kukonzanso madongoso anu, ndi kukonza madongosolo atsopano.
4. Yerekezani yankho lanu ndi zomwe ziri mu Chaputala 6.
5. Yerekezani mndandanda wanu ndi womwe uli mu Chaputala 6.
6. Zomwe mwapeza mu kuunikira kwanu zimakuthandizani ku:
 - a. Kukonzanso madongosolo anu.
 - b. Kukonza madongosolo atsopano pamene akale akwaniritsidwa.
 - c. Kuphunzira kuchokera zomwe mwachita bwino.
 - d. Kuphunzira ku zomwe simunachite bwino.
 - e. Ngati simunaukirensa dongosolo lanu ndi kugwiritsa ntchito zotsatira za kuunikira kwanuko, chonde yambani.